

# MASOMPHENYA APA PATMO



... Pamene M'bale Neville amalengeza zimenezo kuti... M'bale Moore ankanena tsiku lina, kukamba za Mzimu wa Ambuye, unadzalowa... ukulowa mnyumbayi. Iye anati, "Izo zinali zopambana kwambiri mmenemo mpaka ine ndinaganiza kuti Mkwatulo wabwera mpaka ine ndinayang'ana pozungulira, ndinawawona ena atakhala apa," ndinati, "ayi, iwo sunabwerebe, chifukwa ngati—ngati iwo akadali pano ndiye ndikudziwa kuti ine ndikadali kuno." Chotero nthawizina Mzimu wa Ambuye umakhala wabwino chomwecho kwa ife.

<sup>2</sup> Ndife okondwa kwambiri kukhala ndi abwenzi ochuluka amene ife tikuwawona mchipinda chino. Ochuluka kwambiri kuti ndingayesere kuwatchula. Ine ndinangopezeka kuti ndikumuwona, akubwera pakhomo, M'bale Carpenter, mwamuna amene anatikwatitsa mkazi wanga ndi ine pamodzi. M'bale Carpenter, wakhala ali mdalitso waukulu kwa ife pano pa tchalitchi, ndipo wakhala mdalitso kwa ife mu njira ya utumiki, ndipo amalalikirira chirichonse, pafupifupi kulikonse. Ndipo ndife okondwa kukhala naye limodzi, oh, ena ambiri zedi.

<sup>3</sup> Tsopano pali funso lina apa limene linaperekedwa kwa ine usiku wapitawu:

**M'bale Branham, kodi anamwali opusa asanu a Mateyu 25 amawerengedwa ngati otsalira a Amitundu? Ndimamva kuti anamwali asanu opusa anapulumutsidwa koma akuyenera kudutsa nthawi ya chisautso chachikulu. Kodi izi ndi zoono? Ngati ndi choncho, kofikira kwawo komalizira kudzakakhala kuti? Kodi iwo angakhale nkhosha zimene zikudzalekanitsidwa ndi mbuzi pa Mateyu 25:33 ndi 34?**

<sup>4</sup> Wafioloje wabwino kwambiri mogwirizana ndi zomwe ine... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]... kuganiza izo aponso, kuti iwo ndi otsalira, anamwali ogonawo ndi otsalira amene akunenedwa mu Chivumbulutso; a mbewu ya mkazi imene imasunga malamulo a Mulungu ndi kukhala ndi umboni wa Yesu Khristu. Mayi amatenga—chidutswa cha nsalu ndi kuiyala iyo pansu; chabwino, tsopano, iyo ndi imene iye akudulapo... kapena amatenga pateni yake ndi kuiyala paliponse pamene iye angafune, mbali imene iye ati adulepo. Ndiyeno imene iye watsala nayo imatchedwa yotsalira, koma iye amasankha kuyidula iyo pamalo ena ake mwa ufulu wa kuganiza kwake. Koma imene yatsalirayo imatchedwa yotsalira.

<sup>5</sup> Tsopano, ngati mungazindikire, panali asanu opusa ndi anamwali asanu anzeru; onse a iwo anali anamwali, opangidwa kuchokera ku chinthu chofanana. Koma, mwa kusankha, Mulungu anasankha Mkwatibwi Wake mwa kusankha maziko

a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, anaika maina awo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa wophedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe; dziko lisanayambe nkomwe, Mulungu mmalingaliro Ake, pokhala wopanda malire.

<sup>6</sup> Ndipo ife timagwiritsa ntchito mawu nthawizina, akuti “kukonzedweratu,” koma iwo ndi chopachikira chotsimikizika mu m’badwo wa mpingo uno umene ife tikukhalamo. Iwo ndithudi anali chinthu chachikulu chimene chinkagwiritsidwa ntchito mmasiku a ofera, chifukwa iwo ndithudi ankawakhulupirira iwo. Koma izo zinachoka kwa Iwo tsopano, kupita ku malingaliro a malamulo, chiphunzitso cha zamalamulo mu mpingo chimene chimabwera. . . Chimene chinali chinthu chabwino, chifukwa zonse za izo zinali zitalowa Chikalvinist ku England mpaka iwo analibe zitsitsimutso nkomwe, ndipo John Wesley anadzabwera akulalikira chiphunzitso cha Arminian chimene chinafanizitsa izo. Mulungu nthawi zonse azazifanizitsa izo.

<sup>7</sup> Chotero ndiye namwali wopusa ndi amene analibe mafuta mu nyali zawo, amene ine ndikukhulupirira kuti anaponyedwa mu mdima wakunja kumene kudzakhala kulira, kususima, ndi kukukuta kwa mano. Ndipo ngati mungafanizitse zimenezo, kapena zolembe zanu zapansi, izo zithamangira kubwerera kenanso ku chisautso chachikulu. Ndipo ine ndikuganiza kuti iwo ndi amene adzatsale mmbuyo ndi kudutsa mu chisautso chachikulu. Ndipo ndi phunziro ndithudi pamene, ngati tikanakhala ndi nthawi yoti tilowe mu zimenezo. Ngati inu. . .

<sup>8</sup> Tsopano, kumbukirani, ine ndinanena poyamba, kumene pamene inu mumva matepi, “Zinthu izi zangokhala basi molingana ndi momwe ine ndikukhulupirira kuti izo ndi zolondola.” Mukuona? Tsopano, ngati iwo akulakwitsa, ine sindiri—Ine sindikudziwa kuti iwo akutero. Ine. . . Ndipo ine ndikhoza kungonena chimene ine ndimakhulupirira. Ndipo ine sindikutanthauza kuti ndipweteke malingaliro a aliyense. Ife tikuyenera kuti tizingozisiya izo pambali tikamalowa muno, ndiyeno nkutenga chinthu chimene chanenedwacho, ndi kuchifufuza icho, ndi kuwona ngati iwo ali Malemba kwenikweni kapena ayi. Ndiyo njira yabwino yochitira izo. Kenako. . . Chifukwa mu tsiku longa limene ife tikukhalamo tsopano, mu fuko limene izo zakunkhidwa mobwereza ndi mobwereza ndi mobwereza ndi mobwereza ndi mitundu yonse ya chirichonse, chabwino, ndi zovuta kuti anthu azimvetse kwenikweni izi, monga izo zimakhallira ku dera loti sikunakhudzidwepo. Inu mukawauza iwo, iwo amakhulupirira izo, umo ndi momwe zimachitikira.

<sup>9</sup> Koma, tsopano, mmodzi amabwera ndi lingaliro *ili*, ndipo wina amabwera ndi lingaliro *ili*, ndipo ife tiri ndi mipingo yachipembedzo pafupifupi naini handiredi ndi chakuti yosiyanasiyana, ndipo aliyense amatsutsana (chiphunzitso

chake) ndi mzake; ndipo pakuyenera kukhala winawake akulakwitsa, ndipo winawake akulondola. Chotero tsopano umboni wokhawo wa izo ndi, ndi kuzibweretsa izo kubwerera ku Baibulo; mwaona, kulola Baibulo. Tsopano, nthawi zambiri, anthu amaika kutanthauzira kwawo kwawo. Koma ife timayesetsa mwakukhoza kwathu kumene tingathe, kuti tisayike kutanthauzira kwa umunthu pa izo. Kungowerenga Izo momwe Izo ziliri, ndi kuti, “Umo ndi momwe Izo ziriri.”

<sup>10</sup> Ndiyeno ine nthawizonse ndakhala ndikuzindikira, ngati iwe utangotenga zimene Iye ananena, izo zidzapangitsa chirichonse kulumikizana basi ndendende mu Lemba. Izo zimakhala pafupifupi ngati kuyika zidutswa za chithunzi pamodzi, iwe umayenera kuti uzinyang’ana pa pateni usanzilumikize zidutswazo pamodzi molondola. Ngati sutero, ine nthawizonse ndimati, “Ungakhale ndi . . . Pa chimene uli nachocho, ukhoza kukhala ndi ng’ombe ikudya udzu pamwamba pa mtengo.” Chotero izo—izo basi sizingawoneke bwino bwino.

<sup>11</sup> Ndipo ngati ife tingalole Mzimu Woyera . . . Ndani analemba Baibulo? Mzimu Woyera unkasunthira pa amuna ndipo amalemba Baibulo. Ndiye popanda Mzimu Woyera, ziribe kanthu kuti ndinu wophunzira bwanji, inu simungalimvetse Ilo. Chifukwa ngakhale Yesu anamuthokoza Mulungu kuti Iye anzibisa Izo kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo amakhoza kuziulula Izo kwa makanda omwe akanakhoza kuphunzira. Ndipo mmodzi aliyense wa ophunzira anali mochulukana kapena pang’ono osatha kuwerenga ndi anthu osaphunzira kupatula mmodzi, ndipo ameneyo anali Paulo. Ndipo Paulo anati anachita kuyiwala zonse zimene ankazidziwa kuti amupeze Khristu. Chotero iye anauza mpingo waku Korinto, iye “sanabwere ndi nzeru za anthu ndi kuyankhula kopambana,” chifukwa pamenepo chawo—chikhulupiro chawo chikanakhala mu nzeru za anthu, koma iye anabwera kwa iwo mu mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera, kuti chikhulupiro chawo chikhale pa ntchito za Mzimu Woyera mogwirizana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo pamenepo ndi pamene ife tikuyesetsa kukhala moyandikira kwambiri, pakali pano, chifukwa sabatayi isanathe, kapena nthawi ya sabatayi isanathe, inu muziwona izo, ndizo ndendende zimene zakhala zikuchitika, ulusi waung’ono uja ukubwera motsika kudutsa m’badwo motsatira.

<sup>12</sup> Ndikukuthokozani inu chifukwa chokwezera bolodiyo mmwamba pang’ono. Zimenezo zikuwonekako bwino.

<sup>13</sup> Tsopano, oh, ife . . . Ndikanakonda tikanakhala nalo ilo nthawi yonse ya chisanu, kuchitira kuti tidzangotenga Bukhu lathunthu la Chivumbulutso ndi kumangodutsa mu Ilo. Iko ndi kuphunzitsa kokongola chomwecho mmenemo. Ndipo ine ndikukumbukira, ine ndikuganiza zakhala ziri zaka twente zapitazo kapena twente-faivi, pamene tchalitchi chinali chikadali chatsopano, ife tinayamba umodzi . . . koyambirira

mu kugwa kwa masamba kumodzi, ndipo zinali pafupifupi mpaka ku kugwa kwa masamba kotsatira, tikudutsa Bukhu la Chivumbulutso.

<sup>14</sup> Tsopano, ine ndikukumbukira ndikutenga Bukhu la Yobu. Oh, M'bale Wright! Ine ndinakhala pa ilo motalika kwambiri mpaka potsiriza mkazi anandilemba ndi kundifunsa ine, iye anati, "M'bale Branham, kodi inu simumuchotsa Yobu pa mulu wa phulusa uwo?" Chabwino, ndimayesetsa kuti ndipange mfundo, chifukwa pamenepo ndi pamene chirichonse chinayikidwapo pamodzi, pa malo amenewo; kufika pamalo amene Mzimu wa Ambuye unadzabwera pa iye, ndiye pamene mphezi ziyamba kung'anima ndipo mabingu nkubangula, Mzimu unadza pa mneneri ndipo iye anawona kudza kwa Ambuye. Ndipo ine ndimafuna ndizipange izo momveka, ndi chifukwa chake ndinamusiya iye pamulu wa phulusa kwanthawi yayitali, kuti—kuti ife tikhoze kupanga mfundo. Ndipo ine ndikudziwa kuti zikhoza kukhala zotopetsa pang'ono, zina. Ndimakhala wa manjenje, nanenso, pamene ndimuvva wina akusewera ndi chinachake, kumawoneka ngati apitirira ndi kumenya izo. Koma mwinamwake Mulungu akumutsogolera munthu ameneyo pa cholinga cha izo.

<sup>15</sup> Tsopano kubwerera kwa otsalira awa, tisanalisiye funsolo. Ine ndikukhulupirira ndikulimvetsa bwino ilo. Ili...Ine ndimakhulupirira moona kuti otsalira ndi osankhidwa ndi Mulungu. Ine—ine ndikukhulupirira zimenezo, kuti Mulungu anasankha wotsalira maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe; ndipo anatero mwa "kudziwiratu" Kwake. Osati mawu...Tsopano penyani *okonzedweratu*, mwaona, chifukwa ndi mawu aang'ono obaya pakati pa anthu. Mukuona? Koma Mulungu, maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, mu malingaliro Ake aakulu opandamalire, anasankha Mpingo, anasankha Yesu, anasankha Mpingo, ndipo ankakhoza kuneneratu pachiyambi chimene chiti chidzakhale kumapeto. Iye...Ngati Iye ali wopandamalire, palibe chirichonse chimene Iye samachidziwa. Iye anadziwa utitiri uliwonse umene ukanadzakhalapo pa dziko lapansi, ndipo ndikangati kamene iwo ukanadzaphethira maso ake. Tsopano, umo basi ndi momwe...ndi mafuta ochuluka bwanji amene iwo ukanadzapanga, ndi zochuluka zomwe iwo wonse ukanadzapanga. Izo ndi zopanda malire, ndiko kupandamalire; inu—inu...palibe njira yoti nkuzifotokozera Izo. Ndipo Mulungu, ndicho chimene Iye ali, Mulungu wopandamalire.

<sup>16</sup> Chotero, ngati inu mungazindikire, Baibulo linanena kuti mmasiku otsiriza kuti wotsutsakhristu yemwe ati adzabwere pa dziko lapansi...

<sup>17</sup> Tsopano mveterani mwatcheru! Ndicho chilema chokhacho...Ine ndikuganiza iye akanadzapeza mamilioni mwa ine. Koma pa M'bale wathu wofunika Billy Graham, tsiku

lina, ulaliki wodziwika uja umene iye analalikirira Lamlungu lapitali, ndipo ine ndithudi ndinaganiza kuti unali uthenga wa munthawi yake. Ndipo . . . koma iye ananena kuti “Satana akunyenganso Osankhidwa.”

<sup>18</sup> Ayi, Baibulo linati, “Iye akanadzanyenga Osankhidwa *ngati* kukanakhala kotheke.” Koma ndi zosatheka, chifukwa Mulungu anawasankha iwo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Mukuona? Mwanawankhosa . . . Yesu Khristu anali Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. Pamene Mulungu achiyika kumene mu malingaliro Ake, Iye akayankhula Mawu amenewo, Iwo sangasinthe nkomwe, Iwo sangasinthe nkomwe. Mwaona, chifukwa Iye—Iye ndi—Iye ndi wopandamalire, ndipo Mawu Ake adzakwaniritsidwa.

<sup>19</sup> Tangoganizani, yemweyo . . . dziko lapansi limene ife tikukhalamoli usikuuno ndi Mawu a Mulungu akuwonetseredwa. Dziko lapansi linakonzedwa pamodzi ndi zinthu zimene sizimawoneka nkomwe. Iye anangoti, “Pakhale,” ndipo zinatero. Ndi zophweka bwanji kuti Mulungu ameneyo achiritse thupi lodwala ndiye, ngati Iye angamange chirengedwe pongoyankhula izo. Mwaona, Mawu Ake. Ngati ife tikanangopeza chikhulupiriro kuti tiwone chimene Mawu Ake ali! Ife tiri omangiririka kwambiri kwa dziko lapansi ndiponso osakanizika mmalingaliro athu mpaka kuti ife . . . Oh, ine sindikudziwa. Takhalapo ndi malingaliro ochuluka kwambiri, operewera kwa awa, ndi operewera kwa awo, ndipo—ndipo izo zangotifikitsa ife pamalo pamene zonse zapotoka. Koma ngati inu mukanakhoza konse kugwedeza chinthu chonsecho, kubwerera podziwa kuti Iye ndi Mulungu, ndipo Mawu Ake sangalephere monganso Iye sangalephere. Ndipo ngati Mawu amenewo alephera, ndiye kuti Mulungu amalephera; ndipo ngati Mulungu amalephera pamenepo . . . Iye si Mulungu. Mukuona? Chotero . . . Ndipo inu mukukumbukira, Iye sanganene chinthu chimodzi *apa* ndi chinachakenso *apa*; Iye akuyenera kukhala ndi lingaliro Lake loyamba kuti akhale Mulungu. Chotero, ife tango- . . .

<sup>20</sup> Ndipo Iye anangotipempha ife chinthu chimodzi, kuti tizikhulupirira kuti chimene Iye ananena ndi Choonadi, ndipo Iye adzachikwaniritsa icho. Oh, ndi zokongola bwanji! Inu mumayembekezera kuti chinthu chodzidzimutsa chichitike; nthawizina zimangotengera chikhulupiriro chapang’ono basi. Sichingapange chozizwitsa, koma ngati mungagwiritsitse kwa icho, icho chidzakutulutsani inu; mungokhala ndi icho. Monga Iye anati, “Mbewu ya mpiru, yochepetsetsa pakati pa mbewu zonse.” Koma kodi inu munayamba mwazindikirapo, mpiru sungasakanizike ndi chirichonse. Inu simungasakanize mpiru ndi chirichonse, izo sizingasakanizikane. Ndipo ngati inu muli ndi chikhulupiriro, chikhulupiriro chapang’ono

chabe chimene sichingasakanizikane ndi kusakhulupirira kulikonse kapena chitchalitchi chirichonse kapena mbalume, mungokhala pomwepo ndi Mulungu, mungokhala ndi Iwo, Iwo adzakubweretsani inu kudutsa mu nkhungu, adzakutulutsani inu kunja. Eya! Mungokhala ndi chikhulupiriro chimenecho.

<sup>21</sup> Tsopano, pachiyambi, pamene Mulungu...Baibulo linanena, mu Chivumbulutso, kuti “Wotsutsakhristu, mu masiku otsiriza...” Tsopano tayang’anani pa mipingo iyi yonse ikubwera pamodzi. “Wotsutsakhristu, mmasiku otsiriza, akanadzanyenga onse amene anali pa dziko lapansi amene maina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa kuyambira pa maziko a dziko lapansi.” Dzina lanu linaikidwa liti mu Bukhu la Moyo? Ife tisanakhale nalo konse dziko lapansi, inu munasankhidwa kuti mudzalandire Mzimu Woyera mu m’badwo uno.

<sup>22</sup> Ine ndalumikizana ndi Eddie Perronet:

Ndazika solo yanga mu mpumulo wa  
kumwamba,  
Kuti ndisadzayendesenso pa nyanja  
zokayikira;  
Mphepo ikhoza kusesa muthengo, nkuntho  
wakuya,  
Koma mwa Yesu ndife otetezeka  
kwanthawizonse.

<sup>23</sup> Palibe chimene chingatilekanitse ife (Mulungu sangatero... samabwerera mmbuyo pa Mawu Ake. Ndipo ngati Iye ali wopandalamire, ndipo nkukupatsani inu Mzimu Woyera *apa*, akudziwa kuti Iye adzakutayani *apa*, Iye akuchita ntchito ya mtundu wanji?), ngati inu simunanamizidwe mu chokuchitikirani chanu, ngati inu muli ndi Mzimu Woyera. Koma penyani chimene Baibulo linanena, Aefeso 4:30, “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo kufikira...” Chitsitsimutso chotsatira? Kodi zimenezo zikumveka molondola? “Inu munasindikizidwa kufikira tsiku la chiwombolo chanu!” Mpaka liti? Mpaka chiwombolo chanu.

<sup>24</sup> Mutenge galimoto yonyamula katundu, muiyike iyo mungolomo, ndipo pamene iyo yalongezedwa bwino bwino...Tsopano, iwo sangaitseke galimoto imeneyo pamenepo, woyang’anira akuyenera abwerepo kaye. Ndipo iye amadzayang’ana, ndi kuwona ngati pali chomasuka chimene chingagwedezeke. Bokosilo likhoza kukhala...Galimoto yonyamula katundu ikhoza kudzaza, koma ngati iyo ili ndi malo omasuka, inu mukuyenera kuilongezanso. Ndipo ndiro limene liri vuto, ambiri a ife sitimalandira Mzimu Woyera; pamene woyang’anira abwera, Iye amadzapeza malo ambiri

omasuka, inu mwaona, chotero Iye amalephera kuti ayikepo chisindikizo.

<sup>25</sup> Wafioloje wamkulu anabwera kwa ine tsiku lina, kapena osati tsiku lina, zakhala ziri zaka zitatu kapena zinai zapitazo, ndipo iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake.” Anati, “Abrahamu ankakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye chilungamo.”

Ine ndinati, “Izo nzoona, kulondola.”

Anati, “Ndi chiyani chinanso chimene munthuyo akanachita koma kukhulupirira?”

Ine ndinati, “Ndizo zonse zimene iye akanachita.”

<sup>26</sup> Iye anati, “Ndiye inu mumapita nazo kuti zinthu izi za Mzimu Woyera kunjja kwa izo?” Tsopano, inu mukudziwa kuti iye anali wa Baptisti. Ndipo iye anati—anati, “Inu mumapita kuti ndi Mzimu Woyera uwu?” Anati, “Ngati munthu akhulupirira! Miniti imene wakhulupirira, walandira Mzimu Woyera.”

Ine ndinati, “Ayi, ayi. Tsopano, inu—inu mukupanga kutsutsana mu Malemba, Malemba samadzitsutsa Okha. Mukuona? Paulo anawafunsa iwo, ‘Kodi munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira?’”

Ndipo iye anati, “Chabwino . . .”

<sup>27</sup> Ine ndinati, “Ndi zoonza kuti Abrahamu atate wa chikhulupiriro anapereka . . . iye anali ndi lonjezano la Mulungu ndipo anakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye chilungamo, koma Iye anamupatsa iye chisindikizo cha mdulidwe ngati chizindikiro chakuti Iye walandira chikhulupiriro chake.”

<sup>28</sup> Tsopano, ngati Iye sanakusindikizeni inu ndi Mzimu Woyera, Iye sanachilandirebe konse chikhulupiriro chanu mwa Iye, inu muli nawo malo ena amene akugwedera. Mukuona? Inu mukhoza kukhulupirira, eya, koma pali malo ambiri amene akugwedera. Koma pamene mwawalongeza malo onse ogwederawo, ndiye Iye amakusindikizani inu ndi Mzimu Woyera kufikira tsiku la chiwombolo chanu. Ndiko kutsimikizira kwa Mulungu kuti Iye walandira chikhulupiriro chimene inu munachivomereza mwa Iye.

<sup>29</sup> Abrahamu anavomereza chikhulupiriro, ndipo Mulungu anati, “Ine ndikupatsa iwe chizindikiro tsopano kuti iwe . . . kuti Ine ndakulandira iwe.” Ndipo Iye anamupatsa iye chizindikiro cha mdulidwe.

<sup>30</sup> Tsopano, pamene inu mumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu ndi kukhulupirira pa Iye ndi kumupempha Iye kuti ayeretse moyo wanu, ndiyeno pamene Iye abwerera ndi Mzimu Woyera ndi kudzakupatsani inu chizindikiro cha Mzimu Woyera, zikatero inu mwasindikizidwa mpaka chiwombolo chanu.

<sup>31</sup> Galimoto ya ngolo iyi apa, ngati iyo ikugwederera... Iyo itapachikidwa pamodzi ndipo nkutsekedwa chitseko chimenecho ndi kuyikapo chisindikizo pa iyo, ndipo iyo—iyo yasindikizidwa mpaka kumene ikupita, makampani a njanji angakumange iwe kwa moyo wako wonse ngati iwe ungaswe chisindikizo chimenecho. Izo sizingaswedwe. Iyo yasindikizidwa mpaka kumene iyo ikupita; osati aliyense amene ali panjira akhoza kukoka icho ndi kuchitsegula ndi kuwona mkati mwake, ndi kuiyenderera iyo ndi kuiwona iyo, ndi kuponyera zinthu zingapo panja, kuyikamo zinthu zina zowonjezera mmenemo. Ayi, ayi!

<sup>32</sup> Mpingo *uwu* udzati, chabwino, mbalume imeneyo, “*Izi* si zabwino, *izo* si zabwino.” Pamene Mulungu akupatsani inu Mzimu Woyera, *izo* zakhazikika! Iwe umadziwa pamene wayima, iwe umadziwa chimene chinachitika, ndipo iwe umasindikizidwa njira yonse mpaka tsiku la chiwombolo chako, kofikira kwanu kwa ulendo wapadziko lapansi lino. Oh, mai! Zimenezo zikuyenera kumupangitsa aliyense kungokhala ndi chikhulupiriro ndi kukhulupirira Mulungu, kungodzuka mu mphamvu ya Mzimu Woyera.

<sup>33</sup> Tsopano, anamwali awa amene sanalandire Mzimu Woyera, (Inu mukukumbukira?) chinthu chokhacho chimene iwo ankachisowa chinali mafuta mu nyali zawo. Nkulondola uko? Baibulo linati *mafutawo* amaimirira “Mzimu Woyera,” ndi chifukwa chimene ife timawadzoza odwala ndi mafuta, ndi zina zotero, chifukwa ndi chiphiphiritso cha Mzimu Woyera. Tsopano, ndiyeno ngati—ngati Mzimu Woyera sunabwere pa iwo, iwo analibe Iwo. Ndiyeno pamene Iye anabwera, iwo anati... Tsopano, kwa anamwali amene anali nawo mafuta, anati...

<sup>34</sup> Inu mwaona, iwo anali atabwerera mu m’badwo wa mpingo; panali ena a iwo mmenemo amene anali anthu abwino koma sanali mu Kuwala kwa nyenyezi, chimene ine ndikutanthauza, chingwe chitaviikidwa mmafuta. Mwaona, ndipo icho chinali kunja. Icho chinali chitatuluka, iwo anali atadzilekanitsa okha. Paulo ananena, mu tsiku lake, “Iwo anadzilekanitsa okha kwa ife, mochita kuwoneka kuti analibe chikhulupiriro.” Mwaona, ndipo anachoka kwa iwo, “Iwo anachoka kwa ife chifukwa iwo sanali a ife.” Tsopano, izo zinayambira mmbuyo mu m’badwo woyambirira wa Efeso uja ndipo zikubwera mpaka mu m’badwo uno lero. Chinthu chomwe chomwecho, uliwonse wa mibadwo imeneyo, zimene zinachitika mmenemo zinalumikizana mpaka mu mibadwo iyi kumusi kuno. Ife tilowamo mmenemo mwakuya mu kanthawi pang’ono.

<sup>35</sup> Tsopano, zindikirani kuti namwali uyu, ngakhale, iye anapita kumene kunali kulira, kuisima, ndi kukukuta kwa mano.



<sup>36</sup> Ndiroleni ine ndinene ichi, mzanga wofunika wokoma; chifukwa kawirikawiri ku tchalitchi kuno, pamene ine ndibwera kuno, ine ndimangobwera kuno ndi kudzakhala ndi msonkhano wa machiritso ndi kupempherera odwala, ndi kunja kuzungulira dziko kwinakwake. Koma nthawi yake ndi ino, ndakhala ndikukuuzani inu nthawi yayitali, ikani chikumbumtima chanu mthumba mwanu. Tsopano ife tikufuna—tikufuna kuti tibwere ndi kudzakhala owona mtima ndi owona kwa wina ndi mzake, chifukwa ife tiri pa tsiku lotsiriza. Eya!

<sup>37</sup> Tsopano, apo ndi pamene inu a Nazarene ofunika ndi a Pilgrim Holiness pansu pa kuyeretsedwa munalepherera. Mukuona? Tsopano, kodi inu mukudziwa kuti Yudasi Iskarioti anakhala mpaka kufika pa malo omwewo? Yudasi anakhulupirira Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi, anamulandira Iye ngati Mpulumutsi. Ndipo iye nayenso anayeretsedwa. Iye anayeretsedwa, mu Yohane 17:17, pamene Yesu anati, “Atate, ayeretseni iwo kupyolera mu Choonadi, Mawu Anu ali Choonadi.” Ndipo Iye anali Mawu. Chabwino!

<sup>38</sup> Mu Mateyu 10, iwo anapatsidwa mphamvu yochiritsa odwala, kuwukitsa akufa, kutulutsa ziwanda. Ndipo iwo anatuluka kupita kumadera onse a—a dziko ndipo anakatulutsako ziwanda, ndipo anabwererako akusangalala ndi kufuula ndipo akutamanda Mulungu. Ndipo Yesu anawauza iwo, “Musakondwere chifukwa ziwanda zakumverani inu, koma kondwerani chifukwa mayina anu ali m’Bukhu la Moyo.” Nkulondola uko? Ndipo Yudasi anali ndi iwo, Yudasi anali ndi iwo, koma izo zinali chaka ndi miyezi sikisi Yesu asanapachikidwe.

<sup>39</sup> Tsopano, ndiye pamene zinadzafika pa Pentekoste, kuti Yudasi alandire Mzimu Woyera ndi zina zotero, iye anawonetsera mangamanga ake. Iye—iye anamukana Yesu, ndipo anadzakhala womupereka Iye. Ndipo pamenepo ndi pamene ndendende pamene mzimu umenewo unadzabwera; kubwera kudzadutsa mwa Lutera, Wesile, unawubweretsa mpingo umenewo ku kuyeretsedwa ndi moyo wa unamwali (wangwiro, wosadetsedwa, woyera, wabwino, anthu abwino kwambiri amene inu munakumanapo nawo), koma pamene izo zinadzafika ku... pamene iwo anayamba kuyankhula mmalirime ndi kulandira Mzimu Woyera, a Nazarene, Pilgrim Holiness, Free Methodist, kenako anati, “Ameneyo ndi mdierekezi.” Ndipo pomwepo ndi pamene inu mumanyoza Mzimu Woyera ndi kudzitsekera nokha kwanthawizonse; “Pakuti aliyense amene anganene mawu otsutsa Mwana wa munthu adzakhululukidwa, koma aliyense amene adzayankhula motsutsa Mzimu Woyera sadzakhululukidwa konse.”

<sup>40</sup> Kumbukirani, ophunzira onse ankayankhula mmalirime. Yesu Khristu anafa pa mtanda, akuyankhula mmalirime. Uh-hum. Chotero ngati simungathe kuthana nawo kuno,

kukhala pa ubwanawe ndi iwo kuno, ndiye zikakhala bwanji kumeneko? Kwa iwo. . . Ngati awa ali adierekezi, chomwechonso iwo anali. Chotero inu mukuona pamenepo ndi pamene izo zinawonetsera mangamanga ake? Apo pakubwera namwali ameneyo, woyera monga ena onsewo, moyo woyera. Ine nditenga mipingo yachikale ya a Nazarene, Pilgrim Holiness, imene inkakhulupirira kwenikweni mu kuyetsedwa, inu simungayike chala pa miyoyo yawo; oyera momwe iwo angathere. Ndi chinthu chabwino kuti tonse tikanakhala chomwecho. Uko nkulondola, inu mukuyenera kutero.

<sup>41</sup> Tsopano, ife tikudziwa ife tiri nawo ochuluka mwa Apentekoste monga onyengezera. Izo nzoona. Koma chimodzimidzi basi monga inu mumawonera dola yabodza, inu mukudziwa kuti iyo inapangidwa kuchokera ku yabwino, yeniyeni. Uko nkulondola. Ndipo pali—pali Mzimu Woyera weniweni, weniweni Uwo umene umayankhula mmalirime ndi kusonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo zakhhalapo kuyambira pa Pentekoste kumatsika. Chotero ife tiyenera kukhala ndi onyengezera. Ife tikuyenera kukhala ndi mkazi woypa amene siwabwino, kuti amupangitse mkazi weniweni kuwonekera. Ife tikuyenera kukhala ndi nthawi yausiku, mdima wakuda, kuti tiwonetsere kuti kuwala kwa dzuwa ndi kopambana. Uko nkulondola. Ndipo inu mukuyenera kudwala, kuti musangalale ndi thanzi labwino. Ndipo ndi lamulo la zabwino ndi zoyipa; ndipo ndi—ndipo nthawizonse zakhala ziripo, ndipo zidzakhhalapo nthawizonse, bola ngati nthawi ilipobe.

Tsopano, chotero, apo ndi pamene mpingo unadzadzisunthira wokha mmwamba.

<sup>42</sup> Tsopano, kodi Yesu sananene kuti “Mu tsiku lotsiriza,” mu Mateyu 24, “kuti mizimu iwiri ikanadzakhala yofanana kwambiri mpaka iyo ikanadzanyenga Osankhidwa kumene ngati kukanakhala kotheka”? Uh-hum. Koma iye amene anasankhidwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi ali nawo Moyo Wamuyaya. Moyo Wamuyaya, inu simungathe kuwuchotsa Iwo. Iwo ndi Wamuyaya monga Mulungu aliri, inu simungathe kusiya kukhalapo chimodzimidzi monga momwe Mulungu sangasiye kukhalapo. Uko nkulondola. Chifukwa ndinu gawo la Mulungu, ndinu mwana wamwamuna ndi wamkazi wa Mulungu, moyo wanu unasinthidwa ndipo ndinu gawo la Mulungu, muli nawo Moyo Wamuyaya. Oh, ine ndimamkonda Iye. Sichoncho inu?

<sup>43</sup> Tsopano, winawake anandipatsa ine cholemba apa, funso laling’ono chabe. Ife sititenga nthawi yochuluka tsopano kuti tiyankhe ilo. Ndipo kumbukirani, nthawi iliyonse mukayika funso laling’ono, Ndiziyesetsa momwe ndingathere kuti ndifike kwa ilo ngati ndingathe. Koma ili linali funso lofunikira:

**Wina amafuna kudziwa ngati ziri zolakwika kuti akazi azichitira umboni, kapena kuyimba, kapena kupereka mauthenga mu malirime, kutanthauzira mauthenga, kapena kulosera, mu mpingo.**

<sup>44</sup> Ayi, si zolakwika, ndi. . . bola ngati izo zikubwera mmalo mwake mwadongosolo. Mukuona? Mpingo uli mu dongosolo, ndipo pokhapo pamene. . . Njira yeniyeni, yona yochitira izo ndi kwa iwo amene amayankhula ndi malirime ndi zinthu, mauthenga awo amaperkedwa uthenga usanachitike kuchokera paguwa, osati pa nthawi imeneyo; chifukwa Mzimu Woyera ukuyenda kuchokera pamalo amodzi pa nthawi, monga Paulo anayankhulira za izo pamene. Koma akazi ali ndi mphatso ya uneneri, ndipo ali ndi mphatso ya malirime ndi kutanthauzira, ndi chirichonse koma kukhala alaliki. Iwo sakuyenera kukhala alaliki. Iwo amaletsedwa kulalikira mmpingo, izo nzoona, kutenga malo, kapena kukhala mphunzitsi kapena chirichonse mu mpingo. Koma kunena za mphatso, mkazi ali nazo zonsezo, akhoza kukhala ndi imodzi kapena iliyonse ya mphatso zisanu ndi zinai zauzimu mogwirizana ndi Akorinto Woyamba 12, ndipo sali womangidwa kuti uthenga wake usamabwere mmalo mwake. Inu mwaona, uthenga uliwonse umadikirira nthawi yake.

<sup>45</sup> “Ngati pali wina amene amayankhula mmalirime, pakakhala kuti palibe wotanthauzira, msiyeni iye akhale chete mpaka pakhale wotanthauzira.” Mukuona? Ndipo mauthenga awa amaperkedwa, kawirikawiri, basi msonkhano usanayambike, ndiye mneneri, kapena, mlaliki, amene ali mneneri wa Chipangano Chatsopano, mlaliki, pamene iye abwera Mulungu amayamba kuyenda kudutsa mwa iye, mwaona, kenako iye akamaliza ndiye mauthenga amayambapo, ena, ndiye basi zisanachitike, izo nthawizonse zimakhala mwadongosolo, nthawizonse; koma mkazi ali ndi ufulu.

<sup>46</sup> Chotsatira, ndikungofuna, nditenge nthawi pang’ono kuti ndiyankhe izi, ndiwerenga mutu wankhani:

ZIKHULUPIRO ZITATU ZOMASULIRIDWA ZA BAIBULO LIMODZI ZIKUYAMBIKA. Washington, Okutobala 15. Akatolika, Achiprotestanti ndi ophunzira Achiyuda omwe akugwira ntchito limodzi anayamba kumasulira kwatsopano limodzi kwa Malemba zimenezo zikhoza kutsimikizira kuti ndi Baibulo limene limayembekezedwa la masiku onse lovomerezedwa.

<sup>47</sup> Zinthu zina zingapo apa ndikufuna ndiwerenge pang’ono ndisanazilengeze izo. Mwakuyankhula kwina, inu mukuona ndendende chimene ife tikuchikamba, ndendende basi chimene Lemba likunena kuti zidzachitika mmasiku ano, kuti zinthu izi zidzalumikizana pamodzi ndi kudzapanga fano la chirombo. Ndendende. Iwo ayeserapo izo, ndipo akugwira ntchito pa

izo, ndipo tsopano iwo ali ndi mwayi wabwino umene iwo anakhalapo nawo wopereka izo, chifukwa izo ziri mmanja mwawo kumene. Ndipo icho ndi chifukwa chimene ine ndikubweretsa mauthenga a uneneri awa, chifukwa ndikuganiza kuti ndi nthawi yake.

<sup>48</sup> Ndipo ngati pali aliyense amene angabwerere usiku uliwonse, ife tidzayesa kuyamba molawirira ndi kudzatuluka molawirira. Ndipo ngati ine sindimaliza phunziroli, ndiye ine ndidzalengeza mmawa wotsatira. Ngati sitimalizitsa kukhazikitsa kwa 19, ndime ya 9 mpaka ya 20 usikuuno, tidzayamba izo mmawa teni koloko. Ife tikudziwitsani inu kumapeto kwa msonkhano, momwe titachitire.

<sup>49</sup> Ndiyeno mawa usiku pa mpingo wa Efeso, kuyamba, kuyenda kudutsa mausiku asanu ndi awiri: Efeso, M'badwo wa Mpingo wa Efeso; ndi Simuna; ndi Pergamo; ndi Tiyatira; ndi Sarde; ndi Filadefiya; ndi Laodikaya, Lamlungu likubwerali.

<sup>50</sup> Ndipo podziwa ngale zopambana izi ziri pansu mu msewu, ndi zovuta kwambiri kuti ndisazigwire mpaka nthawiyo. Kumangoziyang'ana izo pansu apo, ndi kumamverera Mzimu ukudyerera pakati pa anthu, izo zimandipangitsa ine kuti ndifune kudumphirapo mwachangu kwenikweni ndi—ndi kunena chinachake cha izo; koma ndikungoyenera kubwerera mmbuyo ndikuziyika mu m'badwo wawo ndi pa nthawi yawo. Chotero ngati inu muphonya kubwera usiku, muwonetsetse kuti mudzapeze tepiyo kapena mwanjira ina imene inu mungakhoze kupezero Iwo, chifukwa ine ndikufuna kuti iyo ipite konsekonde. Ndipo ine ndachita izi chifukwa ndikumverera kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera kuti ndichite chomwecho; ndicho chifukwa chokhacho chimene ine ndikuchitira izi. Ndipo ine, ngati ndikanati ndisaganize kuti izo zingathandize mpingo. . . Ndipo mu tsiku lino, kumbukirani, ora lifika posachedwapa pamene ife sitimadzakhala ndi misonkhano iyi, ndipo inu mukuyenera kuchita izo pakali pano pamene ife tikadali ndi nthawi yochitira izo. Mwaona, ife sitikudziwa nthawi imene iwo ati adzaletse izi, tsopano.

<sup>51</sup> Ndipo chotero padzakhala mgwirizano pakati pa mipingo ndipo iyo idzaziyanjantsa yokha pamodzi, adzapanga wamkulu wa chitaganya cha mipingo, chimene inu muli nacho kale ndi nyumba yayikulu ya U.N. ndipo chipembedzo chirichonse chiri mmenemo. Ndipo mwina inu mudzayenera kukhala wa china mwa zipembedzo zimenezo kapena mudzachotsedwamo. Ndipo imeneyo ndi nthawi imene ife tikuyenera kudzawonetsa mangamanga athu ndi kudzakhala otsimikiza kuti ife tikudziwa, osati zongopeka, koma kudziwa PAKUTI ATERO AMBUYE pamene iwe ukuima. Mpingo wawung'ono wakhala nthawizonse uli mu kagulu kochepa, ndi gulu laling'ono kwambiri limene. . . kachingwe kakang'ono, monga—chingwe chofiira chimene

chimadutsa mu Baibulo, koma ndi Mpingo nthawizonse. Ndipo ife tikufuna kukumbukira zimenezo.

<sup>52</sup> Tsopano ndemanga pang'ono chabe ife tisanawerengenso. Mmawa uno ife tinatenga Umulungu Wapamwamba wa Chivumbulutso cha Yesu Khristu, chimene Mulungu anamuwulula Iye kwa ife mmawa uja ngati Umulungu Wapamwamba: INE NDINE Wamkulu (osati ine *ndinali* kapena *ndidzakhala*), INE NDINE, nthawizonse. Ndipo ife tikuzindikira mu mutu wa 1 uwu wa Chivumbulutso, wa Chivumbulutso...Kodi vumbulutso la chiyani? Yesu Khristu. Kodi chinthu choyamba chimene Iye akudziulula Yekha apa ndi chiyani? Mulungu wa Kumwamba. Osati mulungu wapatatu, koma Mulungu mmodzi. Mulungu mmodzi, ndipo Iye akudziulula Yekha mwanjira imeneyo koyambirira kwa Chivumbulutso. Ndipo akuyankhula izo kanayi mu mutu wa 1 kuti pasakhale kulakwitsa. Chinthu choyamba chimene inu mukuyenera kudziwa, nchakuti: Iye si mneneri, Iye si a—mulungu wamng'ono, Iye si mulungu wachiwiri, Iye ndi Mulungu! Iye ndi Mulungu. Ndipo chotero Vumbulutso linabwera, ndipo ife tikupitirira nalo Ilo usikuuno kupitirira mpaka mmusi pamene ife tikupeza mawonekedwe Ake asanu ndi awiri a umunthu Wake.

<sup>53</sup> Ndipo, oh, Mulungu atithandize ife pamene tikuphunzitsa Mawu awa. Ine—Ine—Ine ndaphunzira izo kuchokera ku mawonedwe a mbiriyakale, koma mudikire mpaka ine ndidzafike pa guwa pano kuti ndidzapeze kudzoza. Chifukwa ine ndikumverera kuti takhala pamodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, ndipo kuti Mzimu wanu, gawo lanu, ka lawi ka Moto (Mzimu Woyera) kamene kali pa inu kamabwera pa wina, ndi pa wina kupita pa wina, Iko kamayatsa Thupi lalikulu la Mulungu ndi kuliyatsa Ilo moto, ndipo pamenepo ndi pamene mavumbulutso. . .

<sup>54</sup> Tsopano, chinthu chimene ife tikuchikamba, funso ili linafunsidwa kwa ine, “Kodi akazi...ndi zina zotero?” Ndizo ndendende chimene chinayambitsa mpingo mu chisokonezo chake pachiyambi, iwo anali atatenga ulemu wonse kuchokera kwa omvetsera nkuwaika iwo paguwa. Koma Mulungu ndi Mulungu wa omvetsera. Iye amagwira ntchito mwa munthu aliyense, Iye amakhala mu mtima uliwonse umene Iye angalowemo. Iye amawapeza anthu amphatso amenewo ndipo amagwira ntchito kudzera mwa iwo. Tsopano, ngati mdierekezi sangathe kuwagwira iwo pa chinthu chimodzi, ndiye iye amabwerapo ndipo amadzangopanga mgwirizano wawukulu wopanda kanthu ndi kuwathamangitsapo anthu. Monga Paulo ananenera, “Pamene inu mubwera pamodzi, ngati inu nonse mungayankhule malirime, ndipo wosaphunzira nkudzabwera, kodi iye sadzati, ‘Ndinu amisala! Opusa!’? Winawake akuyankhula mmalirime, ndipo *izi* ndi *izi* mosagwirizana,

ndi chirichonse, izo sizingagwire ntchito. Koma,” iye anati, “ndiye ngati wina anenera ndi kuwulula chinsinsi cha mumtima, pamenepo iwo adzati, ‘Zoonadi Mulungu ali nanu.’” Koma ngati wina ayankhula ndi malirime mwa vumbulutso ndi kupereka kutanthauzira kwake, chinachake choti chirimbikitse mpingo, ndiye mpingo wonsewo udzalimbikitsidwa ndi icho. Chinachake chimene chingadzayankhule ndipo Mulungu nkuyankhula mu zinenero zimene ife sitikudziwa kalikonse ka izo ndipo nkupereka kwa wina ndi kutanthauzira izo mwa wina, ndi kunena chinthu china chimene chidzachitike ndendende momwe chanenedwera, ndiye inu muli ndi Mzimu wa Ambuye pakati panu. Ndipo, oh, tiyeni tirimbikire zimenezo, abwenzi; tiyeni—tiyeni tiwusunge moto umenewo uziyaka.

<sup>55</sup> Tsopano, basi tisanatsegule a... mndandanda wawukulu uwu wa Lemba, Ine ndikudabwa ngati zingakhale zowonjeza ngati ife tingaimirire ndi kusintha kakhaliidwe kathu kwa maminiti pang’ono chabe pamene ife tikupemphera.

<sup>56</sup> Mulungu Wamphamvuzonse amene munamubweretsanso Ambuye Yesu kwa akufa ndipo mwamupereka Iye kwa ife (patadutsa zaka naintini handiredi) monga Mulungu wosalephera wa Kumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha ichi ndi chifukwa cha Kukhalapo Kwake ndi ife tsiku ndi tsiku mu kuyenda kwathu kwa tsiku ndi tsiku. Ndipo ndife okondwa kwambiri kudziwa kuti mu nthawi ino ya chisokonezo pamene dziko silikudziwa choti lichite, iwo akukumba maenje pansu, ndipo iwo akudzirimbitsa okha mu konkire, koma, O Mulungu, iwo sangakhoze kubisala ku mkwiyo wa Mulungu. Pali limodzi lokha—yankho limodzi, Ambuye, ndipo ndife okondwa kuti talandira Izo: “Pamene Ine ndidzawona Magazi Ine ndidzakudutsani inu.” Oh, momwe ife tiri okondwera ndi chitetezo chokwanira usikuuno cha Magazi a Mwanawankhosa wa Mulungu, Wansembe Wamkulu, atayima mu Ulemerero usikuuno akupanga kupembedzera pa kuvomereza kwathu. Ndife okondwa kwambiri kukhala naye Iye usikuuno, Woyankhula wamkulu, Mzimu Woyera wawukulu, wopereka kudzoza wamkulu, Wopereka-moyo wamkulu.

<sup>57</sup> Ndipo tsopano, Ambuye Mulungu, pamene ine ndawayitanira anthu awa pamodzi pansu pa denga lino usikuuno, ndipo ife tasonkhana pano ngati mpingo kapena gawo la iwo, ife sitimasonkhana mu dzina la kachisi uyū kapena mu dzina la munthu aliyense, koma mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole Mzimu umene umalamulira thupi Lake ndi malingaliro Ake, ndi kumulamulira Iye, ubwere mwa ife usikuuno ndipo udzawatanthauzire Mawu ndi kuwalalikira Mawu, ndi kuwapereka Iwo ku mitima yathu yanjala pamene ife tikudikirira pa Iye. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake ndi kwa ulemelero Wake. Amenii. (Khalani pansii.)

58 Tsopano kwa inu amene muli ndi Mabaibulo anu, tsegulani ku mutu 1 wa Chivumbulutso ndipo muyambire pa ndime ya 9; mapensulo anu ndi mapepala, ndipo ine ndiyetsa kuti ndikupatseni inu madeti pang'ono ndi zina zotero pamene ine ndikupitirira.

59 Tsopano, izi kwenikweni. . .Lero mmawa linali ngati la ulaliki, kuyika maziko pa Umulungu, wa Vumbulutso; Mulungu kukhala akuwululidwa mwa Khristu. Ndi angati akukhulupirira Zimenezo? Mulungu anawululidwa mwa Khristu, Yehova anawululidwa mwa Khristu. Tsopano Mulungu ali kuti wofuna kuwululidwayo? Mu Mpingo Wake, ndi anthu Ake, mwa ife. Mzimu womwewo, ntchito zomwezo, mawonetseredwe omwewo, chikondi chomwecho, chikhululukiro chomwecho, kuleza mtima komweko, kudekha, chipiriro, mtendere, chifundo, zonse zimene zinali mwa Khristu ziri mu Mpingo. Kumbukirani, musunge izi mmalingaliro: zonse zimene Mulungu anali Iye anazitsanulira mwa Khristu (Iye anali chidzalo cha Umulungu mthupi), ndipo zonse zimene Khristu anali Iye anazitsanulira mu Mpingo. Mulungu pamwamba pathu, Mulungu nafe, Mulungu mwa ife. Utatu wa Mulungu, Mulungu anawonetseredwa mu kachitidwe katatu kosiyanana: Atate, Mwana, Mzimu Woyera.

60 Vumbulutso linawonetsera kuti Iye si amulungu atatu, komanso Iye sanadulidwe mu zidutswa zitatu. Koma Iye ndi Mulungu mmodzi amene anali Mulungu mmasiku a Utate, Iye anali Mulungu mmasiku a Umwana, Iye ndi Mulungu mu masiku a nyengo ya Mzimu Woyera, Mulungu yemwe yemweyo. Osati atatu osiyanasiyana, osati anthu atatu, osati umunthu utatu. Iye ndi Munthu mmodzi, umunthu umodzi. Inu simungakhale umunthu wopanda kukhala munthu. Anthu ena anati, "Iye si anthu atatu, koma Iye ndi umunthu utatu." Simungathe kulekanitsa izo; chifukwa ngati Iye ali umunthu, Iye ndi munthu; akuyenera kukhala munthu kuti apange umunthu. Chotero Iye ndi Munthu mmodzi, umunthu umodzi; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; Alfa, Omega; Iye amene anali, amene alipo, ndipo adzabwera. Oh, Iye ali ZONSE basi. Ine ndimakonda zimenezo.

61 Penyani chikhalidwe Chake, moyo Wake, ntchito Zake. Icho chikuyenera kuwonetseredwa pomwe pano mu kachisi uyu, chimodzimidzi basi monga momwe zinaliri mu tsiku Lake. (Sindikunena izi mwatsankho; Mulungu akudziwa zimenezo.) Osati kuno kokha, koma kudutsa dzikoli. Ndine wokondwa kuti izo ziri chomwecho. Ndiye ife timadziwa pamene tayima chifukwa ife tiri ndi Mzimu womwewo mwa ife, ukuyenda ndi ife ndi kumawonetsera kuti Iye ali pano. Si ife, ndi Iyeyo; ife sitingachite zinthu zimenezo, ameneyo ndi Mulungu. Pambali pa zimenezo, mu dziko la sayansi, Iye analola kuti chithunzi Chake chijambulidwe. Ndi ife, mwa ife, potizungulira ife, pamwamba

pathu, mwa ife, akugwira ntchito mkati ndi kunja kwa ife. Oh, ndi zodabwitsa bwanji!

62 Iwo anakakonda kuyimba nyimbo yaying'ono:

INE NDINE amene ndinayankhula ndi Mose,  
mu chitsamba choyaka moto,  
INE NDINE Mulungu wa Abrahamu,  
Nyenyezi Yowala ya Mmawa.  
INE NDINE Rozi la Sharoni; oh, inu mumati  
Ine ndinachokera kuti?

Kodi inu mumawadziwa Atate anga, kapena  
kodi inu mungalidziwe Dzina Lawo?

Oh, inu mukunena kuti Ndine ndani, kapena  
mumati Ine ndinachokera kuti?

Kodi inu mukuwadziwa Atate anga, kapena  
kodi inu mungalidziwe Dzina Lawo?

NDINE Alfa, Omega, woyamba kuchokera  
kumapeto,

INE NDINE chirengedwe chonse, ndipo Yesu  
ndiye Dzinalo.

63 Oh, ndi zodabwitsa bwanji, Vumbulutsolo! Tsopano, kumbukirani, inu simungakhoze kuzipeza Izo kudzera mwa fioloje, Ilo silimabwera mwanjira imeneyo. Ilo limangobwera ngati vumbulutso. Ubatizo wa mmadzi, kugwiritsa ntchito Dzina la Yesu Khristu, ukhoza kokha kuperekedwa ngati vumbulutso. Yesu ndi Mulungu kukhala Munthu yemwe yemweyo zikhoza kungobwera ngati vumbulutso. Baibulo lonse linamangidwa pa vumbulutso. Mpingo wonse unamangidwa pa vumbulutso. Mateyu 17 amati, “Pakuti ine ndinati, ‘Pa thanthwe ili (vumbulutso lauzimu) Ine ndidzamangapo Mpingo wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.’” Ife tinabetchera aliyense kuti atiwonetse ife, paliponse, mbiriyakale kapena Lemba, pamene panakhalapo anthu aliwonse amene anabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” kunja kwa mpingo wa Katolika kufikira tsiku la Martin Luther. Kenako mpingo wa Chiprotestanti, iwo unali . . .

64 Ndipo choyipa chirichonse, mvetserani, pamene ife tikulowa mu mibadwo ya mpingo, Choyipa chirichonse chimene chinali mu mpingo woyamba uja, chinapitirira mwa wotsatira. Chinkangopitirira kumatsikira pansu mpaka potsiriza izo zikudzathera mu chinyengo chathunthu mu tsiku lotsiriza. Choyipa chirichonse chimangopitirira kukalowerera mu mpingo uliwonse, kalingaliro kakang'ono kalikonse kamene kanayambapo. Monga mu Genesis, mpesa, unayamba kukula, iwo unayanga njira yake kudutsa mpingo ndi kudzatulukira mu masiku otsiriza. Nzosadabwitsa Baibulo linati, “Odala ndi iwo amene adzapulumuka mu tsiku limenelo.” Inde, bwana, amene adzathawa zinthu zonsezi.



<sup>65</sup> Tsopano mufunsi Mulungu kuti...pamene ife tikuyankhula za Vumbulutso, mupempheni Iye kuti akupatseni inu vumbulutso la Izi. Pakuti Izi zikhoza kungodziwika kokha mwa vumbulutso, ndipo inu mukhoza kupulumutsidwa mwa vumbulutso. Inu muli ndi chidziwitso cha Izo, mwaluntha, koma inu simungapulumsidwe mpaka Izo zitaululidwa kwa inu. “Palibe munthu amene angamutchule Yesu Khristu, kokha mwa Mzimu Woyera.” Icho ndi chimene Baibulo limanena. Palibe munthu amene anganene kuti Yesu ndi Khristu kufikira iye atalandira Mzimu Woyera. Iye akhoza kunena kuti, “Abusa amanena chomwecho, Baibulo limanena chomwecho.” Izi ndi zooni. “Mpingo umanena chomwecho.” Izo nzoona. Koma iwe sumadziwa wekha kufikira Mzimu Woyera utaulula Izo kwa *iwe*, ndipo Iye nkukhala mwa *iwe*. “Palibe munthu amene angamutchule Yesu kukhala Khristu, pokhapokha mwa Mzimu Woyera.” Osati mwa chidziwitso, osati mwaluntha.

<sup>66</sup> Momwe angalipangire Baibulo chimenecho...Kuyesera kulifinyira Ilo, kulipangitsa Ilo kukhala lowayenera Ayuda, Akatolika, ndi Achiprotestanti, pamene iwo ndi osiyana monga usana uliri ndi usiku. Ndimaganiza kuti Ayuda amadziwa bwinoko kuposa zimenezo; ine ndikuganiza mwinamwake ndi nthawi yoti izo zifike, pamene izo zonse zikuyenera kupita mu chinyengo chachikulu ichi. Chotero, ndipo zinthu zonse mungokumbukira, ife sitingaziimitse izo, koma chinthu chokhacho chimene ife tingachite ndi kuponyera Kuwalako kumeneko, mwinamwake kudzipereka tokha ngati ofera ndi kuchokapo, chotero ndiyo njira yokhayo imene ife tingachitire izo. Koma ambiri akuyenera kudzachita izo. Ndipo chotero umo ndi momwe Baibulo limakhazikitsidwira ndi zinthu zimene ife tilowemo. Ngati sindipenyetsetsa, ine ndilowa mu zimenezo.

<sup>67</sup> Tsopano, chinthu choyamba pa Bukhu la Chivumbulutso, icho chimayamba ndi kuti Ilo ndi Vumbulutso la Yesu Khristu, yemwe Iye ali. Tsopano, Yesu Khristu ndi Mulungu Wamphamvuzonse. Ife tikudziwa zimenezo. Ndi angati amakhulupirira zimenezo? nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Iye ndi Mulungu Wamphamvuzonse, ndipo Iye ali ndi Dzina limodzi. Dzina limenelo ndi dzina lokhalo limene linaperekedwa pansu pa Kumwamba limene inu mukuyenera kupulumutsidwa nalo, Yesu Khristu. “Nchifukwa chiyani iwo amaliwopa Ilo pa dziwelo?” ndi zomwe ine sindingadabwe. Uh-huh. Mukuona? Ndi chifukwa chakuti mzimu umenewo unakwawiramo kale mu M’badwo wa Smurna; ndipo unadziyanga wokha mpaka kudutsa mu m’badwo wawukulu wa mdima uja, ndipo unachipanga icho kukhala chiphunzitsa, ndipo watulukamo ndi icho mu tsiku lotsiriza lino. Tsopano, ingopenyani mbiriyakale ndi Baibulo pamene ife tikudutsa sabata ino, momwe izo—momwe izo zikutulutsira zinthu zimenezo poyera.

<sup>68</sup> Tsopano chinthu chotsatira. Ilo linaperekedwa ndi Khristu kwa Yohane, kudzera mwa mngelo, kuti likaperekedwe kwa Yake (chiyani?) mipingo, kuti akawulule Izo kwa mipingo Yake. Ndipo nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja Lake zinali amithenga asanu ndi awiri a mipingo isanu ndi iwiri. Ndipo munthu aliyense amene adzakhale ndi Uthenga, adzakhala nawo iwo, Uthenga woona womwewo umene ukuyambira pachiyambi.

<sup>69</sup> Ndi zochuluka, pamene ife tizifika kumalo akuya kumeneko, kuti tikawone momwe Mulungu anasunthira zinthu izi, ndi zodabwitsa. Izo zidzangokupangitsani inu kufuula. Ine, kuweringa izo, ndipo kenako nkuyenda mozungulira pang'ono ndi kudzalira, nkubwerera ndi kudzakhalsano pansi, kenako nkuyenda mozungulira kwa kanthawi. Ine ndi wokondwa kwambiri kudziwa kuti: Kodi Mulungu anakhala bwanji wachifundo kwa ife kutilola ife kuti tiwone chinthu chimenecho mu ora limene ife tikukhalamoli? Bwanji, izo ziri monga Yesu ananenera, “Munthu anagulitsa zonse zimene anali nazo kuti akagule daimondi winawake.” Inu mumagulitsa kwa dziko, zinthu za mdziko, ndi chirichonse chimene chikukhudzana ndi china chirichonse, kuti mukhale ndi Ichi. Uko nkulondola, muyike nangula wanu yense pa Chimenecho. Ndi nangula wamoyo kuwona vumbulutso Lake la Mawu Ake.

<sup>70</sup> Tsopano, aliyense amene awerenga Iwo ndi wodala. Nkulondola uko? Ndipo ife tinanena mmawa uja, ngati iwe sungathe kuweringa, aliyense amene angamve Iwo akuwerengedwa, ndi wodala. Tsopano, Iwo akuyamba ndi mdalitso kwa iwo amene angakhale pansi ndi kumamvetsera Iwo akuwerengedwa, ndipo ndi themberero kwa aliyense amene angayesere kuwonjezera chirichonse kwa Iwo kapena kuchotsapo chirichonse kwa Iwo. Ndiye ngati Baibulo momveka limawulula kuti Yesu anali Mulungu Wamphamvuzonse, ndiye tsoka kwa iye amene angachotse izo mmenemo. Eya. Ilo ndi vumbulutso. Aliyense amene adzawonjezera kalikonse... Iwo ndi mndandanda wathunthu wa—wa Chivumbulutso; ilo ndi Bukhu lotsiriza la Mulungu, Mawu Ake otsirizira, Ake... Ndipo vumbulutso lirilonse limene lingabwere mosiyana ndi Iwo, ilo ndi la uneneri wabodza; si Mulungu, chifukwa ichi ndi Choonadi.

<sup>71</sup> Ndipo, kumbukirani, ili ndi bukhu lokhalo mu Baibulo limene Khristu analivomereza, Iyemwini. Taganizirani za zimenezo! Bukhu lokhalo, ndi vumbulutso la Iyemwini. Bukhu lokhalo limene Iye anayikapo chisindikizo Chake, ndipo anayikapo madalitso Ake ndi matemberero Ake. Madalitso kwa iwo amene adzalandire Ilo, themberero kwa iwo amene sadzalandira Ilo.

<sup>72</sup> Tsopano—tsopano ife tikufika pa chisumbu cha Patmo tsopano kuti tiyambe, ndi ndime ya 9. Malo oyamba, ife tikufuna kunena kuti ndi... Mutu wa izi ndi: *Masomphenya Apa Patmo*.

Izo zinachitika mu A.D., pakati pa A.D. 95 ndi 96. Malowo anali pa chisumbu cha Patmo. Malo ake ndi mamailosi sarte kuchoka pagombe la Asia Minor, kumadzulo, moyang'anizana ndi mpingo waku Efeso, mu Nyanja ya Aegean imene imachita malire ndi Mediterranean. Amenewo ndi malo amene icho chiri.

<sup>73</sup> Taganizani! Tsopano, chisumbu chaching'ono ndi cha mamailosi sarte kuchokera pa gombe la Asia Minor, mu Nyanja ya Aegean. Moyang'anizana ndi mpingo wa Filadel-... kapena mpingo wa Efeso, kumene Uthenga woyamba unaperekedwa, kumene Yohane anali m'busa nthawi imeneyo. Mwakuyankhula kwina, anayang'ana mmbuyo kummawa ndipo iye anali akuyang'ana molunjika ku mpingo wake, kuchokera pamene iye anali. Ndipo Uthenga woyambirira unali kwa mpingo wake, umene unkayimira m'badwo wa mpingo. Chabwino, masomphenyawa anaperekedwa kwa Yohane Woyera waumulungu, amene anali m'busa wa tchalitchi ku Efeso nthawi imeneyo.

<sup>74</sup> Kodi chisumbu ichi chinali chotani? Icho chinali kuti, ndipo chinali motani? Chabwino, izo zimadziwika mu mbiriyakale ngati chisumbu chamiyala chodzaza ndi njoka, zinkhanira, abuluzi, ndi zina zotero. Ndi mamailosi sarte kuzungulira kwake, ndipo chozadza ndi miyala. Chinkagwiritsidwa ntchito, mmasiku a Yohane, ngati Alcatraz. Malo amene ufumu wa Roma unkakaikako zigawenga, zigawenga zoyipa kwenikweni, zimene sakanatha kuzisunga mu ndende ndi zina zotero, iwo amakawaika iwo kunja uko pa chisumbu chimenecho kuti akafe; amakawasiya iwo kumeneko kufikira atafa.

<sup>75</sup> Funso: Nchifukwa chiyani Yohane anapita kumeneko? Munthu wa umulungu, munthu wolungama, munthu wa mbiri yabwino, wamakhalidwe abwino, sanakhalepo mmavuto, nchifukwa chiyani munthu ameneyu anakapezeka kumeneko? Baibulo linati, "Chifukwa cha Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu."

<sup>76</sup> Tsopano ife tiri ndi poyambira. Chisumbu cha Patmo, mu nyanja ya Aegean, mailosi sarte kuchoka pagombe, pafupifupi mailosi sarte kuzungulira icho, kwamiyala, kodzaza abuluzi ndi zinkhanira ndi zina zotero, ndipo chinkagwiritsidwa ntchito ngati ndende (ngati Alcatraz). Iwo amatenga mkayidi amene sangakhoze kumusunga mndende kuno, iwo... wachifwamba woyipa chomwecho, iwo amakamuyika iye ku Alcatraz.

<sup>77</sup> Ndipo tsopano iwo anamutenga Yohane woyera uyu... womaliza mwa ophunzira, ndipo mmodzi yekhayo amene anafa imfa yachilengedwe. Yohane, asanapite ku chisumbu, anaimbidwa mlandu wokhala "mfiti," ndipo anawiritsidwa mu mtsuko wa mafata kwa maora twente foro, osamuwotcha iye. Inu simungakwanitse kuwuwiritsa Mzimu Woyera kuti uchoke mwa munthu...?... Anamuwiritsa iye kwa maora twente-foro mu

mtsuko wa mafuta, popanda kuvulala kulikonse. Ndipo anati, chifukwa chimene—Aroma anapereka, amati, “Iye anali mfiti, ndipo anawalodza mafutawo.” Chimene malingaliro athupi angaganize! Tsopano, inu mwaona, pamene iwo atitcha ife “owerenga maganizo, ndi ambwebwe, ndi Bezezebule,” kodi inu mukuwona kumene mzimu wakale uja umachokerako? Koma inu mukuwona kumene Mzimu weniweni umachokerako? Ndi mibadwo ya mpingo. Mukuona? Maora twente-foro, kuwiritsidwa mmafuta otentha, obwatama, ndipo osamukhudza nkomwe iye. Oh, momwe Mulungu anamutchinjirizira iye mwa Iye ndi Mzimu Wake Woyera. Ntchito yake inali isanathe.

<sup>78</sup> Iwo anakamuyika iye pa chisumbucho kwa zaka ziwiri. Ndipo pamene Mulungu anali ndi iye kunja kumeneko kwa yekha, iye analemba Bukhu la Chivumbulutso pamene Mngelo wa Ambuye ankawulula izo kwa iye. Ndipo kenako mwamsanga pamene izo zinali zitatha, iye anabwerera ku dziko la kwawo ndipo anakakhala m’busa wa mpingo ku Efeso. Ndipo anafa ndipo anayikidwa mmanda ku Efeso, Yohane waumulungu.

<sup>79</sup> Oh, ndi poyambira bwanji tsopano! Chabwino, mpingo nthawi imeneyo pansu pa Yohane, kapena pansu pa kusautsika kwakukulu, Yohane akulemba ndime ya 9:

*Ine Yohane, yemwenso ndiri m’bale wanu . . . mu chisa- . . . ndi mzanu mu masautso, ndipo mu ufumu ndi mu chipiriro cha Yesu Khristu, ndinali pa chisumbu chotchchedwa Patmo, chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni wa Yesu Khristu.*

<sup>80</sup> Mwakuyankhula kwina, iye anatenga Mawu a Mulungu ndipo anali kuwatsimikizira Iwo, kuti Iwo anali Mawu a Mulungu, ndipo Khristu anabwerera kudzera mwa iye ndipo anadzachitira umboni kuti iye amalondola. Ndi zimenezotu. Mawu a Mulungu akuwonetseredwa mwa iye, kutsimikizira kuti iye anali wantchito wa Mulungu. Ndiye iwo sakanakhoza kukana Izo, chotero iwo anachita kumuza iye kuti anali “mfiti.” “Iye anawalodza mafutawo ndipo iwo sanamupweteke iye, ndipo iye anawalodza anthuwo ndipo iwo sanachiritsidwe, ndipo iye anali wam’bwebwe amene sakanakhoza . . . Mtundu winawake wa munthu woyipa, woyipa mzi- . . . mzimu wonyansa.” Ndipo ndi chifukwa chake iwo anakamuyika iye kunja uko, ankaganiza kuti iye anali wowopsya kuti azikhala pakati pa anthu. Koma iye anali akungochita chifuniro cha Mulungu, ndipo Mulungu anali ndi cholinga pansu pa chochitika chimenecho.

<sup>81</sup> Iye sakanakhoza kumugwiritsa iye ntchito, ndi mazunzo onse ndi zinthu, chifukwa oyera anali akubwera, “Oh, M’bale Yohane, ife tidzachita chiyani za *izi*? Ndipo ife tidzachita chiyani?”

<sup>82</sup> Yohane anali mneneri, ife tikudziwa zimenezo. Ndipo chotero iwo ankafunsa mafunso amenewa, chotero Mulungu

anangopangitsa Ufumu wa Chiroma kuti umutenge iye ndi kukamuika iye kunja uko pa chisumbu. Ndipo anati, “Tsopano, bwera, Yohane, ine ndikufuna ndikuwonetse iwe chinachake chimene chiti chidzachitike.” Wotsirizira wa atumwi, panalibenso wina woti alembe Izo koma Yohane. Chotero iwo anakamusiya iye pa chisumbu cha Patmo kuyambira A.D. 95 mpaka A.D. 96. Ndipo iye analemba Ilo, ndipo iye anati:

*Ine...ndine m'bale wanu, ndi mzanu mu chisautso,...*

<sup>83</sup> Tsopano, iye samalankhula za Chisautso Chachikulu. Chimenecho sichinali Chisautso Chachikulu, ndipo icho sichimabwera kwa Mpingo. Chisautso Chachikulu chimabwera kwa Myuda, osati kwa Mpingo. Chotero icho sichinali Chisautso, Chisautso Chachikulu.

<sup>84</sup> Tsopano ndime ya 10:

*Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva kumbuyo kwanga a...liwu, ...la lipenga,  
Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye,...*

<sup>85</sup> Tsopano, inu simungachite chabwino chirichonse mpaka poyamba mutalowa mu Mzimu; Mulungu sangakugwiritseni inu ntchito. Ndinu—ndinu—ndinu—ndinu...Kuyesetsa kwanu konse ndi—ndi kopanda ntchito kufikira mutachita izo mu Mzimu. “Ngati ine ndingayimbe, ndiziyimba mu Mzimu. Ngati ndingapemphere,” anatero Paulo, “Ndizipemphera mu Mzimu.” Ndiyeno ngati pali chirichonse chimene chingabwere kwa ine chimene chiri chabwino, icho chikuyenera kuwululidwa kwa ine mwa Mzimu ndi kutsimikiziridwa ndi Mawu (kuwonetseredwa ndi zotsatira zimene izo zimabala).

<sup>86</sup> Tsopano monga, mwa kuyankhula kwina, ngati ine ndingati Yesu Khristu analonjeza mu Mawu Ake kuti ngati ine ndidzalapa, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndidzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. Chinthu choyambirira kwa ine kuti ndichite ndi kulapa. Zawululidwa kwa ine kuti izo ndi zowona. Kenako nkubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndiye zotsatira zake zikhala: Ndidzalandira Mzimu Woyera.

<sup>87</sup> Ngati ine ndikudwala, ndipo Iye anandilonjeza ine kuti ngati ndingadzakhulupirire ndipo akulu ampingo nkudzandidzoza mafuta, kudzandipempherera ine, pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala. “Ambuye, ndikukhulupirira. Ndatsatira malangizo Anu, mulole mkulu andipempherere, andidzoze ndi mafuta.” Izo zakhazikitsa, izo zonse—izo zonse zatha.

<sup>88</sup> “Oh,” inu mukuti, inu “sindikumva kusiyana kulikonse, ngakhalebe.” Yesu sanabadwe, pamene Mulungu anamupha Iye

maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe, pamene Iye anali— Iye anali Mwanawankhosa wa Mulungu, anaphedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Koma mmalingaliro a Mulungu Mwini, Iye anali atachita kale. Ine sindinali kuno nthawi imeneyo, ngakhalenso inu; koma mu bukhu la Mulungu, ngati maina athu anali mmenemo, iwo anayikidwamo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

<sup>89</sup> Pamene Mulungu anena chirichonse, Icho chikuyenera kuchitika. Chotero pamene mukumana ndi zoyenereza za Mulungu, musingokumbukira, Mulungu adzadziwonetsera Yekha ndi kusamalira zina zonsezo, musingopita patsoyolo, iyo ndi ntchito yomalizidwa. Oh, kodi izo si zodabwitsa? Oh, mai, taganizani! Mungomuza Mulungu. . . Ndipo Mulungu anati, “Muchite *izi*, ndipo Ine ndidzachita *izi*.” Chabwino, ngati ndipita kukachita *izi*, Iye akuyenera kudzachita *izo*.

<sup>90</sup> Tsopano, mdierekezi amati, “Mwaona, Iye akuchedwa.”

Zimenezo sizimapanga kusiyana kulikonse. Daniele anapemphera nthawi yina ndipo anali masiku twente wani Mngelo asanafike kwa iye, koma sanakhumudwe nazo, iye ankadziwa kuti Iye abwera mulimonse, chotero iye anangodikirira mpaka Iye atafika kumeneko. Lingaliro lake ndi limenelo. Oh, pamenepo ndi pamene iwe ukupeza chikhulupiriro. Tsopano ife tikuyenera kuchoka pa zimenezo, ife tikhoza kukhala ndi msonkhano wa machiritso mofulumira, sichoncho ife? Uko nkulondola. Eya, wa chikhulupiriro. Koma ife tikufuna msonkhano wa wochiza-solo, kuti uchiritse mkatimu, chifukwa izo ndi zimene zingakutengereni inu nthawi yaitali, inu mupeza Moyo Wamuyaya. Moyo Wamuyaya sumasowa kapena kukalamba, iwo umakhalabe, umakhalabe chimodzimodzi.

<sup>91</sup> Tsopano, iye analowa mu Mzimu chirichonse chisanachitike. Chinthu choyambirira chimene iye anachita, iye anali pa chisumbu chatchedwa Patmo (zinthu zonsezi zimene iye anachita), ndipo iye anati, “Ndinamva Liwu,” ndi zinthu zina zonsezi. Koma chirichonse chisanachitike, iye anali mu Mzimu. Ndipo ngati inu mungazindikire izo mu Baibulo lanu, chirembo chachikulu Mzimu, Mzimu Woyera. Amen! Iye analowa mu Mzimu. Oh, ine ndikungoganiza kuti izo ndizodabwitsa:

*Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye. . .*

<sup>92</sup> Pa tsiku lanji? Tsiku la Ambuye. Tsopano, pamakhala zokambirana zazikulu. Tiyeni tingozitontholetsa zimenezo, kwa miniti yokha.

<sup>93</sup> Tsopano, monga ife tinanenera mmawa uja, ena amati vumbulutso, la Mateyu Woyera 17, linali “Petro.” Mpingo wa Katolika umati, “Iye anamanga Mpingo Wake pa Petro; iye anali papa woyamba.” Iye akanakhala bwanji papa ndi kukhala wokwatira? Mukuona? Ndipo anati, “Petro anapita ku Roma,

ndipo anayikidwa kumeneko.” Ndiye mudiuze ine malo amodzi ake, mbiriyakale kapena kulikonse, kumene Petro anapita ku Roma. Mukuona? Paulo anatero, koma osati Petro. Chabwino.

<sup>94</sup> Chotero ife tikupeza kuti kachitidwe konse aka ndi zinthu, zangokwawiramo. Mukuona? Koma, ndipo anthu lero ali... konsekonse kumene mungapite, iwo... Mpingo wina waukulu uli ndi msomali winawake umene unali mdzanja Lake. Inu mukudziwa ndi misomali ingati imene iwo anali nayo, misomali yovomerezeka, lero imene inali mu...? Naintini. Iwo ali ndi mafupa, iwo anali—iwo anali ndi zidutswa za miinjiro, ndi zogwira ndi chogwirira. Ndipo ife tiribe—ife tiribe zinthu zimenezo, ife sitikusowa zimenezo. Khristu ali moyo! Iye ali mwa ife, osati msomali wina, kapena chidutswa cha mtanda, kapena chidutswa cha fupa, kapena chinachake. Iye ndi Mulungu wamoyo, akukhala mwa ife tsopano, akudziwonetsera Yekha. Iye tiri ndi nkhani imodzi yokha ya chikumbutso, ndiyo Mgonero wa Ambuye, chikumbutso cha imfa Yake. Koma tikakamba zokhudza Khristu Mwiniwake, Iye alindi ife ndipo ali mwa ife. Ndipo ndicho chinthu chimene ife tikufuna kukupiza (ulemerero wa Mzimu Woyera) kudziko lapansi. Kukupiza Iwo mpaka Kuwala kuzime. Chabwino.

<sup>95</sup> Tsopano, a... Chotero, inu mwaona, ife tinatenga mbali ina imeneyo ya msewu. Inu mukudziwa nthawizonse ndimayesera kukhala ichi, ndipo Ambuye wathu wakhala akundiwululira ine; pali mapeto amodzi, ndi mapeto enanso, koma pakatikati pa msewu pali Choonadi. Kodi inu munazindikira Yesaya, pamene Iye ananena kuti padzakhala msewu waukulu? Yesaya 35. Ndipo inu mukukumbukira momwe abale athu ofunika achi Nazarene anakonda kuyimbira nyimbo ija, inu mukudziwa, “*Msewuwaukulu wa Chiyero. Msewuwaukulu wa Chiyero.*” Tsopano, ngati mungawerenge Baibulo lanu molondola, ilo silimati “msewuwaukulu wa chiyero.” Ilo linati, “Padzakhala msewuwaukulu ndi *kanjira*, ndipo udzatchedwa,” osati msewuwaukulu wa chiyero, koma “*kanjira* ka chiyero.” *Ndi* ndi mlumikizi amene amamaliza chiganizo chanu. Mukuona? “Padzakhala msewuwaukulu *ndi* *kanjira*, ndipo kazidzatchedwa *kanjira* ka chiyero,” osati msewuwaukulu wa chiyero.

<sup>96</sup> Mwaona, msewu umamangidwa, *kanjira*... Msewu wabwino ukamamangidwa, gawo lokwera kwambiri limakhala pakati, chifukwa zimapangitsa zinyalala zonse kuti zizigwera mbali ziwiri zonse. Ndi zimenezotu. Pamene munthu abwera kwenikweni kwa Khristu, iye amayika maso ake pa Khristu. Ngati iye akhala wotengeka pang’ono, iye amadzakhala wotentheka. Ngati iye ali wozizira pang’ono, iye amapita mbali ina iyi ndi kungokhala chabe nkha, kumbali ina iyo; mwawona, luntha lake. Koma chinthu chenichenicho chimakhala pakatikati pa msewu, ndi Mzimu wokwanira mwa inu, umakusungani inu kukhala mukutentha ndi kumayenda.

Ameni! Ndi kumadziwa mokwanira kuti mudzisunge nokha pansi pa kumvera kwa Mzimu, kuti muziyenda monga momwe Mzimu ukuyendera; osati kufikira kapena osati utapita, basi monga momwe Mzimu ukuyendera.

<sup>97</sup> Mpingo wa Katolika unati, “Vumbulutso linali Petro.”

Mpingo wa Chiprotestanti unati, “Anali Khristu.”

Koma Baibulo limaphunzitsa, “Linali Vumbulutso limene Iye anampatsa (Mulungu anamupatsa iye) la Khristu.”

“Inu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.”

“Wodala ndi iwe Simoni, mwana wa Yona, thupi ndi mwazi sizinaulule izi kwa iwe, palibe munthu, seminare, kapena nyumba ya ophunzira unsembe, chirichonse, chinaphunzitsa Izo kwa iwe. Koma Atate Anga amene ali kumwamba awululira izi kwa iwe. Ndiwe Petro, pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawuluka Iwo.”

<sup>98</sup> Tsopano tafika pamalo ena pano pamene iwo ali ndi malingaliro awiri osiyana. Tsopano, ine ndikhoza kukhala kuti ndikulakwitsa; ngati ndikutero, Mulungu andikhululukire ine. Koma nditsutsana ndi a Seventh-day Adventist amene amanena kuti, “Linali tsiku lachisanu ndi chiwiri limene iye anali, tsiku la Ambuye.” Abale a Seventh-day Advent, ndi ambiri a iwo, amanena kuti linali tsiku la sabata limene iye analitcha tsiku la Ambuye. Mpingo wa Chikristu umalitcha ilo, tsiku la Ambuye, “A—Lamlungu, tsiku loyamba.” Ndipo ife tikuzindikira nthawi zambiri kuti—kuti mpingo wa Chikristu panobe, lero, anthu Achiprotestanti, amalineni ilo ngati “Tsiku la Ambuye, Lamlungu.” Zimenezo si zamwamalemba. Lamlungu linali tsiku loyamba la sabata mu Baibulo, osati tsiku la Ambuye. Ndipo silinalinso tsiku lachisanu ndi chiwiri, sabata. Izo sizingakhale zotheka kuti ilo likhale limodzi la masiku amenewo chifukwa zinamutengera Yohane zaka ziwiri kuti alembe Chivumbulutso. Linali tsiku lanji limenelo? Padzakhala ochuluka a masiku achisanu ndi chiwiri amenewo ndi masiku oyamba anadutsapo.

<sup>99</sup> Baibulo, Chivumbulutso chinalembedwa kuyambira A.D. 95 mpaka 96, zaka ziwiri. Linali tsiku la Ambuye. Tsiku la Ambuye ndi lomwe linanena, ndipo ndi zomwe zinali. Yohane anatengedwera mu Mzimu kupita mu tsiku la Ambuye. Lero ndi tsiku la munthu, koma tsiku la Ambuye lidzafika. Mpaka mmusi kudutsa Malemba ife tipeza kuti iye anali mu tsiku la Ambuye, anagwidwira mu Mzimu ndipo anatengedwera kupita ku tsiku la Ambuye. Ameni! Uko nkulondola. Mwaona, iye anali mu tsiku la Ambuye. Baibulo limayankhula za tsiku la Ambuye. Ife tifika mu zimenezo mu kamphindi pang’ono, Malemba ambiri.

<sup>100</sup> Chinthu choyamba, tsiku la sabata, monga ife timayankhulira za ilo, tsiku la sabata sikusunga tsiku linalake. Ife tiribe lamulo loti tizisunga Loweruka ngati sabata. Ife



tiribe lamulo loti tizisunga tsiku loyamba ngati sabata, mu Chipangano Chatsopano. Baibulo linanena, mu Ahebri mutu wa 4, “Ngati Yesu akanawapatsa iwo mpumulo, kodi Iye sakanadzayankhula mtsogolo mwake za tsiku lina.” Uko nkulondola. Koma pamenepo patsalira mpumulo, kapena kusunga kwa sabata, kwa anthu a Mulungu. Pakuti ife amene tinakhulupirira, nafenso, tinalowa mu mpumulo Wake; ife tinasiya ntchito zathu monga Mulungu anachitira kwa Zake.

<sup>101</sup> Penyani! Oh! Ambuye alemekezeke. Ine ndikungomverera bwino kwambiri, ndapita kutsoglo kwa inemwini.

<sup>102</sup> Zindikirani, mu tsiku la sabata. Mulungu anapanga dziko lapansi mmasiku sikisi, ndipo tsiku lachisanu ndi chiwiri Iye analowa mu mpumulo ndipo sanabwerenso kudzamanga mayiko ena. Kenako Iye anapereka ilo kwa anthu ngati chikumbutso. Chifukwa simukanatha kulisunga ilo tsopano, chifukwa pamene mukusunga sabata kuno, mbali ina ya dziko lapansi ndi Lamlungu kenanso pamenepo. Mukuona? Chotero izo zinawonetsera kuti inali ya anthu, malo ndi nthawi ya Israeli. Komano pakutsalira kusunga sabata kwa anthu a Mulungu.

*Kwa ife amene...tinakhulupirira kuti tilowe mu mpumulo Wake...ngakhale ntchito... (Ine ndikubwereza Ahebri, mutu wa 4)...ngakhale ntchito zinali zitamalizidwa kuyambira ku maziko a dziko lapansi.*

*Pakuti iye anayankhula pamalo ena...motere,... tsiku lachisanu ndi chiwiri... .*

*Ndipo kenanso, iye anayika padera tsiku linalake, akuti mwa Davide, . . . (inu amene mumalemba, Ahebri 4)*

*Kenanso, iye anayika padera tsiku linalake, akuti mwa Davide, Mpaka lero, patapita nthawi yayitali; izo zimamveka, Pamene inu mumva...kapena anati, Pamene mumva mawu ake, musaumitse mtima wanu.*

*Pakuti ngati Yesu akanawapatsa iwo mpumulo, (tsiku) . . .kodi iye sakanayankhula mtsogolo mwake za tsiku lina.*

*Koma pamenepo patsalira...mpumulo (kapena kusunga kwa sabata) . . .*

<sup>103</sup> Mawu oti “mpumulo.” Sabata ndi mawu achirendo kwa ife, amene amatanthauza “mpumulo.” Ndi mawu Achihebri amene amatanthauza “mpumulo” tsiku, tsiku la sabata; osagwira ntchito, kupumula.

*Pakuti ngati Yesu akanawapatsa iwo mpumulo, . . . kodi iye sakana . . .yankhula za tsiku lina.*

*Koma apo patsalira...mpumulo (kapena kusunga sabata) kwa anthu a Mulungu.*

*Pakuti ife amene talowa mu mpumulo wake, . . . timasiya kuchoka ku zathu . . . ntchito, monga Mulungu anachitira kuchoka ku zake.*

<sup>104</sup> Ife sitimabwereranso ku izo tsiku lotsatira la sabata ndi kuyambiranso izo, ife talowa mu Mpumulo. Yesu poyankhula pa madalitso, Iye anati, “Munawamva iwo akunena a nthawi yakale, ‘Iwe usaphe ayi.’ Ine ndinena kwa inu, aliyense, amene amkwiyira m’bale wake popanda chifukwa, wamupha kale. Inu munamvapo akuti, iwo a nthawi yakale, ‘Iwe usachite chigololo.’ Limenelo ndi lamulo. Koma ine ndinena kwa inu, aliyense amene ayang’ana pa mkazi ndipo nkumusilira iye wachita naye kale chigololo mumtima mwake.” Nkulondola uko?

<sup>105</sup> Chotero zonse za zinthu izi zinali zikumbutso, zizindikiro chabe, zodabwitsa, kuyembekezera nthawi yeniyeniyo kuti idzabwere. Tsopano, pamene Yesu anatsiriza zimenezo, Mateyu 11, (madalitso), Iye anati:

*Idzani kwa Ine, inu nonse amene muli othodwa, otopa, ndi olemedwa, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo ku miyoyo yanu.*

*Tengani goli langa pa ine, ndipo phunzirani kwa ine; chifukwa ndine wofatsa ndi wodzichepetsa . . . (nkulondola uko?)*

*Idzani kwa ine, inu nonse amene muli othodwa ndi . . . olemedwa, ndipo ine ndidzakupatsani inu mpumulo ku solo yanu. (“Ngati mwagwira ntchito tsiku limodzi, masiku khumi, zaka zisanu, zaka-sarte faivi, zaka fifite, zaka nainte, ndipo mwatopa ndi kufooka, bwerani kwa Ine, Ine ndidzakupatsani inu Mpumulo. Ine ndidzachotsa katundu yense wa tchimo pa inu, ndi kudzalowa mwa inu, ndi kudzakupatsani inu mpumulo wangwiwo ndi kukhutitsidwa.”)*

<sup>106</sup> Tsopano, kodi mpumulo umenewo ndi chiyani? Mulole—tiyeni tingokhazikitsa izi pang’ono pokha, tiwone chimene icho chiri. Ena a iwo anati, “Bwanji, inu mupite mukajowine mpingo.” Ayi! “Mulembe dzina lanu mu bukhu.” Ayi! “Chabwino, mtundu winawake wa ubatizo wa mmadzi.” Ayi! Tiyeni tingokhazikitsa izo ndi kuwona chimene izo ziri. Kodi inu mungakonde kuti muchite zimenezo pomwe pano pamene ife tikudikirira? Ife tiwona kumene Yohane anapita. Kuti ndi mtundu wanji wa tsiku limene iye anapitako?

<sup>107</sup> Pamene Yesu anafa pa dziko lapansi, ndipo ntchito Yake nkutha, Iye anakalowa kwinakwake.

<sup>108</sup> Tsopano tiyeni tibwerere ku Yesaya mutu wa 28, ndi ndime ya 8. Ine ndikukhulupirira ndi pamenepo, tsopano, Yesaya 28:8. Ndipo tiyeni tiwerenge, Yesaya 28, mneneri akuyankhula zaka seveni handiredi ndi thwelofu izo zisanachitike. Tsopano, ndi ngati amene akufuna kuti adziwe chimene *sabata* loona

liri, mpumulo woona uli? Ndi izi apa. Tsopano, apa ndi pamene mneneri anayankhula izo, ndipo ndikuwonetsa pamene zinakwaniritsidwa. Penyani, Yesaya 28:8:

*Pakuti onse . . . (mneneri akuloseza za masiku ano)*

*Pakuti magome onse adzaza ndi masanzi ndi zonyansa, (anthu kumadya mgonero, amene amasuta ndi kumwa ndi kumachita mabodza ndi kuba) . . . chotero kuti palibe malo oyera.*

*Ndani amene iye adzamuphunzitse chidziwitso? . . .*

Ndani amene mungamuphunzitse chidziwitso lero?

<sup>109</sup> Ndi angati amene anamumvetsera Billy Graham lero? Unali ulaliki wabwino umene iye amalalikira, momwe anthu angakhulupirire bodza ndi kumangokhalabe mu bodza limenelo ndipo—ndipo ngakhale kumadzilungamitsa okha ndi kumaganiza kuti akuchita zabwino. Anthu wamba achi Amereka, iye anati, ndikumati, “Sefa ya munthu wanzeru, ndi ndudu ya munthu wosuta,” kumatenga limodzi la mabodza a mdierekezi, ndipo mmalo momupanga iye kukhala wopusa, chirichonse chimene iye ali, posuta chinthu choterocho ndiko kuyesetsa kumupanga iye kukhala munthu wanzeru. Iye ndi wopusa ngakhale kuti azisuta iyo, pamene a . . . pamene iyo ndi yodzaza ndi imfa ndi khansa ndi china chirichonse, ndipo komabe iye amawusutira iwo kutsikira mmapapo ake. Iye ndi wopusa. Osati a—osati a—sefa ya munthu wanzeru, ndipo palibe chinthu choterocho. Munthu wanzeru samagwiritsa ntchito zinthuzo.

<sup>110</sup> “Palibepo moyo pokhapokha iwo utakhala mu Oertel’s 92,” kapena chinachake chonga zimenezo. Palibepo Moyo kunja kwa Khristu, umenewo ndiwo Moyo woona weniweni. Nchiyani chimawapangitsa amuna ndi akazi kumwa zinthu zimenezo? Chifukwa iwo akuyesetsa kuti akhutitse ludzu limenelo mmenemo limene Mulungu anayika mmenemo kuti azimuchitira ludzu Iye, ndipo iwo akuyesetsa kukhutitsa izo ndi zinthu za mdziko. Ndipo ndicho chifukwa chimene tiri ndi zinthu zimenezo. Ndi chifukwa chake anthu amachita monga chomwecho, chifukwa iwo akuyesetsa kuthetsa ludzu limenelo limene liri mwa iwo la Mulungu, ndipo mdierekezi akuwapatsa iwo imfa mmalo mwa Moyo.

*. . . magome onse adzaza ndi masanzi . . .*

<sup>111</sup> Atsogoleri a mipingo, china chirichonse, amalankhula za izo, “Palibe vuto kumakhala ndi chisangalalo choyera chaching’ono.” Palibe chinthu ngati chimenecho!

*Ndani adzaphunzitse chidziwitso? ndipo kwa ndani iye ati adzamupange . . . kumvetsa chiphunzitso? iwo amene aletsedwa kuyamwa mkaka, ndi kuchotsedwa pa mabere. (Tsopano ife sitirinso makanda.)*

*Pakuti langizo liyenera kukhala pa langizo, lamulo pa lamulo; mzere pa mzere, mzere pa mzere; apa pang'ono, ndi apo pang'ono:*

*Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena iye adzayankhula ndi anthu awa.*

*Kwa amene iye anati, Iyi ndi... (chiyani? kusunga sabata!)... mpumulo mmene mungapangitse olema... (“Bwerani kwa Ine nonse olema ndi othodwa.”) ... angapangitse ofooka kuti apumule; ndipo uku ndiko kutsitsimutsa: komabe iwo sanamvere.*

<sup>112</sup> Kodi zimenezo zinachitika liti? Zaka seveni handiredi ndi thwelofu mtsogolo pamene pa Tsiku la Pentekoste milomo yachibwibwi inadzakhala pa anthu ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime ena ndipo, Mzimu Woyera unatenga miyoyo yawo, ndipo unaletsa zinthu zawo za chidziko. Kenako iwo analowa mu Mpumulo ndi Khristu. Paulo anati, mu Ahebri mutu wa 4, “Ife amene talowa mu mpumulo Wake tapuma ku ntchito zonse za dziko lapansi monga Mulungu anachitira pa tsiku la kulenga Kwake, Iye analowa mu mpumulo Wake, ndipo ife timalowa ndi Iye ntchito zathu za padziko zikatha.” Pamenepo ndi pamene pali Sabata lanu lenileni, loona.

<sup>113</sup> Chotero Paulo ananyamulidwa ndipo analowa mu Mzimu wa Sabata umenewo, ndipo anasamutsidwa ndi Mzimu Woyera njira yonse mpaka tsiku la Ambuye.

<sup>114</sup> Nchifukwa chiyani timakhala ndi nkondo? Nchifukwa chiyani timakhala ndi mavuto? Nchifukwa chiyani fuko limalimbana ndi fuko? Yesu anabwera, Kalonga wa Moyo, ndipo iwo anamupha Iye.

<sup>115</sup> Mu masabata angapo, kapena ngakhale pakali pano, pali mphalapala ndi Santa Clause ndi—ndi mabelu ndi mitundu yonse ya zinthu itakolekedwa, umene uli mwambo wachikunja. Ndi nkhani ya mpingo wa Katolika. Anthu kumalipira mitengo yayikulu ndi kumasinthana mphatso ndi zinthu monga choncho, chikunja! Khrisimasi ndi tsiku lopembedza.

<sup>116</sup> Ndipo tiri pomwepo, Khristu sanabadwe pa tsiku la twente faivi la Disembala ndiponso. Iye sakanatero. Ngati munakhalapo ku Yudeya, mapiri amakhala odzaza ndi chipale, moyipirapo kuposa momwe zimakhallira kuno. Anabadwa mu Epulo pamene chirengedwe chonse chimatulukira.

<sup>117</sup> Tsopano, koma ndi mwambo wawo. Ndipo bwanji—chifukwa chiyani ife timachita zinthu zimenezo? Chifukwa timatsatira miyambo ya anthu mmalo mwa malamulo a Mulungu. Iwo... Chinachake chonga chimenecho sichingakhale chofunikira, koma iwo anangopanga tsiku lamalonda kuchokera mwa ilo. Ndi chamanyazi, chochititsa manyazi kuti iwo azichita zinthu ngati zimenezo. Mwambo wachikunja! Kodi ndi liti limene Santa

Claus anakhalapo ndi chochita ndi Yesu? Ndi liti limene kalulu wa Isitara kapena nkhuku kapena . . . itapakidwa mangamanga ndi mtundu wina wa utoto kapena chinachake, kapena mtundu wina wa kalulu woyera kuti angakhale ndi chochita ndi chiwukitsiro cha Yesu Khristu? Kodi inu simukuwona momwe dziko lamalonda . . . ?

<sup>118</sup> Ndi chifukwa chake iwo amagulitsa mabuku awa a gwedemula, ndi zithunzi zonyansa, ndi zovunda, ndi zinthu monga zimenezo, ndi chifukwa chakuti chikhalidwe cha anthuwo chimakhumbira zamkutu zoterozo. Ndi chifukwa chakuti pali chinachake cholakwika mu mtima, iwo sanalowepe konse mu Mpumulo umenewo ndi Mulungu ndi kusiya zinthu izi. Pamene iwo abwera mwa icho ndi kulandira Mzimu Woyera, ndiye kuti athana nalo dziko lapansi ndi zinthu za mdziko.

<sup>119</sup> Mulungu anamusamutsira iye. Oh, sindikukhulupirira kuti iye anatengedwa monga Paulo, tsopano, kukwera kupita mmiyamba mwachitatu ndipo nkukawonako zinthu. Chabwino, Mzimu Woyera wofunikira unachita masabata angapo apitawo, pano, unandirola ine ndiwone . . . Mwakuyankhula kwina, Ine ndimaiwopa imfa, ndipo Mzimu Woyera unanditengerako ine ndipo unakandisonyeza ine chimene icho chinali. Inu munawumva umboniwo. Kenako pamene ine ndinadzabwerera, “Ndiye, imfa, mbola yako ili kuti?” Ndinasamutsidwa kuti ndikawone chimene chinali kuseri kwa katani. Iye anandilola ine kuti ndibwerere kudzakuzani inu kuti kuseri kumeneko ife si mizukwa ndi mizimu, ife timakakhala amuna ndi akazi, achinyamata, osafa konse, osadwala konse, basi kuseri kwa chopimba. Imfa siingachitense chirichonse kwa inu kuposa kukukokerani inu ku Malo amenewo.

<sup>120</sup> Tsopano, Yohane anasamutsidwa kuchokera ku chisumbu cha Patmo, mu Mzimu, kupita mu tsiku la Ambuye. Lino ndi tsiku la munthu, anthu akumenyana, koma tsiku la Ambuye lidzabwera pamene maufumu awa adzakhala maufumu a Ambuye wathu ndi a Khristu Wake, zikadzatero padzakhala Zakachikwi zopambana. Tsiku la Ambuye, tsiku lakudza Kwake, chiweruzo Chake, limenelo lidzakhala tsiku la Ambuye.

<sup>121</sup> Lero ndi tsiku la anthu, ndipo nchifukwa chimene iwo amakukankhani kankhani ndi kumachita nanu zimene iwo akufuna kuchita, koma idzakhhalapo nthawi . . . Amakutchani inu . . . iwo amakutchani inu tsopano, “woyera wodzigudubuzana ndi wotentheka,” koma idzafikapo nthawi, mwaona, imene iwo sadzachita zimenezo. Iwo adzafuula ndi kuisisima ndi kudzagwa pa mapazi anu. Baibulo linati, mu Malaki 4, inu muzidzayenda ngakhale pa maphulusa iwo atatha kuwotchedwa; osawasiyira iwo muzu kapena nthambi. Ndizo ndendende zomwe Baibulo limanena, “Olungama adzayenda pa maphulusa a oipa.” Ndizo ndendende. Sidzawasiyira muzu kapena nthambi, palibe choti adzabwererense. Ndipo iwo adzathedwa. Tsopano ili ndi tsiku

la munthu (zochita za munthu, ntchito za munthu, mpingo wa munthu, malingaliro a munthu), koma tsiku la Ambuye likubwera.

<sup>122</sup> Tsopano, iye anali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye. Chabwino, ndipo chinthu choyambirira chimene iye anachimva pamene anali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye... Tsopano ife tiri ndi ndime ya 10:

...mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndipo iye  
anamva... a... liwu, longa... lipenga,

<sup>123</sup> Tiyeni tisadutse fanizo limodzi, tsopano. Ngati tikuyenera kudzalitenga ilo mawa, ife tikhoza kudzalitenga ilo. Winawake azingoyang'ana wotchi, kuti nthawi isandithere.

<sup>124</sup> Chabwino, tsopano, "...ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye." Tsopano kumbukirani, chinthu choyambirira chimene inu muyenera kuchita ndi chiyani? Kulowa mu Mzimu. Kodi mavumbulutso awa adzabwera bwanji kwa inu? Lowani mu Mzimu. Inu mudzalandira bwanji Mzimu Woyera? Lowani mu Mzimu. Lowani mu Mzimu!

<sup>125</sup> Pamene inu munali wochimwa ndipo mukapita kokavina, inu munkakalowa mu mzimu *umeneu*. Oh, mai, mumayamba kuwomba mmanja ndi kugwedeza mapazi anu, ndi kumasangalala, ndi kuponyera chipewa chanu pansu, ndi kumayenda yenda, kumachita mopusa. Inu munkakhala mu mzimu wa zimenezo. Kodi inu mungalingalire munthu, anali wovina, akupita kokavina, ndikuti, "Chabwino, ndipo inu nonse mukukhala ndi nthawi yabwino, ine ndikuganiza."

"Oh!" iwo angati. "Iwe maluwa apakhoma, choka pano!" Mukuona?

<sup>126</sup> Kupita ku masewero a mpira, winawake nkumugwetsa yemwe amakhala ndi liwiro, kapena chinachake chimzake, nkukhala ndi kumangoyang'ana, ndikuti, "Chabwino, ndikuganiza zimenezo ndi zabwino." Ayi, inu simungakhale wokonda mpira, simungakhale weniweni... simungakhale mu mzimu wa mpira. Pamene winawake amugwetsa waliwiro, iwe umaimirira ndi kudzafuula, "Psyii! Mai! Wapambana!" Kugwetsera pansu chipewa cha winawake kuchokera pamutu pake monga *choncho*, nkusakhalapo wina wonena mawu za izo.

<sup>127</sup> Ndiye mu mpingo mukalowa mu Mzimu, mumadzuka ndi kufuula, "Ulemerero! Aleluya! Ambuye alemekezeke!"

Winawake nkutembenuka, nkuti, "Woyera-wodzigudubuza." (Oh, M'bale Wood...)

<sup>128</sup> Ine ndikufunsani inu funso. Ngati ndife oyera odzigudubuza chifukwa timachita zimenezo, ndiye iwowo ndi *osayera*-odzigudubuza kunja kumeneko. Ine kulibwino ndikhale woyera-wodzigudubuza (Sichoncho inu?) kuposa kukhala wosayerayo. Mai! Ndithudi! Osayera-odzigudubuza.

<sup>129</sup> Tsopano, iye anali mu Mzimu. Iye analowa mu Mzimu, kenako zinthu zinayamba kuchitika. Ndiyeno pamene iye analowa mmenemo, iye anamva lipenga. Tsopano, lipenga nthawizonse limalengeza kufika kwa chinachake. Monga mukamabwera. . . A—mfumu ikuyandikira, iwo amaliza lipenga. Pamene Yesu azidzayandikira, Iye adzaliza lipenga. Nkulondola uko? Pamene Yosefe amapita, iwo ankaliza lipenga. Ndipo tsopano chinachake chikubwera, Yohane analowa mu Mzimu ndipo anamva lipenga. Iye anamva lipenga, ndipo anapotoloka kuti ayang'ane chimene chinali kumbuyo kwake pamene iye anamva lipengalo; iye atalowa mu Mzimu.

<sup>130</sup> Mwinamwake anali kuvina, akulumpha, akuthamanga kuzungulira pa chisumbucho. Iye anali ndi nthawi yabwino, iye anali mu Mzimu. Chotero, ndipo iye. . . Zimenezo zikhoza kumveka mosinjirira, koma ine sindikutanthauza izo mwanjira imeneyo, mwaona. Iye akanakhoza! Ndizo. . . chabwino, iye mwinamwake ankachita zimenezo. Ine ndikukhulupirira kuti iye anali ndi nthawi yabwino mu Mzimu, akumangoyamika Mulungu, chifukwa izo ndi ndendende zomwe zinadzachitika pamene Mzimu unadzagwa pa iwo pa nthawi yoyamba. Pamene Mzimu Woyera unadzagwa pa iwo, iwo anadzandima ngati amuna ndi akazi oledzera, ndipo anachita ngati iwo anali ataledzera, ndi kumangobwebweta. Ndi kumaitana. . . kumapitirirabe monga chomwecho mpaka anthu anati, “Anthu awa akhuta vinyo watsopano.” Umo ndi momwe iwo anachitira nthawi yoyamba, chotero Mzimu unadzabweranso, iye mwinamwake anachita mwanjira yomweyo. Mukuona? Palibe chatsopano za ichi—chinthu ichi, ichi ndi chipembedzo cha *nthawi-yakale*. Eya.

<sup>131</sup> “Mu Mzimu pa tsiku la Ambuye.” Tsopano, ife tikumva izi. Tsopano chiyani? Tsopano, kodi iye ankachita chiyani? Iye anasamutsidwa kuchoka pa chisumbu tsopano, mu Mzimu, kupita ku tsiku la Ambuye. Ndipo mwamsanga pamene iye anakafika mu tsiku la Ambuye, iye anamva lipenga. Ndi chiyani ilo? Ndiye kuti Winawake akufika. Wamkulu akufika. Lipenga limamveka, Winawake akubwera! Iye anayang'ana! Aleluya! Lipenga:

*Akuti, Ine ndine Alfa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza. . . (osati kulengeza za munthu wachiwiri kapena wachitatu, koma Munthu yekhayo). . . Ine ndi zonse ziwiri Alfa ndi Omega, . . . (“Ndisanakuwonetseni inu chirichonse, Ine ndikufuna ndikuuzeni kuti Ine ndine ndani!”)*

<sup>132</sup> Chachikulu cha mavumbulutso onse ndi Umulungu, Umulungu Wapamwamba wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Inu simungafike poyambira poyamba mpaka inu mutakhulupirira zimenezo, tulukani. . . Izi ndi zomwe Petro ananena, “Lapani, ndipo kenako muwone Umulungu. Mubatizidwe mu Dzina

la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiwo cha machimo ako, ndiye mukatero ndinu okonzeka kupita mu Mzimu.” Chinthu choyamba inu mukuyenera kudziwa ndi Umulungu wa Khristu. “Ndine Alfa ndi Omega! Ndine wochokera ku A mpaka Z, palibenso wina koma Ine. Ine ndinali pachiyambi, Ine ndidzakhala pamapeto. Ine ndine Iye amene analipo, amene alipo, ndipo ali nkudza, Wamphamvuzonse.” Taganizani za Zimenezole! Izo ndi zimene lipengalo linanena.

133 Samala Yohane! Iwe walowa mu Mzimu, chinachake chiwululidwa kwa iwe. Ndi chiyani chimenecho? Kulira kwa lipenga, chinthu choyamba, “Ndine Alfa ndi Omega.” Choyambirira cha mavumbulutso onse. (Oh, wochimwa, gwada, lapa tsopano nthawi isanathe kwambiri.) “Ndine Alfa ndi Omega.” Ndicho chinthu choyambirira chimene Iye anamulola iye kuchidziwa, yemwe Iye anali. (Ndi ndani akuyandikirayu? Kodi uyu ndi Mfumu Yesu? Mfumu Mulungu? Mfumu Mzimu Woyera?) Iye anati, “Ndine zonse za Izo! Ndine kuyambira ku A mpaka Z. Ndine chiyambi ndi mapeto. Ndine Wachisavundiyo, Wamuyaya Uyo!”

134 Patangopita kanthawi pang’ono ife tikumuwoona Iye mu mawonekedwe Ake ofutukuka ka seveni, penyani chimene Iye ali pamenepo. “Ine ndine chiyambi ndi mapeto. Ine ndine Alfa ndi Omega, woyamba ndi wotsiriza. Ine ndinalipo pasanakhale woyamba; ndipo sipadzakhalanso wotsiriza, Ine ndidzakhala pobe,” mwakuyankhula kwina. “Woyamba ndi wotsiriza!”

*. . . ndipo, Chimene iwe uti uchiwone, ulembe mu bukhu, ndipo uchitumize. . . kwa mipingo seveni imene ili ku Asia; ku Efeso, . . . Smurna, . . . Pergamo, . . . Tiyatira, . . . Sarde, . . . Filadelfeya, ndi ku Laodikaya.*

135 Chabwino, choyamba cha mavumbulutso onse ndi Umulungu Wapamwamba wa Yesu Khristu. Inu mukuyenera kudziwa kuti Iye ndi ndani pamene inu mumva Liwu. Chabwino, Liwu lomwe lija limene linamveka pa Phiri la Sinai, Liwu lomwe lija limene linamveka pa Phiri la Chiwalitsiro, Mmodzi yemweyo, “Mmodzi wonga Mwana wa munthu.”

136 Tsopano penyani mu ndime yotsatira iyi. Chabwino:

*Ndipo ndinapotoloka . . . (Mutu 12 tsopano.)*

137 Ife tiyisiya mipingo iyi yokha kwa miniti, chifukwa sabata yonseyi tikubwera pa mipingo iyi. Mwaona, chotero ife tingodutsapo pa iyo.

138 Koma Iye anati, “Izi . . . Ine ndikulangiza iwe kuti utumize Uthenga uwu umene Ine ndikukuwonetsa iwe.” Ndi ndani? “Ndine woyamba ndi wotsiriza. Ndine Wapamwamba Uyo. Ndine Wamphamvuzonse Uyo. Ndipo Ine ndabwera kuti ndidzakuuze iwe kuti ndikukupatsa iwe Uthenga wa kwa mipingo isanu ndi iwiri. Ine ndikufuna kuti ulembe Iwo,



ukonzekeretse Iwo.” Mukuona? “Ndipo mipingo isanu ndi iwiri imene ili ku Asia.” Tsopano, iyo inali mipingo kumeneko nthawi imeneyo ndi chikhalidwe mwa iwo chimene chinkaimira mibadwo ya mpingo iyi imene inkabwera.

139 Tsopano:

*Ndipo ndinapotoloka kuti ndiwone liwu limene linkayankhula kwa ine. Ndipo ndikutembenuka, ndinawona zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide;*

140 “Zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide.” Tsopano, ndi. . . Kutanthauzira kwa King James, kumene mwinamwake inu muli nalo la Scofield kapena—kapena mwinamwake Thompson Chain, kapena ena a iwo, si zolondola pamenepo. Silimanena kuti zoyikapo makandulo, ilo limati zoyikapo nyali; zoyikapo nyali, ine ndikukhulupirira, ndiwo mawu olondola, okhoza amene ananenedwa mu kumasulira koyambirira. Mwaona, mwakuyankhula kwina, zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri izi zinali mipingo isanu ndi iwiri. Iye akudzanena mtsogolo pang’ono, a-. . .mu ndime ya 20 apa, “Zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zimene iwe unaziwona ndi mipingo isanu ndi iwiri.” Chotero, inu mwaona, ngati iyo ikanakhala kandulo, ikanatha posakhalitsa ikanayaka nkutha, mu kanthawi pang’ono chabe. Koma si makandulo, ndi—choyikapo nyali. Ilo likuchipereka icho ngati choyikapo nyali. “Potembenuka ndinawona wina ngati Mwana wa munthu atayima pakati pa. . . pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri.”

141 Tsopano—tsopano taonani. Kandulo ikanatha posachedwa, ikanazima, sipakanakhalanso chirichonse kwa iyo, mu maora pang’ono iyo ikanatha. Koma choyikapo nyali, choyikapo nyali chonga ichi, . . .

142 Apa, tiyeni—tiyeni titenge Lemba apa, tiyeni—tiyeni titenge Zakariya 4:1, ndiye tikhoza mwinamwake kudzatenga kuchokera kwa Zakariya pamenepo chimene ife tikufuna. Zakariya 4:1, ndipo ine ndikukhulupirira ndiye kuti mwinamwake mu izi ife titha ku—kukokera pamodzi chimene tikuchifuna. Ine ndikulephera kumupeza Zakariya mu Zefaniya, ndingatero? Chabwino. Chabwino. Baibulo langa lakale latsala pang’ono kutha. Zakariya 4:1, mvetserani mwatcheru tsopano, inu mupeza chithunzi chokongola apa:

*Ndipo mngelo. . .*

143 Mneneri, tsopano, basi zaka faivi handiredi ndi naintini Khristu asanabwere:

*Ndipo mngelo amene anayankhula ndi ine anadzabweranso, ndipo anandidzutsa ine, monga ngati munthu amene wadzutsidwa kutulo, (Tsopano mneneri ali mu masomphenya.)*

*Ndipo iye anati kwa ine, Iwe ukuwona chiyani? Ndipo ine ndinati, ine ndayang'ana, ndipo taonani choyikapo kandulo (Tsopano, mawu omwewo amamasuliridwa ngati "choyikapo nyali.") chonse cha golide, ndi mbale pa...pamwamba pake, (Imeneyo inali nyali.) ndi nyali zake zisanu ndi ziwiri pamenepe, ndi mapaipi asanu ndi awiri pa nyali zisanu ndi ziwirizo, zimene ziri pamwamba pake: (Mwaona, mibadwo ya mpingo yomweyo ikubwera. Mukuona?)*

*Ndi mitengo iwiri ya azitona pambali pake,... (Tsopano, mtundu wANJI wa... Nchiyani chimene iwo ankayatsa mu nyali zimenezo mu nthawi ya Baibulo? Pali amene akudziwa? Mafuta. Mafuta a mtundu wANJI? Mafuta a Azitona.) ...mitengo iwiri ya azitona... (Ndi chiyani chimenecho? Chipangano Chatsopano ndi Chakale; ndi iwiri itayima pambali pake.) ...umodzi ku mbali ya kumanja kwa mbaleyo, ndipo wina mbali ya kumanzere kwake.*

*Ndipo ndinayankha ndipo ndinayankhula ndi mngelo amene amayankhula ndi ine, kuti, Izi ndi chiyani, ambuye wanga?*

*Ndipo mngelo amene ankayankhula ndi ine anayankha ndipo anati kwa ine, Iwe sukudziwa chimene izi—izi zingakhale? Ndipo ine ndinati, Aji, ambuye wanga.*

*Ndipo iye anayankha ndipo anayankhula kwa ine, kuti, Awa ndi mawu a YEHOVA kwa Zerubabelo, akuti, Osati ndi mphamvu, osati ndi mphamvu, koma ndi mzimu wanga, atero YEHOVA wa makamu. (Iye adzabwezeretsa Yerusalemu.)*

144 Tsopano, kodi choyikapo kandulo ndi chiyani? Ndi choyikapo nyali. Ndipo zindikirani kukongola kwake. Apa, pamene iye anatembenuka, iye anamuwona Wina uyu ngati Mwana wa munthu apa atayima pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide, chimene chikutanthauza mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo imene ili nkudza. Ndipo paipi iliyonse, kapena—kapena choyikapo nyali, chitalumikizidwa ndi m'phika waukulu wa mafuta. Ndipo mu mafuta awa munatuluka nyali yaying'ono yosawoneka bwino imene inali ndi chingwe mkati mwake chitapachikidwa mmafutawo. Ndipo bola... Iwo anatsanulira mafuta pamwamba pa choyikapocho, chomwe chinadzaza tsinde lalikululu, ndi nthambi yayikululu, ndipo iyo inatulukira mu tsinde, monga chonchi. Ndipo nyali yokhala ndi chingwe cholendewera pansu, iyi—paipi iyi yolowa mu... imapitirirabe kuyaka, usana ndi usiku. Inu simunkachita kuti muziiyatsa iyo, iyo siinkazima konse; iwo ankangotsanulira mafuta mu paipi yaikuluyo. Ndipo zoyikapo nyali izi zimene

zimatuluka monga chonchi, zimakhala ndi nyali zitakhala pamwamba pake. Chingwe cha nyali chimatsikira mkati umu, chimatenga moyo wake kuchokera mmenemo. Oh, ndi zosiyana bwanji ndi kandulo. Ndi zosiyana bwanji! Ndi choikapo nyali, ndipo chikukoka mafuta.

<sup>145</sup> Tsopano, zoyikapo nyali izi, moto umene unali pa zoyikapo nyali izi mu Chipanganano Chakale. Iwo akayatsa nyali imodzi, iwo samayatsanso nyali yotsatira ndi moto womwewo umene anali nawo mu dzanja lawo. Iwo ankayatsa nyali imodzi, kenako ankayinyamula iyo ndi kuyatsira nyali inayo, kenako nkuyisiya iyo pansu. Ndipo amayatsa nyali iyi, ndipo kenako ankatenga ndi kudzayatsa nyali iyi ndi moto womwewo umene iwo anawuyamba poyambirira. Oh, ndikuyembekeza kuti izo sizikudutsa pamwamba pamutu wanu. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” moto womwewo (Mzimu Woyera) umayatsa uliwonse wa mipingo imeneyo kudutsa mibadwo.

<sup>146</sup> Kodi Yesu sananene mu Yohane Woyera 15, “Ine ndine mpesa, inu ndinu nthambi”? Tsopano, Iye ndiye Mpesa wawukulu, ife ndi nthambi. Tsopano, mpesa sumabala zipatso...

<sup>147</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...kuti mutha kutenga mtengo wa zipatso zowawasa, ngati lalanje, ndipo mutha kutenga a—nthambi kuchokera pa—kuchokera, chabwino, ine ndinganene, mtengo wa mphesa, ndi kugawaniza malo aang’ono mu mtengo wa lalanje ndi kudzayikamo chipatso cha mphesa mmenemo, icho chimera. Mukapita cha apa ndi kukatenga nthambi ya mandimu ndi kukaiyika iyo pa mtengo wa lalanje, iyo idzakula, kapena mutenge makangaza, ndipo mutenge iwo, kapena, chipatso chowawasa chirichonse, namchesi kapena manyumwa, chirichonse cha zipatso zowawasa zimenezo, ndi kukaziyyika izo mumtengo uwu, ndipo chiphukira kuchoka pa moyo wa mtengo wa malalanje uwo; koma sichimabereka malalanje. Iwo udzabala zipatso za mphesa, udzabala matangelo, iwo udzabala mandimu, koma ukukhala moyo kuchokera pa moyo wa mpesa weniweniwo, koma ngati mpesa umenewo ungasatutse mpesa wina...nthambi ina, iyo idzakhala ya moyo womwewo umene uli mmenemo, iyo izidzabala malalanje. Chifukwa, pachiyambi, mu muzu wake muli moyo wa mtengo wa lalanje, koma ina ikhoza kumakhala moyo kuchokera mwa iwo bola ngati uli mtundu wa chipatso chowawasa. Koma iwo sungabereke chipatso choyambirira, chifukwa icho si chapachiyambi.

<sup>148</sup> Umo ndi momwe mpingo uliri. Iwo awugawaniza Mpesawo ndipo amezatsanitsamo Chipresbateria, Methodisti, Baptisti, ndi zina zotero monga choncho. Iwo ukubala chipatso cha Baptisti, chipatso cha Presbateria, chipatso cha Methodisti, koma ngati zitati...mtengo umenewo ukadzabereka mpesa

wina, iwo udzakhala mtundu wampesa womwewo umene Iwo unabweretsa pa Tsiku la Pentekoste: Mpesa wapachiyambi! Iwo udzayankhula mu malirime ndipo udzakhala ndi mphamvu ndi zizindikiro za Khristu woukitsidwa mmenemo. Chifukwa chiyani? Chifukwa ukukula kuchokera mu chirengedwe chimene iwo unadzalidwamo. Kwenikweni, iwo sunabzalidwe mmenemo, iwo wabadwira mmenemo! Ambuye alemekezeke! Oh, mai! Sindinaganize za izo nthawi imeneyo.

<sup>149</sup> Mwaona, yinayi yamezanitsidwamo; iwo anawamezanitsa iwo mu mtengomo, kuti iwo abale zipatso zamtundu wawo. Iwo sangatenge *Ichi*. Iwo sakhulupirira *Icho*, chifukwa iwo sanayambe adziwapo kalikonse ka Izo. Koma ngati iwo anabadwira mu Moyo womwewo umene unachokera mu mtengo umenewo, ndicho chinthu chokhacho chimene iwo angabereke, ndi Moyo wa tsinde lapachiyambi.

<sup>150</sup> Masinde a nyali awa onse amakwanira mu mphika umodzi waukulu, chogwirira chachikulu chimodzi, ndi zosiyanasiyana naini. . . kapena zogwira nyali seveni zosiyanasiyana zotuluka kuchokera pa izo. Ndipo pamene izo zimatero, iliyonse ya nyali zimenezo zinali kutunga kuchokera mu m'phika wawukulu wa moyo wake. Ndipo kuwala kwake kunali chifukwa chakuti kandulo yake inali itamizidwa mu mbiya yayikuluyi. Oh, ndi chithunzi chokongola bwanji cha imodzi ya nyenyezi zisanu ndi ziwiri izo (izo zimaimira zimenezo) ndi moyo wake uli pamoto ndi Mzimu Woyera apa. Ndipo izo. . . Mwa chikhulupiriro akuyaka ndi Mzimu Woyera, ndipo moyo wake ndi kandulo, kapena osati kandulo, koma chingwe chimene chamizidwa mu Mzimu Woyera (mwa Khristu), ndipo kudzera mu chingwe chimenecho iye akukoka Moyo wa Mulungu kuti upereke Kuwala ku mpingo wake. Oh, ndi chithunzi bwanji cha wokhulupirira woona! Ndi mtundu wanji wa Kuwala umene iye akupereka? Kuwala kwa mtundu womwewo kumene kunalipo pamene kandulo yoyamba inayatsidwa.

<sup>151</sup> Pamene m'badwo wa mpingo woyamba unayamba, unali wa Efeso. Paulo, mngelo wa mpingo umenewo, imodzi ya nyenyezi. Pali nyenyezi zisanu ndi ziwiri chimene chikutanthauza angelo asanu ndi awiri, asanu ndi awiri "amthenga." Sabata ino ndikhonza kutenga Lemba ndi mbiriyakale ndi kukutsimikizirani inu kuti chirichonse cha izo ndi choona mwa mngelo aliyense, ndipo mngelo aliyense anali ndi Kuwala komweko. Uko nkulondola. Ndiyeno pakati pa mibadwo iyi, Mmodzi wamkulu uyo amene ali nkudza.

<sup>152</sup> Zindikirani, tsopano iwo akutunga kuchokera mu mtsuko wawukulu uyu wa Mafuta, Kuwala. . . moyo wamizidwa mwa Khristu. Inu mwafa, ndipo moyo wanu wabisidwa mwa Khristu kudutsa. . . kapena wabisidwa mwa Mulungu kudzera mwa Khristu, ndipo mwasindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Palibe njira iliyonse imene ingakuchotseni inu pamenepo. Kodi

mungachite bwanji zimenezo? Palibe amene angakusokonezeni inu. Mapeto a moyo wanu akuyaka ndi Mzimu Woyera; oh, akuyaka, kupereka Kuwala. Kodi mathero ena a moyo wanu amididwa kuti? Mwa Khristu. Inu ndi akufa ndipo mwabisidwa mwa Khristu, Mzimu Woyera, ukutsekereza izo pamenepo kuti inu muthe. . . mdierekezi asakukhudzeni inu. Ameni! Iye akhoza kusokosera ndi kumapanga phokoso. Ngakhale imfa imene siyingakukhudzeni inu, “O imfa, mbola yako ili kuti? Chigonjetso chako chiri kuti? Tikuthokoza Mulungu amene amatipatsa chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.”

153 Mapeto a ndime iyi, tiyeni tiiwerenge iyo:

*Ndipo potembenuka, ine ndinawona zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide;*

*Ndipo pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide monga. . . Mwana wa munthu, . . .*

154 Mai! Kodi inu munazindikira? Nyenyezi, zoyikapo kandulo, nyali. Kodi izo zikutanthauza chiyani? Kodi izi zikutanthauza chiyani? Kuti nyengo imene ife tikukhalemoyi ndi nthawi yausiku, makandulo ndi nyali ndi nyenyezi zimatanthauza usiku. Ndipo kodi nyenyezi imachita chiyani? Imanyezimiritsa kuwala kwa dzuwa mpaka dzuwa litabwerera. Lidalitsike Dzina la Ambuye! Ndipo mtumiki woona wa Mulungu samanyezimiritsa kuwala kothwanima kwina, tsinde lina lofanana, mankhusu ena akuyaka; iye amanyezimiritsa kuwala kwa golide kwa Khristu kwa Mpingo, kuti “Iye ali yemweyo, ndipo Iye ali moyo, ndipo Iye akuwala pa ine.” Ameni! Kumeneko ndiko Kuwala kumene iye amawonetsera. Nyenyezi imanyezimiritsa kuwala kwa dzuwa, mwawona, chotero ife tikunyezimiritsa Kuwala kwa Mwana wa Mulungu. Kumachita chinthu chomwe chomwecho chimene Iye ankachita, kupereka Kuwala. Kuwala kwa mtundu wanji? Kuwala kwa Uthenga kwa iwo.

155 Tsopano tiyeni timuwone Iye mopitirira pang’ono, pamene ife tikutenga ndime yonse ya 13:

*Ndipo pakati (pamenepo ndi pakati) pa zoyikapo nyali zagolide monga. . . Mwana wa munthu, atavekedwa chovala chofika kumapazi, ndipo atamangira lamba wagolide pachifuwa.*

156 Tsopano pa pali umboni wina wosonyeza kuti chiphunzitsa ichi ndi cholondola pokhala kuti ili ndi tsiku la Ambuye. Kodi inu munamuzindikira Iye? Iye sanali wansembe panthawiyi, komanso Iye sanali mfumu, Iye anali woweruza. Zindikirani, wansembe, wansembe wamkulu, pamene iye amalowa mmalo opatulika kapena kulowa kukatumikira, ku msonkhano, iye ankadzimangirira yekha mchiwuno. Kumanga lamba wake mchiwuno, zinkatanthauza kuti iye amatumikira; samamanga konse iyo pa phewa pake. Koma apa Iye akutulukira,

akutulukira akuyenda ndi lamba atamangidwa pamwamba, lamba pa phewa Lake; atamangira pa chifuwa, pachifuwa, ndi lamba wagolide, atamangira mmwamba. Ndi chiyani chimenecho? Woyimira mlandu, woweruza. Woweruza atavala lamba wake pa phewa, atadzimanga apa, osati mmusi ngati wansembe. Mwaona, izo zikuwonetsera kuti Iye sanali mu unsembe Wake tsopano, Yohane anapita njira yonse mpaka anakalowa mu tsiku la Ambuye ndipo anamuwona Iye akubwera ngati woweruza.

<sup>157</sup> Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ndi woweruza? Tiyeni tiwerenge Yohane Woyera 5:22, mofulumira, tiwona ngati Iye ali woweruza kapena ayi. Yohane Woyera 5:22:

*Pakuti Atate saweruza munthu aliyense, koma wapereka kuweruza konse kwa Mwana:*

<sup>158</sup> Nkulondola uko? Iye ndi woweruza, Woweruza Wapamwamba. Ndipo Yohane akuwonetsa kuti Iye sanali mu tsiku la uneneri Wake, ngati mneneri, komanso Iye sanali wodziwika mu masiku a ufumu Wake, koma Iye anali mu tsiku la Ambuye ngati Woweruza. Tsopano, ndi angati akudziwa kuti wansembe atakhala ndi lamba wake, chingwe chake mchiuno mwake chimatanthauza kuti anali akugwira ntchito? Aliyense amene amawerenga Zipangano, amene amadziwa Chipangano Chakale, amadziwa zimenezo. Pamene wansembe wamanga mchiuno mozungulira apa, iye amakhala mu utumiki, iye ndi wantchito. Koma Iye anali atadzimangira mmwamba umu, woweruza.

<sup>159</sup> Tiyeni tiwerenge patsogolo pang'ono:

*. . . lamba wagolide . . . anali . . . pa chifuwa . . .*

<sup>160</sup> Uko nkulondola, pamwamba kuzungulira *apa*, Iye anali Woweruza.

Tsopano ife tiwerenga ulemerero wofutukuka pasanu ndi pawiri wa Umunthu Wake. Oh, mai! Izi zimandipangitsa kuti ndifuule ndisanafike kwa izo. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Zindikirani! Oh, ichi ndi chinthu chodabwitsa chotero. Ingomvetserani:

*Ndi mutu Wake . . .*

<sup>161</sup> Tsopano penyani, Iye ndi zinthu zisanu ndi ziwiri, apa iye akutchula: mutu Wake, tsitsi Lake, maso Ake, mapazi Ake, Liwu Lake, zinthu zisanu ndi ziwiri zimene Iye akuzinena apa, ulemerero wofutukuka pasanu ndi pawiri wa Yesu Khristu. Ndiroleni ine ndiwerenge Izo:

*Mutu wake ndi tsitsi lake linali loyera ngati ubweya, woyera ngati chipale; . . . maso ake anali . . . a malawi a moto;*

*...mapazi ake ngati...mkuwa wabwino, ngati kuti wawotchedwa mu ng'anjo; ndipo mauu ake... mkokomo wa madzi ambiri.*

*Ndipo mu...Ndipo iye anali ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja lake lamanja: ndipo kuchokera mkamwa mwake mukutuluka lupanga lakuthwa konsekonse: ndipo nkhope yake inali ngati dzuwa likuwala mu mphamvu yake.*

162 Ndi masomphenya bwanji! Kodi iye anawona chiyani apa? Mwana wa Mulungu wa ulemerero, ndi chizindikiro. Tsopano, tiyeni—tiyeni tingokhala okonzeka tsopano.

163 Oh, mai, ndimagaliza kuti anali naini, ndi eyiti okha. Ine sindinayambebe. Chabwino. Zimenezo ndi zabwino. Tsopano, pepani abale awa ayimirira, zikundipangitsa ine wamanjenje kuwawona iwo ataimirira, inu mwaona, chifukwa ine ndikudziwa kuti miyendo yawo ikupweteka. Ngati ndikanangokhala ndi njira iliyonse abale, ya chirichonse chimene ndikanachita, ine ndithudi ndikanachichita icho. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu mumvetse ichi kwambiri. Ndipo muime kanthawi pang'ono ndipo Mulungu akupatseni mphotho kwambiri, ndiro pemphero langa.

164 Tsopano—tsopano zindikirani, chinthu choyamba, tsopano ife tikuzindikira, mutu Wake ndi tsitsi Lake zinali zoyera ngati ubweya. Mutu wake ndi tsitsi Lake zinali zoyera ngati ubweya. Tsopano, izo sizitanthauza kuti Iye anali wokalamba, amene anachita izi. Icho sichinali chifukwa chake. Iye sanali wokalamba kuti achite izi. Iye anali...Zinali chifukwa cha ukatswiri Wake ndi chomuyenereza ndi nzeru Zake. Chifukwa Iye ndi Wamuyaya, ndipo Wamuyaya sangakalambe. Inu mukumvetsa?

165 Tiyeni titsegule koyamba, ndipo ife ti—ifeyi timujambula Iye apa monga chonchi, ndipo tipeza chimene Iye ali. Tsopano, tiyeni titsegule ku Daniele 7:9, kwa miniti chabe, inu mukuwona chithunzi chomwe chomwecho mu Daniele pamene Iye akubwera ngati...kuno ku nthawi ya Amakedzana. Ndipo pafupifupi aliyense, wophunzira Baibulo, amadziwa bwino bwino kumene ife talunjika pakali pano. Daniele 7, ndi ndime ya 9; ine ndiyambira pa 8:

*Ndipo ine ndinapenyetsetsa nyanga, ndipo, taonani, pamenepo panabwera...nyanga ina yaying'ono, patsogolo—patsogolo pake panali zitatu za nyanga zoyambazi zinazulidwa ndi mizu yake: ndipo, taonani, mu nyanga iyi munali maso ngati...munthu, ndi pakamwa poyankhula zinthu zazikulu.*

*Ndipo ndinayang'ana mpaka mipando yachifumu itaponyedwa pansu,...*

166 Tsopano mvetserani. Mvetserani mwatcheru, tsopano. Kodi mukukhoza kundimva ine kumbuyoko bwino bwino? Nenani “Ameni,” ngati mungathe. Ine ndinamufunsa mkazi wanga kumbuyo uko. Ndikuganiza kuti choyankhulira ichi apa ndi... icho ndi chamoyo kwambiri apa, sichoncho? Tsopano, ine ndikufuula kwambiri, ndikuganiza, mu ichi.

167 Chabwino, tsopano Daniele 7:9:

*Ndipo ndinayang’ana mpaka mipando yachifumu inaponyedwa pansi, ndipo Wamakedzana anakhala pansi, amene zovala zake zinali zoyera ngati chipale, ndipo tsitsi la pamutu pake linali ngati... ubweya weniweni: (wamasiku Amakedzana.) mpando wake wachifumu unali ngati lawi lamoto, ndipo magudumu ake anali moto woyaka.*

*Ndi moto—mitsinje yamoto inaperekedwa ndi kutuluka pamaso pake: ndipo masauzande masauzande anatumikira kwa iye, ndi teni... kuchulukitsa ka teni sauzande anaima pamaso pake: ndipo chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabukhu anatsegulidwa.*

168 “Tsitsi loyera!” Zonse... aliyense amadziwa kuti amenewo ndi oweruza akale mmasiku akale. Monga oweruza achingerezi anakonda kuvala wigi yoyera. Ndi angati akukumbukira zimenezo? Oweruza akale ankavala wigi yoyera chifukwa anali... Ndipo apa Iye ali, kuwonetseranso kuti Yohane ali pa tsiku la Ambuye, iye anamuwona Iye ngati woweruza. Amen! Osati ngati wansembe, osati ngati mfumu, osati ngati mneneri, koma ngati woweruza. Atate (Ndi Yohane Woyera 5:22) anapereka chiweruzo chonse kwa Iye. Ndipo Iye ndi woweruza tsopano, wabwera kudzaweruza mafuko. Oh kwa tsiku limenelo pamene inu mudzamuwona Iye monga choncho! Tsitsi lake linali loyera ngati chipale, Daniele anamuwona Iye akubwera kwa wamasiku Amakedzana. Muwoneni Iye akulumikiza ziwiri izi pamodzi. Chabwino:

*...ndipo chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabukhu anatsegulidwa.*

*Ndipo ndinawona pamenepo chifukwa... Ndipo ndinawona pamenepo chifukwa cha liwu la aakulu—mawu aakulu amene nyanga... (Ayi, ndapeza malo olakwika, sichoncho ine?)*

169 Daniele 7:9, eya, ndi ife apa:

*...ndipo magudumu ake...*

*Ndipo mtsinje wamoto unatuluka pamenepo ndi kubwera... kuchokera... iye: ndipo makumi a masauzande anabwera ndipo anatumikira kwa iye,...*

*Ndipo ine ndinapenya pamenepo chifukwa cha liwu la mawu aakulu amene nyanga inayankhula:*



ndipo *ndinapenya ngakhale mpaka chirombocho chinaphedwa, ndipo thupi lake linali litawonongedwa, ndipo linaperekedwa ku—malawi oyaka.* (Uhm!)

*Zokhudza zirombo zinazo, izo zonse zinali ndi ulamuliro wawo utachotsedwapo: (ndizo mphamvu zonse za Amitundu ndi maufumu zidzagwa) komabe miyoyo yawo inatalikitsidwa kwa nyengo ndi nthawi.*

*Ndipo ine ndinawona mu masomphenya a usiku, ndipo, taonani, wina ngati Mwana wa munthu akubwera...mitambo ya kumwamba,...(Kodi ife tinamuwona Iye akubwera motani mmawa uno, mu ndime ya 3? Akubwera mmitambo ya kumwamba, Mwana wa munthu.) ...mmodzi wonga kwa Mwana wa munthu akubwera mmitambo ya kumwamba, ndipo iye anabwera kwa wamasiku Amakedzana, ndipo iwo anamubweretsa iye pafupi ndi iye.*

*Ndipo kunaperekedwa kwa iye ulamuliro, ndi ulemenero, ndi ufumu, ndi anthu onse, ndi mafuko, . . . zinenero, zimutumikire iye: ulamuliro uwu ndi ulamuliro wosatha, umene sudzatha, ndipo ufumu wake udza. . .ufumu wake sudzawonongedwa.*

<sup>170</sup> Anabwera kwa wamasiku Amakedzana amene tsitsi lake linali loyera ngati ubweya. Ndipo Yohane anatembenuka ndipo anamuwona wina ngati Mwana wa munthu atayima pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide, ndi tsitsi loyera ngati chipale, Woweruza! Osadzimanga mchiuno, koma atadzimanga mozungulira pachifuwa, pamwamba apa, woweruza! Ndi lamba wa woweruza paphewa Pake, Iye anayima ndi wa golide, wangwiro, woyera, woyengeka, lamba amene anagwira chirungamo Chake. Chophimba chake! Iye anaphimbidwa paliponse mpaka ku mapazi. Penyani mawonekedwe ofutukuka pasanu ndi pawiri a umunthu Wake ndi ulemelero.

<sup>171</sup> Tsopano, ine ndikukhulupirira, ndime ya 14:

*Tsitsi Lake. . .Mutu wake ndi tsitsi lake zinali zoyera ngati ubweya, zoyera ngati chipale; ndipo maso ake anali. . .malawi a moto;*

<sup>172</sup> Mutu, tsitsi; “maso ake anali ngati malawi a moto.” Taganizani za zimenezo! Maso amenewo amene kale anaphimbidwa ndi misozi yaumunthu, tsopano asanduka malawi a moto. Mu mkwiyo Iye wayima pamenepo ngati woweruza wokwiya. Nchifukwa chiyani inu munamukana Iye? Oh, wochimwa, taganizani za zimenezi! Taganizani za zimenezi, membala wofunda wa mpingo! Taganizani za zimenezi, Katolika, Baptisti, Presbateria, Pentekoste! Taganizani za zimenezi, Akatolika! Namwali wanu Maria anayenera kupita mpaka pa pentekoste ndi kukalandira Mzimu Woyera, ndi kudzandima ndi kumachita ngati mkazi woledzera. Amake

kumene a Khristu ankayenera kupeza zimenezo asanalowedwe kupita Kumwamba. Kodi akazi inu mudzapita bwanji kumeneko mochepera mulimonse kuposa pamenepo? Taganizani za zimenezo, amuna, aliyense wa inu!

<sup>173</sup> Tsitsi lake, ndi maso ake nthawi ina anachita khungu ndi misozi ya umunthu, komabe ine ndikufuna kuti inu muwone chinachake chokhudza maso amenewo. Pamene Iye anali akadali pa dziko lapansi, iwo anachita mdima ndi misozi ngati munthu, pakuti Iye anafuula pa manda a Lazaro. Kulondola! Atadzaza ndi chifundo; umunthu Wake. Iye anavekedwa, Iye anali Mulungu atavekedwa mu umunthu, kuti adzachotse tchimo. Komabe kumbuyo kwa umunthu umenewo, Iye anali ndi chinachake kumbuyo Kwake chimene chinkakhoza kuyang’ana pansu mu mtima wa munthu ndi kudziwa zonse za iye. Bwanji? Panali chinachake kumbuyo Kwake, komabe Iye anali atavala mnofu wachivundi.

<sup>174</sup> Koma iwo sanadziwe kuti anali ndani. “Ngati inu simukukhulupirira,” Iye anati, “kuti Ine ndi Iye, inu mudzafa mmachimo anu.” Uko nkulondola. “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine; koma ngati Ine ndikuchita ntchito za Atate Wanga, ndiye mukhulupirire ntchito ngati simukundikhulupirira Ine.” Oh, momwe Iye ankayesetsera kufikitsa Uthenga kwa iwo, vumbulutso! Amakhoza kuyang’ana pansu mu mtima wa munthu, nkudziwa zonse za iye. Momwe ine ndimaganizira za zimenezo! Maso amenewo amene nthawi ina anapyoza kudutsa mapiri, anayang’ana pa nkhope ya mazunzo, ndipo amakhoza kulira ngati munthu, komabe amakhoza kutenga Mzimu wa Mulungu kuseri kwa masomphenya a umunthu kumeneko ndi kupenya zinthu zonse; zinthu zimene zinali, zinthu zimenezo zimene zinalipo—zinalipo, ndi zinthu zimene zinkabwera. Kuneneratu chimaliziro kuyambira pachiyambi, ndicho chifukwa chakuti Mulungu anali kumbuyo kwa maso a umunthu amenewo. Lolani Mulungu alowe mmoyo wanu ndi kukulamulirani inu, ndipo Iye adzakuwonetsani inu zinthu zimene zikubwera. Pakuti simukhalanso inu pamenepo, ndi Mzimu Woyera mmoyo wanu kumbuyo uko ukuyang’ana kudutsira maso achivundi awo kuti atenge zinthu.

<sup>175</sup> Oh, ulemelero kwa Mulungu! “Ine ndizatsanulira cha Mzimu Wanga pa thupi lonse, ndipo ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera, anyamata anu adzawona masomphenya, akulu anu adzalota maloto.” Aleluya! Nthawizina Iye amayenera kuti akugonetseni inu kuti Iye akhoze kuyang’ana kudzera mwa inu, koma ndithudi Iye adzakuwonetsani inu nthawi zambiri. “Anyamata anu adzawona masomphenya, akulu anu adzalota maloto; pa adzakazi Anga ndi antchito aakazi ndidzatsanulira Mzimu Wanga.” Osati, “Pa madikoni Anga ndi azibusa, ndi pa Anga. . .” “Pa aliyense amene angafune, pa thupi lililonse,

Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga.” Inu mukudabwa chifukwa chimene ndimafuulira izi, koma izo zikubwera mu mibadwo ya mpingo iyi.

<sup>176</sup> Oh, apo Iye anali, maso amenewo. Ndipo, kumbukirani, tsiku lina, maso amenewo amene anaphimbidwa misonzi, maso amenewo adzaima pa chiweruzo. Tsopano iwo ali ngati malawi amoto akuthamanga uku ndi uko kudutsa padziko lonse lapansi, ndipo palibe chimene chimachitika kupatula chimene Iye akudziwa. Oh, mai, zinalembedwa. Kuthamanga uku ndi uko pa dziko lapansi kumawona mayendedwe aliwonse, kumazindikira lingaliro lirilonse, kudziwa chirichonse chimene mukuchita, zolinga za mtima, chimene mukufuna kuchita. Iye amadziwa zonse za izo. Iye amadziwa ngati inu mumamukonda Iye. Iye amadziwa ngati zolinga zanu ziri zolondola, kuti muzimutumikira Iye. Iye amadziwa zonse za izo. Ndipo zidzakhala bwanji inu mukadzaima tsiku limenelo pamene tchimo lirilonse lidzakhale powonekera pamaso pa Iye, ndipo Iye akuyima pamenepo pa Mpandowachifumu Woyera wa Chiweruzo?

<sup>177</sup> Mulungu, ndipulumutseni ine kumalo amenewo! Sindikufuna kuti ndidzawone zimenezo. Pamene Mulungu wokwiya adzatulukira kumeneko ndi moto ukuthwanima mmaso Kwake, ndi chirungamo, tsitsi loyera pamutu Pake monga choncho, ndi maso Ake akuthwanima ndi moto amene amadziwa malingaliro aliwonse a mtima wanu, ndi chirichonse chimene munkafuna kuchita. Ndibiseni ine mu Thanthwe la Mibadwo long’ambikira ine! Munthu wachikulireyo anakonda kuyimba, “Pamene dziko lapansi likuyaka moto, mudzaima pambali panga. Mudzaima pafupi ndi ine, ndipo mulole chifuwa Chanu chikhale mtsamiro wanga. Mundibise ine umo mu Thanthwe la Mibadwo.” Mulungu, ine sindikufuna chiweruzo Chanu. Ine sindikufuna Wanu. . . Chimene ine ndikufuna ndi chifundo Chanu, Ambuye. Ndipatseni ine chifundo Chanu, osati chirungamo Chanu. Mungondipatsa ine chifundo Chanu. Osati malamulo Anu, osati chirichonse. . . Mungondipatsa ine chifundo, Ambuye, ndizo zonse zimene ndingathe kuchonderera. Palibe chirichonse mmanja mwanga chimene ndikubweretsa (sindine wabwino, palibe mbiri), kokha pamtanda Wanu ndikumamatira. Ambuye, ndizo zonse zimene ine ndikuzidziwa: Wina anabwera kudzatenga malo anga.

<sup>178</sup> Onani mawonekedwe Ake ofutukuka pasanu ndi pawiri tsopano a munthu Wake, ndipo muwona icho chimene Iye anachita.

*Mutu wake. . . unali woyera ngati chipale; ngati ubweya, tsitsi loyera; ndipo maso ake anali ngati. . . (tiyeni tiwone). . . Mutu wake. . . unali woyera ngati. . . chipale; ndipo maso ake anali. . . malawi a moto;*

*Ndipo mapazi ake anali ngati . . . mkuwa woyengeka,  
monga wowotchedwa mu ng'anjo;*

<sup>179</sup> Penyani tsopano. Ife tangozindikira kumene pamene Iye anaphimbidwa, inu mukudziwa. Tsopano penyani. Mutu Wake, maso Ake, tsopano Iye akutsikira kumapazi Ake ngati mkuwa. Penyani kusiyana kwa chithunzi chimene Yohane anawona cha Yesu, ndi chimene Daniele anawona cha ufumu wa padziko lapansi, mutu wagolide ndi zina zotero.

<sup>180</sup> Tayang'anani pa chimene ichi chinali apa, kuyima pamenepo, mkuwa. Kodi mkuwa umayankhula chiyani? Mkuwa umayankhula za chiweruzo, chiweruzo Chaumulungu. Zimawonetsera kuti cholinga Chake chonse chikubwera pa dziko lapansi pano ngati Mulungu, kuti adzapangidwe kukhala thupi, ndipo Iye anatifera ife ndipo anatenga ziweruzo za Mulungu, chiweruzo Chaumulungu, ndipo walandira Ufumu umene uli mkuwa, ndipo wolimba, ndipo sungathe kusunthidwa. Palibe cholimba kuposa mkuwa, ndipo sanapeze kanthu kalikonse kamene kangasinthe izo.

<sup>181</sup> Chiweruzo! Mkuwa umayankhula za chiweruzo Chaumulungu chimene chaperekedwa. Tayang'anani pa njoka yamkuwa mchipululu. Kodi njoka ya mkuwa ija inkaimira chiyani? Njokayo inkaimira tchimo; koma, pokhala mkuwa, chiweruzo chinadutsa kale pa tchimo.

<sup>182</sup> Tsopano, zindikirani komanso masiku a Eliya, pamene iwo anali atamukana Eliya ngati mneneri, ulusi wawung'ono umenewo, m'badwo wa mpingo wa amakedzana. Limodzi la masiku awa ndidzabweretsapo ndi kukuwonetsani inu kuti Israeli anali ndi mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, nawonso, ndipo inayimirira ndendende ndi iyi. Ndipo mu m'badwo wa mpingo wawo, mu masiku a Eliya, iwo anamukana iye ndipo panali zaka zitatu ndi miyezi sikisi kunalibe mvula. Ndipo mneneri wamakedzana ananena kuti "mu mlengalenga munawoneka ngati mkuwa," Chiweruzo cha Umulungu pa mafuko chifukwa chokana Mulungu ndi kumumvera Yezabeli.

<sup>183</sup> Mkuwa umaimiranso chiweruzo Chauzimu pa guwa pamene nsembeyo inkaphedwa, guwa la mkuwa, inkaphedwa. Maziko kumene anali a mkuwa, chiweruzo. Iye anaponda mponderamo mphesa mwaukali wa Mulungu ndipo anatenga chiweruzo chathu pa Iye. Tsegulani Chivumbulutso 19:15, miniti chabe, tiyeni tiwone chimene Iye anachita. Chibvumbulutso 19:15, tiyeni tiwerenge kamphindi chabe ngati ndingayipeze. Eya, tiyeni tiyambire ndi . . . tiyeni tiwone, pafupifupi ndime ya 12:

*Maso ake anali . . . malawi a moto, ndipo pamutu pake panali korona, akorona ambiri; ndipo iye anali ndi dzina litalembedwa, limene palibe munthu aliyense ankalidziwa, koma . . . iyemwini.*

*Ndipo iye anavekedwa ndi chovala choviikidwa mmagazi: ndipo dzina lake linkatchedwa Mawu a Mulungu. (Tsopano, kumbukirani, Dzina Lake silinali Mawu a Mulungu, Dzina Lake linkatchedwa chomwecho. Mukuona?)...dzina lake linkatchedwa Mawu a Mulungu.*

*Ndipo magulu ankhondo...a kumwamba...magulu ankhondo amene anali kumwamba anamutsatira iye atakwera akavalo oyera, atavekedwa mu nsalu yabafuta, yoyera ndi yaukhondo.*

*Ndipo kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa, kuti ndi ilo iye akanthe nalo fuko: ndipo iye adzawalamulira iwo ndi ndodo ya chitsulo: ndipo iye adzayenda... (Ndi chiyani chimenecho?)... kuyenda mopondera mphesa mwa ukali wa mkwiyo wa Mulungu Wamphamvuzonse.*

184 Kodi Iye anachita chiyani? Mkwiyu wa Mulungu unali pa ife chifukwa chokhala ochimwa. Nkulondola uko? Palibe amene akanakhoza kudzipulumutsa yekha. Palibe chimene ife tikanakhoza kuchita, ndife tonse “Obadwira mu tchimo, okulira mu kusaeruzika, obwera pa dziko lapansi tikuyankhula mabodza.” Ndipo kodi Iye anachita chiyani? Anabwera pa dziko lapansi, Aleluya, ndipo anadzayenda moponderamo mphesa! Mkwiyu wonse wa Mulungu Wamphamvuzonse unatsanuliridwa pa Iye. “Ndinu woyenera, O Mwanawankhosa wa Mulungu, chifukwa Inu munaphedwa.” Kutengera machimo adziko lapansi pa Iye, ndipo Iye ananyamula machimo athu, kuti Mulungu anatsanulira ukali wamkwiyu Wake pa Iye. “Ndipo Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Palibe munthu amene anafa ngati Munthu ameneyo! Iye anavutika mpaka magazi ndi madzi zinalekanitsidwa mu thupi Lake. Ndipo madontho a magazi anatuluka pa mphumi Pake Iye asanamwalire.

*...moponderamo mphesa wa...mkwiyo...wa ukali...wa Mulungu Wamphamvuzonse.*

185 Tsiku lina mapazi amkuwa amenewo achilungamo (Ulemelero!), pamene Iye adzabwera ngati woweruza, Iye adzayenda wotsutsakhristu, ndi adani Ake onse. Aleluya! Iye adzayenda pa dziko lapansi ndi ndodo ya chitsulo mdzanja Lake. Amen! Oh, lapa, mzanga wochimwa, pamene iwe uli nawo mwayi wolapa. Muyesere, kuzichotsa zimenezo ndi kuganiza kuti iyo ndi nkhani yaying’ono imene singachitike. Izo zidzachitika! “Izo sizingachitike kwa ine.” Izo zidzachitika kwa inu!

<sup>186</sup> Mapazi a mkuwa, anaponda adani Ake. Chifukwa Iye anazunzika ndi kuponda moponderamo mphesa mwaukali wa Mulungu kuti alipire machimo athu. Ndipo kenako ife, olakwa, osauka, mphutsi zomvetsa chisoni monga ife tiriri, timadzutsa mphuno zathu zazing'ono mmwamba ndi kumawerenga mtundu wina wa bukhu losakhulupirira Mulungu ndi kumayesera kuganiza kuti “kulibeko Mulungu,” ndi kuti “palibe chinthu chonga *ichi*, ndipo chiweruzo sichingabwere.” Iye adzatenga mapazi amkuwa amenewo ndi kuphwanja mdani Wake. Iye adzagonjetsa wotsutsakhristu. Iye adzaitenga mipingo ya chinyengo imeneyo ndipo adzaiponyera iyo mu Muyaya kutali, kwinakwake mpaka kumoto wonyeketsa kumene iye adzawonongedwe ndi kuthedwa. Ndipo Iye adzalamulira pa dziko lapansi, Iye ndi Mpingo Wake kwa nthawizonse. Ulemelero!

<sup>187</sup> “Mutu, woyera ngati ubweya,” chirungamo, ukatswiri, kudziwa kuyankhula, wokwanira, nzeru. Wakale, woyera, amayankhula za nzeru, wokalamba. Akudziwa chimene Iye akuchita. Iye ndi—Iye ndi Kasupe wa nzeru. Iye ndi Kasupe wa kudziwa zinthu. Iye ndiye Kasupe wa chinthu chabwino chirichonse, chotero Iye akuimiridwa mwa ichi ngati Mwana wa munthu, anali atavala tsitsi loyera ili likulendewera pansi. Daniele anamuwona Iye zaka handiredi zambiri, zaka seveni handiredi, ndipo anati, “Iye anali Wamasiku Amakedzana. Ndipo mmodzi wonga Mwana wa munthu anabwera mu mphamvu ndipo analumikizana ndi Wamasiku Amakedzana uyu, ndipo chiweruzo chinakhazikitsidwa.”

<sup>188</sup> Tsopano ine ndikungofuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Ine ndikuyankhula ndi inu mpingo wofunda. Anamwali khumi anatuluka kuti akakumane ndi Ambuye, asanu a iwo anali anzeru, asanu opusa; monga ife tinazitengera mmawa muja, mtengo womedzanitsidwa. Tsopano, kumbukirani, pamene iwo ankapita kukakumana ndi Mulungu... Tsopano penyani, Baibulo linati, “Mabukhu anatssegulidwa.” Daniele 7:9, “Mabukhu anatssegulidwa.” Limenelo ndi bukhu la wochimwa. “Ndipo bukhu lina linatssegulidwa.” Nndani anabwera ndi Iye? Mpingo kuchokera mu Mkwatulo. Oh! “Mateni a masauzande kuchulukitsa masauzande kuchulukitsa masauzande a masauzande anabwera ndi Iye ndipo anatomikira kwa Iye,” Mkazi wake, Mkwatibwi. Oh, ulemelero! Mkazi wake anabwera ndi Iye, Mpingo.

<sup>189</sup> Chiweruzo chinakhazikitsidwa, ndipo mabukhu anatssegulidwa. Ndipo bukhu lina linatssegulidwa, amene anali namwali wogona, ndipo munthu aliyense anaweruzidwa chomwecho kuchokera mu bukhu. Inu mudzafunsi kuti mupereke chifukwa chimene inu simunatero, ndipo kenako ndi chiyani pamenepo? Inu mukudziwa bwino tsopano, inu mukudziwa bwino. Inu mwina simunadziwe Izo mmbuyomo,

koma inu mukudziwa tsopano. Mukuona? Pamene ngati wolungama uyu adzapulumuka movutikira, wochimwa uja ndi wopanda umulungu uja adzawonekera pati? Iye amene amakana, amadziwa bwinoko ndipo kenako amakana Iwo. Kodi iwo adzawonekera kuti? Mapazi Ake ngati mkuwa, chiweruzo Chaumulungu.

<sup>190</sup> Tsopano, tiyeni tiwone, titero posakhalitsapa...mpaka kumapeto kwa tsamba tsopano:

...tsitsi *longa ubweya*,...*ndipo maso ake anali*...  
malawi *a moto*;

*Ndipo mapazi ake ngati—mapazi ngati*...*mkuwa*,...  
*kuwochedwa mu ng'ango*; *ndipo liwu lake*...*mkokomo wa madzi ambiri*.

<sup>191</sup> “Liwu la madzi ambiri.” Kodi *madzi* amaimira chiyani? Ngati mukufuna kuti mulembe izo, tsegulani Chivumbulutso 17:15, ndipo mupeza kuti Baibulo linati, “Madzi amene iwe uwawona ndi makulidwe, ndi unyinji, ndi anthu, ndi malirime.”

Chabwino, *Liwu*. Ndi chinthu choyipa bwanji kwa moyo umene ukutitimira pa nyanja ya moyo, wopanda woyendetsa woti amutsogolere iye, wopanda pogwira, akuyandama ndi mafunde, kuti amve mkokomo wa mathithi aakulu, kusesereka kwa madzi! Ndi chinthu choyipa bwanji kwa moyo umene ukutitimira! “Liwu la madzi ambiri.” *Liwu Lake* ndi chiyani? Ndi chiweruzo, liwu la azitumiki, kudutsa Mzimu Woyera, amene amafuulira kwa anthu mu m’badwo uliwonse, atayima pamenepo, Liwu la madzi ambiri linali kufuula, kukandapala kwake ndi unyinji, Liwu la nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimenezo mu dzanja Lake, kwa m’badwo wa mpingo uliwonse, kulalikira ubatizo wa Mzimu Woyera, ubatizo mu Dzina la Yesu, kuyankhula mu malirime, mphamvu ya Mulungu, kuwuka kwa Khristu, Kudza Kwachiwiri, Chiweruzo Chauzimu. Liwu la madzi ambiri linatuluka mwa uyu amene amawoneka ngati Mwana wa munthu, madzi ambiri.

<sup>192</sup> Chimene chiti chidzakhale kudziwa kuti inu munakhala mu msonkhano ndipo munamva kuti muyenera kukhala bwino ndi Mulungu ndi kulandira Mzimu Woyera, ndi moyo wotitimira kuti mukamve liwu limenelo likuyankhula mu msonkhano umene inu munakhalamo, ndipo munamva ziweruzo za Mulungu zikulalikiidwa, ndipo nkuzikana Izo. Mathithi aakulu ali pansu panu pomwe, matsitso aakulu amene adzakutengerani inu ku chiwonongeko Chamuyaya.

<sup>193</sup> Liwu la madzi ambiri, munthu wachinayi wa Iye. Liwu la madzi ambiri. Kodi inu mudzachita motani zimenezo pamene izo zalembedwa mu Ulemelero, pamene liwu usikuuno lajambulidwa? Liwu lanu lajambulidwa. Malingaliro anu ajambulidwa. “Monga momwe munthu amaganizira mu mtima mwake, chomwechonso iye ali.” Zindikirani, liwu

lanu limamveka mokweza Kumwamba kuposa lanu...Ine ndikutanthauza, malingaliro anu amafuula Kumwamba kuposa momwe mawu anu amamvekera padziko lapansi. Ndithudi, ndi chomwecho. Mulungu amadziwa malingaliro ndi zolinga za mtima, Iye amadziwa zonse za izo.

<sup>194</sup> Iye anati kwa Afarisi, “Onyenga inu, mungayankhule bwanji zinthu zabwino, pamene mu kuchuluka kwa mtima kamwa limayankhula? Kumanditcha Ine, ‘Mphunzitsi, wabwino,’ ndipo Ine ndikudziwa, Ine ndikutha kuyang’ana kudutsa mwa inu ndi kuwona kuti ndinu onyenga. Inu simukutanthauza zimenezo.”

<sup>195</sup> Oh, izo zidzakhala chiyani pa tsiku limenelo pamene Liwu limenelo lidzamveka likubangula kuchokera mmadzi ambiri, mibadwo yambiri ya mpingo ikupangidwapo?

<sup>196</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu chinachakenso. Ndiroleni ine ndinene chinachake kwa anthu inu amene mwapulumsidwa, ndiroleni ine ndinene ichi kwa inu.

<sup>197</sup> Tsopano, iwe solo yotitimira, iwe wotitimira wosauka amene ukusesereka kupita ku mathithi aakulu amenewo, samala. Ichu chidzakhala chinthu chowopsya mukadzadziwa kuti palibe kupulumuka kwa inu pamenepo. Inu simungathe kupulumutsidwa ndiye, inu mudzadziwa kuti chiwonongeko chanu chiri patsogolo panu. Pamene inu mudzadziwa kuti mkati mwa mphindi pang’ono inu mudzamva Liwu limenelo likuyankhula, “Chokani kwa Ine, inu akuchita kusaweruzika, kulowa mu moto wosatha wokonzedwera mdierekezi ndi angelo ake.” Mudzadziwa pamene mudzamva kubangula kwa mathithi aakulu amenewo a maliwu amenewo a misonkhano ija, pamene inu mukudutsa izi. Oh, ndi chinthu chowopsya bwanji, ndi maloto oyipa bwanji! Musalole kuti izo zidzachitike kwa inu, anthu. Lapani, khalani pa ubale ndi Mulungu tsopano, pamene inu mungathe kukonza.

<sup>198</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu chinachakenso. Nchiyani chiri chokoma kwa munthu amene wazikika, atagona pansu pa mtengo wobiriwira nthawizonse, kuti amve mtsinje wamafunde? Oh! Ndiwo Mpingo umene ukukhala mmalo amwambamwamba ndi Liwu la Mulungu likuwomba mafunde mokoma ndipo nkumayankhulana nawo pamenepo. Mukuona chimene ichu chiri? Ichu ndi chitsutso kwa wochimwa, ndi mdalitso kwa wopulumutsidwa. Munthu amene wamangirira boti lake pa Thanthwe Khristu Yesu, ndipo amangogona ndi kumamvetsera, momwe iye angapumire! Lowani mu mpumulo umenewo.

<sup>199</sup> Momwe ine ndimakondera kufika kumene madzi akuyenda. Ngati ife tipita kokawedza kapena chirichonse, ine kawirikawiri ndimayesetsa kuti ndizipezere malo kumene madzi akuchita mafunde, chifukwa izo zimangokupangitsa iwe kuti uzipuma. Iwe umangowamva iwo akuyankhula usiku wonse. Oh, mai!



200 Kodi zimenezo si zokongola pamene iwe ungazike kwenikweni moyo wako mwa Khristu, pamalo oterowo mpaka utha kukhala chete pamaso pa Iye? Ndi kumva Liwu Lake likuyankhula kwa iwe, “Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiza iwe. Ine ndine Ambuye amene ndimakupatsa iwe Moyo Wamuyaya. Ine ndimakukonda iwe. Ine ndinakudziwa iwe maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ine ndinalembe dzina lako pa Bukhu, iwe ndi Wangu. Usawope ayi, ndi Ineyo. Usachite mantha, Ine ndiri ndi iwe.” Kenako ndimayimba:

Ndazika solo yanga mu mpumulo wa moyo,  
Sindidzayendanso pa nyanja zamkuntho;  
Namondwe angawopsyeze molusa kusesa  
molusa, mkuntho wakuya;  
Koma mwa Yesu ndine wotetezeka nthawi  
zonse.

201 Kumbukirani, Liwu limene limayankhula mokoma kwa inu, lidzamutsutsa wochimwayo. Chigumula chomwecho chimene chinapulumsa Nowa, chinamuwononga wochimwa. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? “Liwu la madzi ambiri.”

202 Penyani tsopano, “Tsitsi ngati ubweya, ndi maso ngati malawi a moto, mapazi ngati mkuwa, ndi Liwu la madzi ambiri.”

*Ndipo iye anali nazo mu dzanja lake lamanja nyenyezi zisanu ndi ziwiri: . . .*

203 “Nyenyezi zisanu ndi ziwiri.” Tsopano tiyeni titenge ndime ya 20 apa:

*Ndipo chinsinsi cha nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene unaziwona ku dzanja langa lamanja, ndi zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Nyenyezi zisanu ndi ziwirizo ndi angelo asanu ndi awiri (kapena atumiki asanu ndi awiri, atumiki asanu ndi awiri) a mipingo isanu ndi iwiri: ndipo zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zimene iwe ukuziona ndi mipingo isanu ndi iwiri.*

204 Iye akumumasulira iye kuti akhale otsimikiza kuti palibe cholakwika. Mngelo mu m’badwo uliwonse wa mpingo. Oh, izo zikhala zokongola, sabata ino, pamene ife tizibwerera mmbuyo mu mbiriyakale ndi kukatenga angelo amenewo ndi kuwona utumiki kumene umene iwo anali nawo. Iwo anali ndi utumiki wofanana. Ndendende chimodzimidzi kudutsa mu m’badwo mu Mpingo wawung’ono umenewo.

205 Nthawi ina mmbuyomu, winawake anati, “Inu mukudziwa, mpingo wa Katolika, pali kunena kwabwino, kwakuti, ‘Ndi mpingo weniweni chifukwa iwo unakhala ulipo kudutsa mibadwo.’”

206 Ine ndinati, “Zimenezo si chinsisi, pamene iwo unali ndi boma lonse ndi zina zonse kumbuyo kwake, ndi momwe iwo

unayimira ndi kugwedezeke ndi namondwe. Koma chinsinsi kwa ine ndi momwe apang'ono awo, ochepetsetsa kwambiri amatha kupaza namondweyo, amene amadulidwa pakati, ndipo amaponyedwa kwa mikango, ndipo amaikidwa pa zikuku, ndi kumadyedwa, ndi kuwotchedwa, ndi mkango... ndipo amaphedwa ndi china chirichonse, ndi momwe iwo anapululumukira zimenezo." Izo zimasonyeza kuti dzanja la Mulungu linali ndi iwo. Ndi zimenezotu. Ndipo mpaka lero Kuwala kwake kukuyakabe. Amen! Inde, bwana!

207 Tsopano, "Nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene zinali mdzanja Langa lamanja." Iye anali ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri mdzanja Lake lamanja, zimene zikutanthauza atumiki asanu ndi awiri a mibadwo isanu ndi iwiri. Oh, izo ndi—izo ndi zokongola. Momwe ife tibwerere mmbuyo ndi kukatenga—mtumiki amene anabweretsa Uthenga ku mpingo wa ku Efeso. Ndi mtumiki amene anabweretsa Uthenga ndi kugwiritsitsa ndi Iwo mpaka imfa, mpaka ku mpingo wa Smurna, ndi kwa mpingo wa Pergamo, Tiyatira, ndipo kumapitirira mpaka mmusi kudutsa m'badwo, ngakhale mpaka mu m'badwo uno tsopano. Atumiki amene ankasunga ndi kubweretsa Kuwalako, ndi kukugwiritsitsa Iko mofanana ndi apachiyambi kumayambiriro, ndipo amabweretsa Kuwala kudzera mwa iye.

208 "Iye anawagwirizira iwo mdzanja Lake lamanja." Taganizani! Dzanja lamanja kwenikweni sizimatanthauza monga Khristu wakhala kudzanja lamanja la Mulungu. Izo sizitanthauza kuti Mulungu ali ndi dzanja lamanja, chifukwa Mulungu ndi Mzimu. Koma Khristu anali dzanja lamanja la mphamvu. Munthu wanu wa dzanja lamanja, mzako—mzako woyima pafupi nawe, wapafupi kwambiri ndi iwe.

209 Ndipo, kumbukirani, nyenyezi zisanu ndi ziwiri zinali mdzanja Lake lamanja. Tangoganizirani, iwo anali kukoka mphamvu zawo, Kuwala kwawo kuchokera kwa Iye. Iwo anali kwathunthu pansu pa ulamuliro Wake, mu dzanja Lake lamanja. Oh! Mtumiki woota aliyense wa Mulungu amakhala chimodzimodzi. Anagwiritsitsa... Ndani angawapweteke iwo? Ndani angawapweteke iwo? Monga mmodzi wa angelo anafuulira kumbuyo uko pachiyambi. Kumbukirani *mngelo* amatanthauza "wamthenga." Ife tilowa mu zinthu zakuya zimenezo kumapeto kwa sabatayi. *Mngelo* amatanthauza "wamthenga." Ndipo iye anati, "Nchiyani chingatilekanitse ife ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu? Kodi ndi matenda? Kodi ndi zowopsa? Kodi ndi usiwa? Kodi ndi lupanga? Kodi ndi Imfa? Ine ndakhutitsidwa" anatero Paulo, "kuti palibe chirichonse chingatilekanitse ife ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu," pakuti ife tiri odzipereka kwathunthu ku dzanja Lake lamanja.

210 Winawake akuti, "Oyera-odzigudubuza! Oyera-odzigudubuza!" Zimenezo sizimawasokoneza iwo mpang'ono

pomwe. “Ndinu otentheka achipembedzo!” Iwo samazimva izo nkomwe. Iwo ndi odzipereka kwathunthu ndipo amakoka Moyo wawo kuchokera ku dzanja Lake lamanja la mphamvu, akunyezimiritsa Kuwala Kwake mofatsa, ndi kukoma mtima, ndi kudekha, ndi chipiriro; zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi zozizwitsa. Mulole dziko lidzitze Izo “ufiti,” chirichonse chimene iwo akufuna, sizitipanga ife kusiyana kulikonse, chifukwa tikudziwa kuti ndife ogonjera ndipo tiri mdzanja Lake lamanja. Kodi zimenezo si zodabwitsa? Mai!

<sup>211</sup> Tsopano tiyeni tifulumire, chifukwa sitikufuna kuti tikutopetseni inu. “Mdzanja Lake lamanja, nyenyezi zisanu ndi ziwiri.”

<sup>212</sup> Tsopano chiwonetsero chachisanu ndi chiwiri ndi chomaliza cha umunthu Wake:

*...ndipo kuchokera mkamwa mwake munatuluka  
lupanga lakuthwa konsekonse:...*

Ine ndimatanthauza, kuti ndicho chachisanu ndi chimodzi.

*...kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga  
lakuthwa konsekonse:...*

<sup>213</sup> Tsopano, Liwu la madzi ambiri, ndipo kutuluka kuchokera mkamwa Mwake...Mdzanja Lake lamanja Iye anali ndi nyenyezi.

*...ndi kuchokera mkamwa mwake munatuluka  
lupanga lakuthwa konsekonse:...*

<sup>214</sup> Tsopano, kodi inu mukudziwa chimene lupanga lakuthwa konsekonse la Baibulo liri? Tiyeni tingochigwira icho kuti inu mudziwe. Tengani Ahebri 4:2, mungobwerera mmbuyo pomwepo tsamba limodzi kapena awiri ndipo mupeza iyo, mwaona. Ahebri ali kumbuyo chabe kwa Chivumbulutso apa; Yuda, ndipo kenako Ahebri. Tsopano, mvetserani izo mwatcheru tsopano. Kapena...Ahebri, mutu wa 4 wa Ahebri, apa ife tiri. Chabwino, Ahebri mutu wa 4 ndi ndime ya 12:

*Pakuti mawu a Mulungu ndi achangu, ndi amphamvu kwambiri, ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, opyoza ngakhale kugawaniza pakati kwa moyo ndi mzimu, ndi molumikizana ndi mafuta a mmafupa, ndipo ndi ozindikira za maganizo ndi zamkati mwa mtima.*

<sup>215</sup> Ndiyeno iwo amakutcha iwe “wowerenga maganizo.” Ndi Mawu a Mulungu akuwonetseredwa mu Mpingo Wake! Akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse lililonse. Mmati, ndinangopezeka ndikuganizira za chinachake pamenepo. Ine sindikudziwa ngati ndinalemba Malem...Pezani Chivumbulutso 19, miniti chabe. Tiyeni titenge izi kenanso, ine ndikuganiza kuti nzoona. Ndine mwinamwake... Chivumbulutso 19, pafupifupi 11:

*Ndipo ndinawona mmiyamba mutatseguka, ndipo tawonani kavalo woyera;... (Apa pakubwera woyeranso, chiweruzo.) ... ndipo iye amene anakhala pamenepo ankatchedwa Wokhulupirika ndi Woono, ndipo mu chilungamo iye amachita... kuweruza ndi kuchita nkhondo. (Inu mukudziwa yemwe iye anali, si choncho? Chabwino.)*

*Maso ake anali... malawi a moto, ... (Iye anali Ndani?) ... ndipo pamutu pake panali... akorona; ... (Uh-oh. Iye anabwera kale mu ufumu tsopano.) ... ndipo iye anali... ndipo—ndipo iye anali ndi dzina litalembedwa, limene munthu aliyense sankalidziwa, koma... iyemwini.*

*Ndipo iye anali atavala chovala choviikidwa mu magazi: ndipo dzina lake limatchedwa Mawu a Mulungu.*

216 Nchiyani chinatuluka kuchokera mkamwa Mwake? Chinapita nchiyani? Wokwera pa kavalo woyera. Ndipo Chivumbulutso, aponso, 7, pamene... Ine ndikukhulupirira 8. Pamene kavalo woyera... ayi, ndi 6. Pamene wokwera pa kavalo woyera anatuluka, Iye anapatsidwa—uta, kuti agonjetsa ndi kugonjetsa.

217 Ndipo lupanga linatuluka mkamwa Mwake. Iye anali chiyani? Wokwera pa kavalo woyera wa Chivumbulutso. Onani lupangalo. “Kuchokera mkamwa Mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse,” Mawu. Ndipo, potsiriza, ndi Mawu Ake, pamene Iwo akuwonekera kwa ana onse a Mulungu, Iye adzapondereza fuko lirilonse pansu ndi Mawu Ake, ndi lupanga lakuthwa ili. Taonani apa chimene chinachitika, pamene ife tikuzipeza izo:

*Ndipo... dzanja lake lamanja... ndipo kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse: ndipo maonekedwe a nkhope yake anali ngati dzuwa lowala mu mphamvu yake.*

218 “Lupanga lakuthwa-konsekonse.” Kodi chimatuluka pakamwa pa munthu uyu ndi chiyani? Mawu a Mulungu. Ndi lupanga lakuthwa konsekonse. Kodi ilo limachita chiyani? Limazindikira malingaliro a mu mtima, zolinga; limapita ngakhale mwakuya kudusa nyama, mnofu, makhungu a magazi, kukalowa mufupa, mpaka mmafuta a mmafupa, mpaka kupitirira apo, ngakhale kwa wozindikira malingaliro ndi zolinga za mu mtima. Ndi chimene Mawu a Mulungu amachita.

219 “Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo tsopano Mawu akusandulika thupi mu Mpingo Wake, akukhala pakati pathu. Angelo Ake mdzanja Lake, akutumikira. Mulungu akudalira pa Mpingo Wake. Mulungu akudalira pa ife a m’badwo uno kuti tibweretse

Kuwala kwa Uthenga uku kupita kwa dziko lomwe likufa, lachikunja, lamiyambo. Mulungu akuyika chipsyinjochu pa ine ndi inu. Tsoka kwa ife ngati achikunja angafe osadziwa. Oh, iwo anapitirira kumawerenga, kumalemba, ndi masamu, ndi mabukhu pang'ono achipembedzo, ndipo iwo apanga osaposa gulu la otembenezidwa. Ndikutanthauza Uthenga! Uthenga si Mawu okha. Paulo anatero. Paulo anati, "Uthenga sunabwere kwa ife kudzera mu Mawu okha, koma Mawu amenewo akuwonetseredwa." Pamene Mawu, mwa Mzimu Woyera, akhala . . . Mawu akabzalidwa mu mtima umene uli ndi Mzimu Woyera ndipo umabala chimene Mawu amanena kuti Iwo akanadzatero. Ndipo Mawu amatha kuzindikira malingaliro a mu mtima! Ulemelero! Oh, mai! Oh! Wozindikira malingaliro ndi zolinga za mu mtima, Mawu amatero.

220 Amapita kuchokera mkamwa Mwake, lupanga lakuthwa konsekonse, amakawadzutsa achikunja. Chinachake chikuyenera kuchitika limodzi la masiku awa. Inde! Mawu a Mulungu, Dzina Lake linali Mawu a Mulungu, Mawu akuwonetseredwa. Taonani, Yesu anati, "Pitani mu dziko lonse lapansi," Marko 16, Malonje Ake omalizira kwa mpingo Iye asanabwerere kuti adzadziwululire Yekha mu m'badwo wa mpingo. Iye anawutuma Mpingo, "Pitani padziko lonse lapansi ndipo mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse." Chiyani? Mukalalikire Uthenga. Marko 16, "Mukalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse." Chimenecho ndi chiyani? Mwakuyankhula kwina, "kawonetsereni mphamvu ya Mzimu Woyera," zimayenera kutero.

221 Tsopano penyani, "kwa aliyense. . ." Osati kukangophunzitsa Mawu; Iye sananene kuti, "Pitani mukaphunzitse Mawu." Iye anati, "Pitani mukalalikire Uthenga." Osati mukaphunzitse Mawu, mukalalikire Uthenga. "Ndipo zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira Uthenga uwu; mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, iwo adzayankhula ndi malirime atsopano, ngati iwo adzatenga njoka kapena kumwa chinthu chakupha icho sichidzawapweteka iwo; ngati iwo adzaika manja pa odwala, iwo adzachira."

222 "Ndipo iwo anatuluka," linatero Lemba, "kukalalikira kulikonse; Ambuye akugwira ntchito ndi iwo, akutsimikizira Mawu ndi zizindikiro zikuwatsatira." Umenewo ndiwo Uthenga, Uthenga ukuwonetsedwa.

223 Zizindikiro izi zidzawatsatira angati? Mpaka kumathero a dziko lapansi, ku m'badwo uliwonse. Pamenepo panali ochepa awo akutsikira kumeneko, atagwirizira Kuwala kumeneko. Nzosadabwitsa Yesu anati, "Musawope, nkhosa zapang'ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu." Kagulu ka nkhosa kakang'ono; apang'ono nthawizonse, osati ambiri.

224 Chabwino, tsopano chobwereza chowonjezera chimodzi. Ndipo ife tinatenga ya 20, chotero tsopano tiyeni tiwone apa pa ndime iyi apa. Tsopano ya 16:

*Ndipo mu dzanja lake lamanja anali ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri: . . .*

225 Tsopano tiyeni titenge . . . ndipo a . . . mawonekedwe Ake:

*. . . kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse: ndipo maonekedwe ake anali ngati dzuwa lowala mu mphamvu yake.*

226 Ngati mungatsegule ku . . . tiyeni tiwone, Mateyu 17. Tiyeni tingopeza iyo pomwe apa pamene ife tiri pa iyo; chotero ife tikungodutsamo, ndipo ambiri a anthu amene akutenga izo, tiyeni . . . kapena akuzilemba izo, ife tingowalola iwo kuti awerenge iyo kuti tidziwe.

227 Mateyu 17, chabwino:

*. . . patapita masiku asanu ndi limodzi Yesu anamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane . . . pa phiri lalitali pawokha,*

*Ndipo anasandulika pamaso pawo: ndipo nkhope yake inawala ngati dzuwa, ndipo zovala zake zinali zoyera monga kuwala.*

228 Iye anasandulika. Kodi Iye anachita chiyani? Anadzidutsitsa Yekha mu kusandulika, anadzipititsa mu tsiku lakudza Kwake. Tsopano penyani, atangotsala maora pang'ono izi zisanachitike, Yesu anali atangopanga chobwereza ichi kumbuyo kuno pa mutu wotsatira, “Indetu ine ndinena ndi inu, kuti ena ayima pano . . .” Ndi angati akudziwa chimene nditi ndinene? “Ena ayima pano sadzachoka, sadzamwalira, mpaka atadzawona Mwana wa munthu akubwera mu Ulemerero.” Nkulondola uko? Ndipo Iye anamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane, mboni zitatu, chifukwa mu Chipangano Chakale chirichonse, mawu apang'ono aliwonse, ankakhazikitsidwa ndi mboni zitatu, ndipo anawatengera iwo pamwamba pa phiri.

229 Zindikirani chimene chinabwera poyambirira. Oh, ine basi sindingayimire pomwe apa, ine ndikuyenera kuti ndipeze ichi. Taonani! Kodi chinthu choyambirira chimene iwo anachiwona chinali chiyani? Iwo anamutengera Yesu pamwamba pa phiri . . . kapena Iye anawatengera iwo pamwamba, ndipo Iye anasandulika pamaso pawo, anasandulika. Zovala Zake zinawala ngati dzuwa pakati pa mphamvu zake, ndipo pamenepo anawonekera kwa Iye Mose ndi Eliya. Kodi Mwana wa munthu akubwera mu mawonekedwe otani tsopano? Ndipo poyamba, adzawonekera, adzakhala Mose ndi Eliya.

230 Tsopano, zindikirani, Yesu asanabwerere pa dziko lapansi . . . Tsopano, izi mzapatsogolo pang'ono pa nthawi, koma Mzimu wa Eliya udzabwereranso pa dziko lapansi

ndipo udzatembenuza mitima ya ana kubwerera kwa atate awo. Baibulo linanena chomwecho. Yesu anamuwona iye apa, atumwi anamuwona iye apa, dongosolo la kudza kwa Mwana wa munthu ali mu ulemelero. Iye ndi woti apatsidwe ulemelero ndi kudzabwerreranso. Chinthu choyambirira, iwo asanamuwone Iye, chinali chiyani? Eliya. Kenako chiyani? Mose; Israeli akubwerera kumeneko, osunga-malamulo. Ndipo kenako Mwana wa munthu waulemelero. Aleluya! Kodi inu mukuliwona dongosolo la kudza Kwakelo? Mzimu wa Eliya, kapena umboni wa m'badwo wa mpingo wotsiriza. Mwaona, akubwera mu mphamvu kuti adzamuwonetsere Iye.

231 Kenako Ayuda handiredi ndi forte foro sauzande adzasonkhana pa Phiri la Sinai, pamene Israeli wasanduka fuko iyemwini; fuko lakale kwambiri padziko lapansi, mbendera yakale kwambiri padziko lapansi; ali ndi fuko lawo lomwe, mbendera yawo yomwe, ankhondo awo omwe, ndalama yawo yomwe, ndi china chirichonse. Iwo ndi mmodzi mwa mamembala a migwirizano ya mayiko chifukwa iwo ndi fuko. Yesu anati iwo sakuyenera kutayidwa kufikira zinthu zonse zitakwaniritsidwa.

232 Chozizwitsa cha momwe gulu la Ayuda lija, ozunzidwa kulikonse, ndipo okanidwa, ndipo oponderizedwa ndi kuponyedwa kunja, monga Mpingo kupyola kudutsa mibadwo yonse ya kukanidwa, komabe Yesu anati, "Pamene mudzawona mtengo wa mkuyu ukuphuka masamba ake, fuko limenelo likubwerera kuti likhale fuko kachiwiri, nthawi ili pafupi, ngakhalenso pakhomo. Indetu Ine ndinena ndi inu, M'badwo uno sudzadutsa mpaka zinthu zonsezi zitakwaniritsidwa." Kupysinjika uku...Anthu awa sadzatha. Hitler anayesetsa kuti awaphe iwo, Mussolini anayesetsa kuti awaphe iwo, Stalin anayesetsa kuti awaphe iwo, wina aliyenseyo, koma iwo sadzakhala ndi chilema konse, kapena kuchotsedwa pa dziko lapansi, iwo adzakhala anthu ndi fuko akuyimirira kumeneko. Amen!

233 Padzabwera Mose ndi Eliya. Oh! Ndikuyembekeza kuti mukumvetsa zimenezo.

234 Chabwino, "Dzuwa likuwala mu mphamvu yake," Mawonekedwe ake, atasandulika, atasinthika. Tsopano chinthu china, mu Chivumbulutso 21:23, ngati inu mukufuna kuti mulembe zimenezo. Mu Yerusalemu Watsopano, 21:23, Iye ndi Mwanawankhosa amene ali mu Mzinda, kumeneko ndiko Kuwala kwake, kukuwala; pakuti iwo sanasowekere kuwala mu Mzindawo, dzuwa silidzatuluka mmenemo, chifukwa Mwanawankhosa amene ali pakati pa Mzindawo adzakhala Kuwala kwake. Ndipo mafuko amene apulumutsidwa adzayenda mu Kuwala kwa Mwanawankhosa! Amen! Iye ndi Kuwala kwa Mwanawankhosa. Oh, kodi inu simukusangalala ndi zimenezo?

<sup>235</sup> Osati zokhazo basi, komanso Iye, pa kudza (Yohane anamuwona Iye mu tsiku la Ambuye), Dzuwa la chirungamo. Tiyeni tipite ku Malaki. Malaki, mneneri wotsiriza wa Chipangano Chakale. Malaki, mutu wa 4.

<sup>236</sup> Ndiri ndi nkhani yaying'ono yoti ndinene za mkazi wanga wokonedwa wakhala kumbuyo uko. Ine ndinamupatsa iye nthawi yovuta tisanakwatirane, ndayesetsa kuti ndizikonze zimenezo titakwatirana. Ndipo ine sindimadziwa ngati ndinkafuna kukwatiranso kapena ayi, ndipo chotero iye anangokhumudwa. Ndipo ine ndinkaganiza kuti iye anali mtsikana wabwino kwambiri kuti ndingomusiya azipita, kumulola mwamuna wina wabwino amukwatire iye amene angamusamalire iye. Ndipo ndinkaganiza kuti sindinali woyenera nkomwe zimenezo; ndipo ine sindiri, woyenera ubwino wake, mulimonse. Chotero iye anali wokhumudwa ndipo sankadziwa choti achite. Izi zakhala zaka zapitazo, pafupifupi zaka twente zapitazo. Iye anakhumudwa kwambiri, anayamba kulira usana ndi usiku. Ndipo ine ndinali kuyesesa kuti ndimusiye iye, osati chifukwa choti sindimamukonda iye, chifukwa ine sindimafuna kuti nditenge nthawi yake; chifukwa, ndimafuna ndimusiye apeze winawake, munthu wina wabwino, chifukwa iye ndi mtsikana wabwino kwambiri kuti angopita monga choncho, ndipo ine nditenge... kumangopita ndi iye ndi zinthu monga chomwecho. Ndipo ine—ine ndinkaganiza kuti ankandikonda ine, ndipo ine ndinkadziwa kuti ndinkamukonda iye. Chotero ndiye ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndingoyesera ku... Ndipeza chibwenzi ndi mtsikana wina ndi kumakayenda naye, ndi kumupangitsa iye kuti amverere moyipa za ine.” Ine ndinakhala ngati ndikanamupha iye, ndinadana nazo izo moyipa pambuyo pake; iye anangoswekeratu. Ine ndinamuza iye, ndinati, “Ndiwe mtsikana wabwino kwambiri, ine—ine sindikufuna kutenga nthawi yako monga choncho.”

<sup>237</sup> Ndipo iye anati, “Koma ine—ine ndimakukonda *iwe*, Bill, ndipo ndiwe yekhayo amene ndingamukonde.” Anati, “Ine—ine nthawizonse ndakhala ndikukukonda iwe.”

Ine ndinati, “Ine—ine ndikuyamikira zimenezo. Koma,” ine ndinati, “iwe ukudziwa,” Ine ndinati, “Ndine wapandekha.” Ine ndinati, “Ine ndi—ine ndizingokhala ngati wokhala ndekha. Waona, ine—ine sindidzakwatira konse.”

<sup>238</sup> Ndipo iye anali atakhazikika kwambiri pa zimenezo, inu mukudziwa, kanthu kakang'ono kosauka. Ndipo iye anapita kunja pa—pa mthunzi. Ndipo iye anapita kunja uko, ndipo iye anakagwada pansu pa mawondo ake, ndipo iye anati, “Ambuye, ine sindikudziwa choti ndichite. Ine—ine sindikufuna kuti ndisakumvereni Inu, ndipo komabe ine ndimamukonda Bill, ndipo ine sindikudziwa choti ndichite. Ambuye, Inu mungandipatse ine chithonthonzo pang'ono chabe? Kodi Inu



mungandithandize ine pang’ono pokha? Ine sindinayambe ndakupemphanipo Inu ichi mmoyo wanga, Ambuye, ndipo ine ndikuyembekeza kuti sindidzakupemphaninso Inu,” iye anati, “koma ngati Inu mutangondithandiza ine, ndipo mundirole ine nditsegule Baibulo ili, ndipo Inu mundipatse ine Lemba. Ine ndamvapo anthu akunena kuti Inu munachita zimenezo.” Ndipo pamene iye anatsegula ilo, linali Malaki 4:

*Taonani, Ine ndikupereka kwa...kapena ndidzakutumizirani kwa inu Eliya mneneri lisanadze ilo—tsiku lowopsya la AMBUYE:*

<sup>239</sup> Iye anati, “Ndinadzuka kuchoka pamenepo wokhutitsidwa kuti tikukwatirana monga china chirichonse.” Mukuona?

*Pakuti, taonani, tsiku likudza, limene lidzawotcha ngati ng’ano; ndipo onse odzikuza, eya, . . . onse iwo ochita zoyipa, adzakhala mapesi: ndipo tsikulo likudza limene lidzawatentha iwo, atero YEHOVA wa makamu, ndipo silidzawasiyira iwo muzu kapena nthambi.*

*Koma kwa inu amene mukuopa dzina langa . . . Dzuwa (D-z-u-w-a) Dzuwa la chirungamo lidzatulukira ndi machiritso mmapiko mwake; . . .*

<sup>240</sup> “Dzuwa likuwala mu mphamvu yake.” Oh! Mphamvu ya Mwana wa Mulungu likuwala pakati pathu usikuuno. Atayima pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide mu mawonekedwe Ake asanu ndi awiri apa ngati woweruza. Monga Mmodzi amene anazunzika ndipo anatifera ife, ndipo anatenga chiweruzo Chaumulungu pa Iyemwini, ndipo anaponda moponderamo mphesa, mkwiyo wa Mulungu. Kwa wochimwa Iye ndi mathithi owopsya, kwa iwe solo yomasuka pa nyanja ya moyo. Ndipo kwa Mpingo, Mpulumutsi wokoma, wokhazikika mu mpumulo, ndi kumamva mtsinje wotumphuka pamene mukugona ndi kupumula wokhutitsidwa mwangwiro mwa Khristu. Ndi nthawi bwanji! Akuwala pa ife ndi kuwala Kwake kotentha, “Musawope, ine ndine Iye amene anali, amene ndiripo, ndipo ndiri nkudza. Ndine Wamphamvuzonse, pambali pa Ine palibe aliyense. Ine ndine zonse ziwiri Alfa ndi Omega, ndipo Ine ndidzapereka kwa iye amene akumva ludzu za akasupe a madzi a Moyo kwaulere.” Oh, ndi lonjezo lotani ndipo iyo ndi nkhani yachikondi yotani! Ndipo Mwanawankhosa pakati pa Mzinda umene sukusowa kuwala, ndipo Iye ndi Dzuwa la chilungamo lokhala ndi machiritso mmapiko Ake.

Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi  
Yowala ya Mmawa,  
Iye ndiye wokongola kwambiri wa teni  
sauzande kumoyo wanga.

Mu chisoni Iye ndi chithonhozo changa, mu  
 mavuto Iye ndi pokhalapo panga,  
 Amandiua ine nkhawa iliyonse pa Iye  
 ndiyitule. Aleluya!  
 Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya  
 Mmawa Yowala,  
 Iye ndi wokongola kwambiri mwa teni  
 sauzande pa moyo wanga.

<sup>241</sup> Inde, bwana! Oh, Nyenyezi ya M'mawa Yaikulu pamene  
 ikutulukira kuti idzawale, ikulemekeza tsiku limene likubwera,  
 ikukankha ilo, kuti "Tsiku likukonzekera kuyambika, Mwana  
 akuyandikira," ndipo Iye amadzikokera Yekha kunja kuseri kwa  
 nyenyezi zina zonse (Oh, mai.) ndi machiritso mu mapiko Ake.

<sup>242</sup> Tsopano kubwerera ku uthenga wathu. Ndipo tikutseka  
 tsopano, kuti tizikakonzekera mawa usiku, chifukwa nthawi ndi  
 kota kuti ikwane naini, ife sitikufuna kuti timusunge aliyense  
 motalika kwambiri, kuti tithe kudzakhala pano.

<sup>243</sup> Chabwino, Dzuwa la chirungamo lokhala ndi machiritso  
 mmapike Ake. Tsopano mawonekedwe Ake. Iye anali woweruza,  
 kapena chinthu china chosonyeza kuti iye anali mu tsiku la  
 Ambuye. Inu mukukhulupirira zimenezo? Iye anapita mu tsiku  
 la Ambuye ndipo anawawona Ambuye ngati woweruza; osati  
 ngati wansembe, osati ngati mfumu, koma ngati woweruza. Iye  
 ndi Woweruza. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Baibulo  
 limati Iye ndi Woweruza. Ndipo apa Iye anali atavala ngati  
 Woweruza, kuwonetsera chimene Iye anali atachita; chimene Iye  
 anali: chimene Iye anali kwa wochimwa, chimene Iye anali kwa  
 Mkhristu. Ndipo apa Iye wayima tsopano ndi Liwu la madzi  
 ambiri, ndipo mawonekedwe Ake anali ngati dzuwa lowala mu  
 mphamvu yake.

<sup>244</sup> Tsopano zotsatira, ndime ya 16. "Ndipo..." Ayi, ine  
 ndikupepesa, ndi ndime ya 17:

*Ndipo pamene ine ndinamuwona iye, ndinagwa  
 pamapazi ake ngati wakufa.*

<sup>245</sup> Mai! Mneneri sakanatha kuyimanso, atawona masomphenya  
 oterowo. Iye basi—Iye anangowaza mphamvu yake, ndipo  
 anagwa pansu pamapazi Ake ngati wakufa. Tsopano penyani:

*Ndipo anayika dzanja lake lamanja pa ine, akunena  
 kwa ine, Usawope ayi; Ine ndine woyamba ndi  
 wotsiriza:*

<sup>246</sup> Oh, mai! Osati mneneri, Mulungu! "Ine ndi woyamba  
 ndi wotsiriza. Ndine woyamba wa Vumbulutso, wotsiriza wa  
 Vumbulutso. Ndine Iye amene anali, Ine ndine Iye amene  
 ndiripo, Ine ndine Iye amene ndiri nkudza." Tiyeni tiwone:

*Ine ndine . . . Ine . . .*

*Ndipo iye anayika dzanja lake lamanja pa ine, akunena kwa ine, Usawope ayi; Ine ndine woyamba ndi wotsiriza:*

*Ine ndine iye amene ali wamoyo, ndipo ndinali wakufa; ndipo, taonani, ndiri wamoyo ku nthawizonse, (Pakali pano. Ndipo kenako iye anafuula mokweza:) Amen; ndipo ndiri nawo makiyi a gehena ndi. . . imfa.*

<sup>247</sup> Tsopano, musachite mantha. Ife tingawope chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani kuti Mpingo uzilephera kusunga Ake. . . kuganiza za Mawu Ake? Tiyeni tiimire apa kwa miniti yokha, chifukwa ife tikutseka. Mpingo uno nchifukwa chiyani kuti uzichita mantha? Nchiyani chimene Iye analonjizapo chimene Iye sanachiwonetsere pamaso pathu? Nchifukwa chiyani kuti muziwopa chilango kapena chapatsogolo? “Musawope ayi! Ine ndine Iye amene anali, Iye amene ali, ndi amene alinkudza. Ine ndine woyamba ndi wotsiriza. Ine ndiri nawo mafungulo a gehena ndi imfa pomwe pano.” Chifukwa chiyani? “Ndapambana ndipo ndagonjetsa gehena ndi imfa (Ndizo ziwiri zonse manda ndi hade; imfa payokha, hade payokha.) kwa inu. Ine ndagonjetsa zonsezo. Ine ndagonjetsa gehena, imfa, manda.” Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali yekhayo wamk- . . .

<sup>248</sup> Amuna ambiri anapita kunja kuti akagonjetse. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Napoleon anapita kuti akaligonjetse dziko lapansi, ndipo iye anatero pa usinkhu wa zaka sarte-firii. Pa usinkhu wa zaka seventini ndi twente-faivi, Napoleon anali woletsa, sankakhulupirira mu kumwa kapena chirichonse. Iye anapita ku France. Iye sanali wachi Faransa, iye ankachokera pa chilumba, iye anapita kumeneko kuti akamubwezere France chifukwa sankamukonda iye, sankakonda France. Koma iye anagonjetsedwa. Ndipo iye anapita chitsogolo ndipo anakagonjetsa France, ndipo anawatenga Achifaransa amenewo ndipo analigonjetsa dzikolo. Ndipo pa usinkhu wa zaka sarte-firii iye anakhala pansu ndipo analira chifukwa panalibe wina aliyense woti amugonjetse, ndipo anamwalira ali chidakhwa. Atagonjetsedwa, sanathe ngakhale kuti adzigonjetse yekha. Mukuona? Ndipo kenako anakumana ndi kugonjetsedwa kwake ku Waterloo, anakumana ndi mathero ake ku Waterloo. Ine ndinapitako kunja uko ndipo ndawonako zikwangwani zakale za zotsalira ndi zinthu kunja uko, pamene ife tinali mdzikolo. Tsopano, ife timutenge mgonjetsi ameneyo, iye anayamba ngati mnyamata ndipo iye anatenga mbali yolakwika kuti akagonjetse, ndipo iye anafa, mwamanyazi.

<sup>249</sup> Koma kunali Mnyamata wina amene anabwera mdziko nthawi ina. Iye anafa ali ndi zaka sarte-firii ndipo Iye anagonjetsa chirichonse chimene chikanagonjetsedwa. Pamene Iye anali pa dziko lapansi Iye anagonjetsa zilakolako, kunyada, Iye anagonjetsa matenda, Iye anagonjetsa ziwanda. Pamene

Iye anafa, Iye anagonjetsa imfa. Pamene Iye anadzauka, Iye anagonjetsa gehena. Iye anakwera mmwamba ndipo anakagonjetsa chirichonse chimene chinali chotsutsana ndi anthu, izo zinapita moponderamo mphesa za Mulungu ndipo anaziphwanya izo ndipo anagonjetsa imfa, gehena, manda, matenda, miyambo, china chirichonse, ndipo anagonjetsa izo zonse, ndipo anadzauka pa tsiku lachitatu ndipo anagonjetsa malo onse ammwamba, ndipo anadzadula nkhungu imeneyo pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo analumikiza Kumwamba ndi dziko lapansi palimodzi. Ulemelero! Oh, mai! Psyii!

<sup>250</sup> Apo Iye wayima Mgonjetsi Wamphamvu Iye atang'amba chopimba pawiri, ndi Uyo pamenepo. Ali ndi mafungulo a ziwiri zonse imfa ndi gehena zitapachikidwa pambali Panga, "Musawope." Anayika dzanja Lake lamanja (mphamvu Yake) pa iye, ndipo anamuukitsa iye ndi mphamvu ya dzanja Lake lamanja, anati, "Musawope, Ine ndine Iye amene ndinali, ndi Iye amene alipo, ndipo adzabwera. Ine ndi woyamba ndi wotsiriza. Ine ndi Iye amene ndinakhala moyo, ndipo ndinafa, ndipo ndiri moyo kenanso kwanthawizonse. Amenii!" Oh!

Uyo! Muwoneni mgonjetsi wamphamvu,  
Uyo! Muoneni Iye powonekera bwino,  
Apo Iye wayima, mgonjetsi wamphamvu,  
Popeza Iye anang'amba chopimba pawiri.

<sup>251</sup> Amenii! Anadula chopinga chirichonse kwa anthu, kuti akhoze kulumikizana monga mmunda wa Edeni. Tsopano, munthu. . . Ine ndimafuna kuzitsamwitsa izo, koma ine ndinena izo. Munthu ndi wamphamvuzonse. Inu simukhulupirira zimenezo, koma iye ali. Munthu wodzipereka kwathunthu kwa Mulungu ndi wamphamvuzonse. Kodi Iye sananene, mu Marko 11:22, "Zinthu zirizonse zomwe munganene, ndipo nkusakaikira mu mtima mwanu, izo zidzachitika. Mutha kukhala ndi chimene mwanena"?

<sup>252</sup> Kodi chimachitika ndi chiyani pamene a mphamvuzonse awiri akumana? Pamene Mulungu ndi munthu abwera pamodzi, a mphamvuzonse awiri, chinachake chimayenera kugwedezeka. Ena- . . . Chirichonse chimene munganene ndi mphamvu yolenga imeneyo ya mphamvuzonse ya Mulungu, podziwa kuti Iye analonjeza izo, ndipo Iye ananena izo mu Mawu Ake, izo zimalenga mphamvu imene imapita kutali ndi kukapangitsa zinthu kuti zichitike, zinthu zimene palibepo, zimapangitsa, izo ngati kuti ziripo, chifukwa a mphamvuzonse awiri akumana. Pamenepo Iye waima! Oh, kodi Iye si wodabwitsa!

<sup>253</sup> Tiyeni tiwone ngati tiri ndi zinthu zina zabwino zowonjezera. Ndime ya 18, tsopano ndime ya 19. Yohane; chinachitika ndi chiyani pamene iye anawona nkhope Yake? Chotsatira chake? Iye anagwa pamapazi Ake; iye sakanakhoza kuyimanso, moyo wake wa umunthu unachokamo, iye

sakanakhoza kuchita izo. Iye anali Mgonjetsi, Iye anali atagonjetsa kale.

254 Tsopano Iye akupereka kulamula, ndipo kenako ife tikuyamba kumaliza mutuwo, ndipo ya 19 iyi:

*Lemba zinthu zimene iwe wazona, ndi zinthu zimene ziripo, ndi zinthu zimene zidzakhale mtsogolo;*

255 Ife tinatenga ndime ya 20:

*Chinsinsi cha nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene iwe unaziwona ku dzanja lamanja, . . . ndizo zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndizo angelo asanu ndi awiri a mipingo isanu ndi iwiri: ndipo zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zimene iwe unaziwona ndi mipingo isanu ndi iwiri.*

256 Oh! Ndi zochititsa kakasi, mzanga. Kumuwona Iye akuyima pamenepo ali wapamwamba. . . upamwamba wa Umulungu Wake. Iye ndiye Woweruza, Wansembe, Mfumu, Mphungu, Mwanawankhosa, Mkango, Alfa, Omega, Atate, Mwana, Mzimu Woyera; Iye amene anali, amene alipo, ndipo ali nkudza. Kuponda mopondera mphesa mwaukali wa Mulungu, ndipo zinakondweretsa chirichonse, kufikira kuti Mulungu (Ananena pa mtanda,), pamene Iye anauka (Iye anati, “Izo zatha.”), zinamukondweretsa Mulungu *kwambiri*, mpaka Mzimu umene unamusiya Iye unadzabwerera mmawa wa Isitara ndipo unadzamutenga Iye ndipo unadzamuukitsanso Iye kwa kulungamitsidwa kwathu.

257 Pamenepo Yohane anayang’ana mmwamba ndipo anamuwona Iye atayima pamenepo ali ndi mapazi a mkuwa, maso ngati malawi a moto akuyenda uku ndi uku pa dziko lonse lapansi. Daniele anamuwona Iye zaka seveni handiredere izo zisanachitike, pa malo omwewo, mtundu womwewo, munthu yemweyo ataima pamenepo, wamasiku Amakedzana, ndi mmodzi wonga Mwana wa munthu amene analumikizana ndi Iye, ndipo chiweruzo chonse chinaperekedwa kwa Iye, atayima pa Chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera.

258 Powona zinthu izi, ife tikuyenera kukhala anthu a mtundu wanji, abwenzi? Mulungu akudalitseni inu ndiro pemphero langa. Mukuona? Kodi inu mukumukonda Iye? Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Kodi mwazika moyo wanu mwa Iye?

259 Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

260 Basi mwakachetechete ndi mofewa, pamene ife tiziimba mwakachetechete, *Ndazika Moyo Wanga Mu Mpumulo Wa Mmwamba*, “Sindidzamvanso mathithi amafunde amenewo akupititsa moyo wanga kutali, koma Iwo adzayankhula mtendere wokoma kumoyo wanga.” Mwakachetechete tsopano, momekeza, aliyense.

Ndazika moyo mu mpumulo wa mmwamba,  
Sindidzayendanso mu nyanja yowopsya;  
Mphepo ingawopsye pamwamba pa, nkuntho  
wowopsya wakuya,  
Mwa Yesu ndine wotetezeka.

Ndazika moyo mu mpumulo wammwamba,  
Sindidzayendanso mu nyanja yowopsya;  
Mphepo ingawopsye pamwamba pa, nkuntho  
wowopsya wakuya,  
Mwa Yesu ndatetezeka.

Kuwalire pa ine, (Mulole kuwala kwa  
Ulemelero, Ambuye,) Ambuye, kuwalire pa  
ine,  
Mulole Kuwala kochokera ku nyumba ya nyali  
kuwalire pa ine;  
Oh, walirani pa ine, Ambuye, walirani pa ine,  
(Tiyeni tikwezere manja athu kwa Iye.)  
Mulole Kuwala kochokera ku nyumba yanyali  
kuwalire pa ine.

Kukhala monga Yesu, (Inde, Ambuye.)  
Kukhala monga Yesu,  
Pa dziko lapansi ndilakalaka kukhala monga  
Iye;  
Kupyola ulendo wa moyo kuchokera padziko  
lapansi kupita ku Ulemerero,  
Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'udza kolasi—  
Mkonzi].

. . . O Mpulumutsi wodabwitsa,  
Pa dziko lapansi ndilakalaka kukhala monga  
Iye;  
Kupyola ulendo wa moyo kuchokera padziko  
lapansi kupita ku Ulemelero,

<sup>261</sup> Kodi inu mungafune kuti Moyo Wake uzikhala mwa inu,  
nkumanyezimiritsa Kukhalapo Kwake? Ngati mungatero, ndipo  
simunalandirebe iwo, kodi mungayimirire kwa pemphero? iwo  
amene angafune kuti akumbukiridwe mu pemphero. Mulungu  
akudalitseni inu.

Kuchokera mkhola la ku Betelehemu. . .  
(Ingokhalani chiimire tsopano, ingokhalani  
chomwecho. . .) . . . kunabwera Mlendo, (Inu  
mudzakhala mlendo ku dziko lapansi.)  
Pa dziko lapansi ndilakalaka kukhala monga  
Iye;  
Kupyola ulendo wa moyo, kuchokera padziko  
lapansi kupita ku Ulemelero,  
Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.

Kungokhala monga Yesu, kukhala monga  
 Ye- . . . (Ndicho chokhumba changa.)  
 Pa dziko lapansi ine ndikulakalaka kukhala  
 monga Iye;  
 Kupyola ulendo wa moyo, kuchokera padziko  
 lapansi kupita ku Ulemelero,  
 Ine ndikungopempha kuti ndikhale monga Iye.

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'udza  
 kolasi—Mkonzi.]

. . . motsika, modzichepetsa ndi motsika.

<sup>262</sup> Tsopano, Atate Akumwamba, ayima pa mapazi awo ndi ambiri omwe akufuna kuti akulandireni Inu. Iwo atopa ndi kumangosuntha suntha, osadziwa kumene iwo akupita, kunja uko ku funde la moyo; ndipo akudziwa mwinamwake kusanache mtima usiya kugunda, ndiye mathithi aakulu, matsitso, patsogolo pawo, moyo wolowerera. Iwo akhala monga iwoeni, iwo akhala monga dziko lapansi, koma iwo akufuna kukhala monga Inu tsopano, Ambuye. Alandireni iwo mu Ufumu Wanu, iwo ndi Anu, Atate, chifukwa Inu mukudziwa mitima yawo ndi zolinga za mitima yawo. Ndipo Inu munazilemba izo, ndipo munanena izo ndi milomo Yanu, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.” Inu munanenanso, Ambuye, “Wodala ndi iye amene awerenga ndi iye amene amva chinenero cha uneneri wa Bukhu ili, pakuti nthawi yayandikira.” Iwo akuzindikira kuti nthawi yayandikira. Iwo sangasoherenso kenanso, Ambuye. Ponyani chingwe cha moyo, akokereni iwo kwa Inumwini, Ambuye. Mulole iwo apite kuchokera usiku uno, akunyezimiritsa Kuwala kwa Yesu Khristu. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, Atate Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu. Mulole iwo modzichepetsa atsatire Ambuye mu ubatizo apa pa tchalitchi; avale Mzimu Woyera mmoyo mwawo kuti athe kukhala monga Yesu masiku awo onse. Ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

Kungokhala monga Yesu, kukhala monga . . .

<sup>263</sup> Ena a inu nonse mwayima pafupi kapena mwakhala pafupi ndi anthu amenewo, amene muli Akhristu, afikireni ndipo agwireni dzanja lawo ndi kuwagwira chanza. Muike dzanja lanu pa iwo, “Mutamandeni Mulungu chifukwa cha moyo wanu.” Maguwa athu onse ndi odzaza apa ndi ana ndi zinthu, sitingathe kuwabweretsa iwo kuno.

Kupyola ulendo wa moyo, kuchokera padziko  
 lapansi kupita ku Ulemelero,  
 Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

Walirani pa ine, Oh, walirani pa ine,  
 Mulole Kuwala kochokera ku nyumba  
 yowunikira, kuwalikire pa ine;  
 Oh, walirani pa ine, Ambuye, walirani pa ine,  
 Lolani Kuwala kochokera ku nyumba  
 yowunikira, kuwalikire ine.

<sup>264</sup> Mukumverera bwino kwenikweni? Simukumverera bwino? Kodi sindinu wokondwa kuti ndinu Mkhristu? Gwiranani chanza ndi munthu wina amene wakhala pafupi nanu tsopano, pamene tiziyimba nyimboyi, *Tidzayenda Mu Kuwala*, Kuwala kokongola uku, Kuwala kwa Ambuye Yesu Khristu kukuwonetseredwa mu thupi.

Tidzayenda mu Kuwala, Kuwala kokongola,  
 Bwerani kumene mame achifundo ali owala;  
 Walirani pozungirira ife, usana ndi usiku,  
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Imbani iyo, aliyense:

Tiyende mu Kuwala, ndi Kuwala kokongola,  
 Bwerani kumene mame, achifundo akuwala;  
 Walirani pozungulira ife, usana ndi usiku,  
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Bwerani, oyera nonse a Kuwala mudzalengeze,  
 Yesu, Kuwala kwa dziko;  
 Kenako mabelu Akumwamba adzalira,  
 O Yesu, Kuwala kwa dziko.

Kwezerani mmwamba dzanja lanu tsopano:

Tiyenda mu Kuwala uku, Kuwala kokongola,  
 Bwerani kumene madontho a chifundo  
 akuwala;  
 Walirani pozungulira ife, usana ndi usiku,  
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

Tizipitirira kuyenda mu Kuwala uku, Ndi  
 Kuwala kokongola,  
 Kumabwera kumene mame achifundo  
 akuwala;  
 Ingowalirani potizungulira pathu, usana ndi  
 usiku,  
 Yesu, Iye ndi Kuwala kwa dziko.

Tiyende mu Kuwala (Kuwala kwa Uthenga),  
 Kuwala kokongola,  
 Kumabwera kumene mame achifundo  
 akuwala;  
 Walirani potizungulira pathu, usana ndi usiku,  
 Yesu, Kuwala kwa dziko.

<sup>265</sup> Kubwerera pachiyambi, pa Pentekoste pamene Mzimu Woyera unadzagwa pa Mpingo. Uthenga unabwera mpaka ku



Smurna; pamenepo panaima Ireniyasi, woyera wamkulu wa Mulungu, akuyankhula m'malirime, mphamvu ya Mulungu, akuukitsa akufa, kuchiritsa odwala, Iye anali kuyenda mu Kuwala. Pambuyo pake kunadzabwera Columba, woyera wamphamvu wamkulu wa Mulungu. Ochuluka a oyera ena aakulu atanyamula Uthenga mpaka mmusi, akuyenda mu Kuwala, Kuwala kwa Uthenga, Kuwala komweko kumene kunadzawala pa Tsiku la Pentekoste; Khristu ataimirira pakati pa anthu Ake, ndi zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide zija zikuwonetsera kunyezimira Kwake monga dzuwa pakati pa kutentha kwake.

<sup>266</sup> Ndi ife pano mu 1961:

Tiyende mu Kuwala, Ndi Kuwala kokongola  
chomwecho,  
Kumabwera kumene mame achifundo  
akuwala;  
Oh, walirani pozungulira pathu, usana ndi  
usiku,  
O Yesu, Kuwala kwa mdziko.

Tiyeni tiime:

Tizipitirira kuyenda mu Kuwala, Ndi Kuwala  
kokongola chomwecho,  
Kumabwera kumene mame a chifundo  
akuwala;  
Walirani pozungulira pathu, usana ndi usiku,  
Yesu, Kuwala kwa mdziko.

Kodi inu mukumukonda Iye?

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye,  
Chifukwa (basi chifukwa) Iye anayamba  
kundikonda ine,  
Ndipo anandigulira chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>267</sup> Osatembenukiranso ku zinthu za mdziko. Ndine wakufa kwa dziko ndipo dziko ndi lakufa kwa ine. Ine ndimangoyenda mwa Khristu, motsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Ine ndimkonda Iye chifukwa Iye amandikonda ine, ndipo amawalitsa madalitso Ake pa ine, kundipatsa ine dzanja lamanja la chiyanjano mu Ufumu Wake. Tsopano ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndipo sichinawonekebe chimene ife titi tidzakhale pamapeto; koma ife tikudziwa kuti tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake lomwe laulemelero, pakuti ife tidzamuwona Iye momwe Iye aliri.

Ndiye tidzakhala tikuyenda mu Kuwala,  
Kuwala kokongola,  
Kobwera kumene mame achifundo akuwalira;  
Walirani potizungulira pathu, usana ndi usiku,  
Yesu, Kuwala kwa mdziko.

<sup>268</sup> Kodi mukumukonda Iye? Inu mukudziwa, pamene uthengawu ukucheka ndi chirichonse, ine ndimakonda kuwamva anthu akulowa mu nyimbo ndi kuyamba kupembedza ndi kumayimba mu Mzimu. Palibenso china chokongola kuposa kuyimba kwabwino kwachikale. Uko nkulondola. Ndimakonda kuyimba kwachikale kwa chipentekoste; osati maliwu ophunzitsidwa moonjeza amene amangogwira mpaka iwo kumaimba manzenene ndipo nkhope yawo nkukhala ya buluu, ndipo osadziwa chimene iwo akuyimba. Ndimakonda winawake yemwe mwinamwake sangathe kuyimba mu dengu komabe ali ndi Mdalitso wa Chipentekoste, tsopano iye akuyimba za izo. Oh, bwanji—ndi nyimbo zaulemerero bwanji zimenezo za pantanda! Oh, mai!

Nyimbo yathu yobalalitsira tsopano:

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wachisoni ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Litenge ilo kulikonse upita.

Mawa usiku seveni koloko, seveni koloko ndendende, misonkhano idzakhala ikuyambika.

Pa Dzina la Yesu kugwada,  
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka  
Iye korona,  
Pamene ulendo wathu udzatha.

Tiyeni tonse tiyimbe tsopano:

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wachisoni ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Oh, litenge kulikonse upita.

Dzina lofunika, Oh ndi lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba;  
Dzina lofunika, Oh ndi lokoma bwanji! (Ndi  
lokoma bwanji!)  
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba.

<sup>269</sup> Tsopano, tatsiriza izo usikuuno. A...anangondifunsa ine tsopano, “Ngati kudzakhale msonkhano mmawa?” Ayi, osati mawa, mukakhale ndi kupumula kwabwino mawa. Mwinamwake mawa usiku, ine sindidzatha kuti ndidzapitirize uthengawo, chotero ndidzautenga iwo tsiku lotsatira. Nthawi iliyonse ndikalephera pa...uthenga wathunthu uwu, ndimawutengera iwo ku tsiku lotsatira. Koma ife tinazikonza kale izi, ndikukhulupirira kuti muli kale mu Mibadwo ya Mpingo. Sichoncho inu? Chabwino.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu pamene tikuimba  
mwakachetechete tsopano:

Pa Dzina la Yesu kugwada, (Lirime lirilonse  
lidzavomereza izo.)

Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka  
Iye korona,

Pamene ulendo wathu udzatha

Dzina lofunika, Oh lokoma bwanji!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba;

Dzina lofunika, Oh ndi lokoma bwanji! (Ndi  
lokoma bwanji!)

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe  
cha Kumwamba.



*MASOMPHENYA APA PATMO* CHA60-1204E  
(The Patmos Vision)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu madzulo, Disembala 4, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)